

CHISINDIKIZO CHACHISANU

NDI CHIMODZI



Tiyeni tiweramitse mitu yathu kamphindi chabe tsopano.

² Ambuye, ife tiri kachiwiri kusonkhananso chifukwa cha utumiki. Ndipo ife tikuganiza za nthawi, mu masiku oyambirira, pamene iwo onse ankabwera ku Shiloh chifukwa cha madalitso a Ambuye. Ndipo tsopano, usiku uno, ife tasonkhana pano kuti timve Mawu Anu. Ndipo monga ife takhala tikuwerenga mu gawo lina ili la Lemba, kuti Mwanawankhosa anali Mmodzi yekha amene akanakhoza kutsegula Zisindikizo, kapena kuzimasula Izo. Ndipo ife tikupemphera kuti usiku uno, pamene ife tiri nacho pansi pa kulingalira Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi chopambana ichi, ife tikupemphera, Atate Akumwamba, kuti Mwanawankhosa adzatsegule Icho kwa ife usiku uno. Pakuti, ife tiri pano kudzamvetisa Icho. Ndipo pamene panalibe munthu pa dziko lapansi, kapena Mmwamba, anali wokwanira, Mwanawankhosa yekha anapezeka wokwanira. Kotero Mmodzi wokwanira-zonse atabwera ndi kutsegula Chisindikizo kwa ife usiku uno, kuti ife tikangokhoza kuyang'ana kupyola katani la nthawi. Icho chikanadzatithandiza ife, ife tikukhulupirira, Atate; tsiku lalikulu ili, lamdima, lodzaza tchimo limene ife tikukhalamo; chikanadzatithandiza ife ndi kutipatsa ife kulimbika. Ife tikudalira tsopano kuti ife tipeza chisomo pamaso Panu. Ife tikudzipereka tokha, limodzi nawo Mawu, kwa Inu, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

Inu mukhoza kukhala pansi.

³ Usiku wabwino, abwenzi. Ndi mwayi kukhalanso pano usiku uno, kukhala mu msonkhano wa Ambuye. Ine ndinachedwerako pang'ono. Ine ndinangopita ku... mwadzidzidzi, kwa munthu akumwalira, membala wa mpingo uno; amayi ake ali, kapena amabwera kuno. Ndipo iwo anati mnyamatayo akumwalira nthawi imeneyo. Kotero ine—ine ndinapita kumusi kukangowona m—mthunzi wa munthu atagona pa kama, akumwalira, mwamuna pafupi msinkhu wanga. Ndipo mu mphindi chabe ya nthawi, ine ndinamuwona munthuyo akuyimirira pa mapazi ake, akupereka mayamiko kwa Ambuye. Ndipo kotero, Mulungu, ngati ife tidzakhale ololera kuvomereza machimo athu ndi kuchita chimene chiri cholondola, kupempha chifundo, kuyitanira pa Iye, Mulungu ali wololera ndi kuyembekezera kupereka izo kwa ife.

⁴ Ndipo, tsopano, ine ndikudziwa mukutentha muno usiku uno. Ndipo—ndipo ziri...Ayi, ine ndikuganiza kutenthako kwatsekedwera kunjja palimodzi. Ndipo—ndipo tiri. . .

⁵ Ine ndinazindikira usiku watha, kapena lero, ili liri tsiku langa lachisanu ndi chiwiri mu chipinda wopanda kuwala, nyali za magesi basi, mwawona; kuwerenga, ndi kupemphera kwa Mulungu kuti atsegule Zisindikizo izi.

⁶ Ndipo apo panali ambiri amene alemba, mu gulu ilo la ofunsa la-...kapena mafunso usiku watha, anali, ambiri kapena pang'ono, osati ochuluka monga mafunso. Iwo anali kufuna kukhala nawo msonkhano wa machiritso, zingatani; amafuna kukhala tsiku lowonjezera, kuti tikhale. . .kuti tikhale nawo msonkhano wamachiritso Lolemba. Kotero ine—ine ndikanati, ndikanakhoza, ine makamaka ndikanakhoza kuchita icho ngati icho chinali—chifuniro cha anthu kuti iwo akanachita izo. Inu mukhoza kuganizira bwino icho ndi kundidziwitsa ine, koma ngati inu mukungofuna kukhala ndi kupempherera odwala.

⁷ Chifukwa, ine ndakonzera nthawi yonse iyi, kwathunthu, kwa Zisindikizo izi, ndi kungodzipatulira ndekha kwa Zisindikizo.

⁸ Kotero inu mukhoza kuganizirapo icho, ndipo kupempherera icho, ndiyeno mundidziwitse ine. Ndipo ndidzatero, ngati Ambuye alola, ine ndikhoza. Pangano langa lotsatira liri ku Albuquerque, New Mexico, ndipo ilo lidzakhala—masiku pang'onobe. Ndipo ine ndiyenera kupita kwathu ku ntchito yina, pa kukonza msonkhano wawukulu wina mu Arizona. Ndipo kotero, ndiye, ngati icho chidzakhala chifuniro cha Ambuye! Inu mupempherere icho, ndipo ine ndichita mofanana, ndiye ife tidzadziwa za icho mtsogolo pang'ono.

⁹ Ndipo ine ndikungofufuza. Tsopano ine ndikuwona. . .Iwe ukayamba kulankhula za matenda, pamenepo iwo amabwera, mwawona. Ine ndikuwona dona uyu akukhala pompa apa. Ngati chinachake sichimuthandiza iye, iye sakhala apa koma pang'ono chabe. Kotero, ndiye, mwawona, ife—ife tingopemphera kuti Mulungu alope. Ndicho chimene inu mwabwerera pano, kubwera kuchokera kutali. Kotero, mwawona, m—Mzimu Woyera umangodziwa chirichonse, inu mukuwona. Kotero Iye. . .

¹⁰ Koma, mwawona, ine ndayesera kuyikonzera nthawi iyi kwa Zisindikizo izi, chifukwa ife tinayikira iyo kwa izo, inu mukuwona. Koma ngati pali. . .

¹¹ Ndi angati odwala ali muno, chonchobe, amene abwera kuti adzapemphereredwe? Tiyeni tiwone manja anu, ponse pozungulira, kulikonse. O, mai! Hum! Chabwino, ndi angati akuganiza kuti icho chikanadzakhala chabwino, chifuniro cha Ambuye, kuti titsalire ndi kukhala nacho ichi, kutenga usiku wa

Lolemba, kungopempherera odwala, nkukhala ndi msonkhano wa machiritso Lolemba usiku? Kodi inu mukanakonda kuchita izo? Inu mungakhoze kuchita izo? Chabwino, Ambuye akalola, ife tidzachita icho ndiye. Mwawona? Ife tidza—ife tidzakhala nawo msonkhano wa pemphero kwa odwala, Lachitatu, kapena Lamlungu usiku, kapena . . . Lolemba usiku, ndi kupempherera odwala.

¹² Tsopano, ine ndikuyembekeza icho sichikusokoneza gulu lija lomwe ine ndikubwerera nalo, kubwerera ku Arizona. M'bale Norman, kodi iye ali pano paliponse? Kodi icho chikusokoneza dongosolo lanu, M'bale Norman, chirichonse? [M'bale Gene Norman ati, "Ayi."—Mkonzi.] M'bale Fred ndi nonse a inu, kodi izo ziri bwino? [Enawo akuti, "Zabwino."] Mukuwona? Ziri bwino. Chabwino.

¹³ Ndiye, Ambuye akalola, Lolemba usiku ife tipempherera odwala, usiku umodzi chabe wayikidwira pambali kwa izo, palimodzi, kumangopempherera odwala. Tsopano, sipadzakhala chirichonse cha Zisindikizo. Ngati Ambuye adzangotsegula Zisindikizo izi, ndiye ife tipempherera odwala, Lolemba usiku.

¹⁴ Tsopano, o, ine ndakhala kwenikweni ndikusangalala nazo izi, mopambana, pa kutumikira Ambuye pansi pa Izi! Kodi inu mwasangalala nazo Izi, kutsegula kwa Zisindikizo? [Osonkhana ati, "Ameni!"—Mkonzi.]

¹⁵ Tsopano, ife tsopano tikulankhula kuchokera ku Chisindikizo Chachisanu kapena . . . Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi, kani. Ndipo icho chikutitsitsa tsopano kuchokera—ndime ya 12 ya mutu wa 6, kutsika mpaka ku ya 17. Ndicho chimodzi cha Zisindikizo zazitali. Ndizo zinthu zambiri ndithu zikuchitika apa. Ndipo tsopano . . .

¹⁶ Kunena mobwereza pang'ono za usiku watha, kukhala ngati kubwerera pang'ono, nthawi iliyonse.

¹⁷ Ndi, nnena, ine—ine ndikufuna kunena chinachake, apanso. Ine ndinapeza, mu bokosi ilo, zinthu zinai kapena zisanu zofunika kwambiri kwa ine. Ine ndinawuzidwa kuti . . . Ndipo ine ndithudi ndikufuna kupepesa. Kodi matepi ayatsidwa? Tepi yayatsidwa? Ine ndikufuna kupepesa kwa abale anga otumikira ndi kwa inu anthu apa. Iwo akuti, usiku wina pamene ine ndinali kulankhula za—za Eliya, pa ora ilo la pamene iwo anali . . . Iye ankaganiza iye anali mmodzi yekhayo anali woti adzakhale mu Mkwatulo, kapena iye mmodzi yekha akanadzapulumsidwa. Ine—ine ndinati mazana asanu ndi awiri mmalo mwa zikwi zisanu ndi ziwiri. Nkulondola uko? [Osonkhana, "Inde."—Mkonzi.] Chabwino, ine ndikutsimikiza pepani kaamba ka icho, anthu. Ine—ine—ine ndimadziwa bwino kuposa izo. Iko kunangokhala kuphonyetsa kwa kulankhula, chifukwa ine ndimadziwa kuti anali zikwi zisanu ndi ziwiri. Ine sindinalankhule icho molondola basi. Ine . . . Ndipo ine—ine

ndikukuthokoza inu. Ndipo icho chikutanthawuza kuti . . . ine ndiri wokondwa kuti inu mukuyang'anira zomwe ine ndikunena. Ndipo inu mukuwona, ndiye, ndicho . . . Chifukwa, icho, ali—ali zikwi zisanu ndi ziwiri.

18 Ine ndiri nazo zolembe ziwiri kapena zitatu pa icho, zimene zinati, “M’bale Branham, ine ndikukhulupirira inu munalakwitsa.” Izo zikuti, “Kodi iwo sanali zikwi zisanu ndi ziwiri mmalo mwa mazana asanu ndi awiri?”

19 Ine ndinaganiza, “Ndithudi ine sindinanene kuti mazana asanu ndi awiri.” Mukuwona? Icho, ndiyeno ine . . . Billy . . .

20 Ndiyeno ine, chinthu choyamba inu mukudziwa, ine ndinanyamula cholembe china. Icho chinati, “M’bale Branham, inu munali . . . ine ndikukhulupirira inu munati mazana asanu ndi awiri.”

21 Ndipo munthu mmodzi anati, “M’bale Branham, kodi awo anali—masomphenya awuzimu kuti—kuti apo pakhala chabe choyimira, ndipo inu mukufaniziritsa icho ndi asanu ndi awiri . . . ?” Zimawayika anthu pamapeto pamene iwe upita nuganiza zinthu zimenezi, mwawona. Ndipo ndi zokwanira, kuti, izo zimandiyika ine pamapeto.

22 Chinachake chinachitika lero pamene Chisindikizo ichi chinawululidwa, kuti ine ndinachita kukayenda kwathunthu kuseri kwa nyumba, kumangoyenda mozungulira, kuseri kwa nyumba kanthawi pang’ono. Uko nkulondola. Icho basi chinali mophweka pafupi kutenga mpweya wanga pomwepo kwa ine. Mukuwona? Kotero inu mukalankhula, manjenje? O, mai! Mukuwona?

23 Chinthu china, mwawona, inu mukutsamira kumene pa chimene ine ndikunena. Ndipo Mulungu adzandifunsa ine pa chimene ine ndikuwuzani inu. Mukuwona? Ndipo kotero ine—ine ndiyenera mwamtheradi kukhala wotsimikiza monga kutsimikiza konse kungakhale kotsimikiza, mwawona, za zinthu izi, chifukwa iyi ili—nthawi yopambana yomwe ife tikukhalamo moyo. Eya.

24 Ine ndinali kuganiza za msonkhano wa machiritso wa Lolembe usiku. Chimenecho chidzakhala chosokonezana ndi inu, M’bale Neville kulikonse? [M’bale Neville ati, “Palibe kanthu. Ine ndidzakhala pomwe apa.”—Mkonzi.] Icho nchabwino.

25 M’bale Neville wofunika! Ine ndikuwuzeni inu, iwo basi—iwo anangopanga mmodzi, ine ndikuganiza, ndiye anataya kachitidwe. Ndiye . . . Iye ndithudi wakhala ali—bwanawe weniweni ndi mzanga kwa ine, ndikukuwuzani inu.

26 Kachisi tsopano wamangidwa, ndipo ali nazo zipinda za Sande sukulu ndi chirichonse chokonzekera, mu dongosolo pano. Ndipo ena a anthu inu omwe muli ozungulira kuno,

kuzungulira Jeffersonville, amene mumafuna kubwera ku mpingo, inu muli nawo malo abwino, ndi malo woti muzibwerako, zipinda za Sande sukulu.

²⁷ Mphunzitsi wabwino, ndi M'bale Neville apa, kwa kalasi la akulu, ndipo m'busa weniweni. Ine sindikunena izo mwa kuyika maluwa kwa iye, koma ndi bwino ndimupatse iye duwa laling'ono tsopano kuposa nkhatu yonse iye atapita kale. Ndipo M'bale—M'bale Neville, ine ndamudziwa iye kuyambira ndiri mnyamata chabe. Tsopano, iye sanasinthe chidutswa chimodzi. Iye akadali Orman Neville, monga momwe iye nthawizonse anali.

²⁸ Ine ndikukumbukira ndikukacheza. Ngakhale nso iye anali nacho chisomo chokwanira kundifunsa ine kupita ku guwa lake pamene anali mlaliki wa Methodist kumusi kuno mu mzinda. Ndipo ife tinali nalo gulu labwino kumusi kumeneko mu Clarksville, a... ine ndikuganiza kumeneko kumatchedwa Howard Park, Mpingo wa Methodist ku Harrison Avenue. Ine ndikuganiza ndiko kumene iye ayenera kuti anakupezani inu, kumusi uko, Mlongo Neville. Kumusi uko, chifukwa iye anali mamba-...

²⁹ Ine ndinabwerera, ndipo ine ndinati kwa mpingo kuno, ine ndinati, "Uwo unali... Ndiye mmodzi wa anthu abwino zedi! Ndipo limodzi la masiku amenewa ndidzamubatiza iye mu Dzina la Ambuye Yesu." Ichu chinachitika.

³⁰ Apa iye ali. Ndipo tsopano iye ndi bwanawe, motsatira kumene pambali panga. Ndipo wawulemu chotero, munthu wolemekezeka! Iye nthawizonse wayima pambali panga monga ngati... moyandikira basi monga momwe iye angakhoze kuyimira. Chirichonse chimene ine ndinganene, iye amangokhala nane ine ndi kukangamira basi motsatira. Ngakhale pamene iye anabwera muno koyamba, iye sankawumvetsa Uthenga panthawiyo, koma iye anawukhulupirira Iwo ndipo anakhala nawobe Iwo. Ndiwo ulemu, ndiwo malemekezo, kwa m'bale monga choncho. Ine sindingamunenere iye zokwanira. Ndipo tsopano Ambuye amudalitse iye. Chabwino.

³¹ Tsopano kubwereza pang'ono za usiku watha, mu kumatula kwa Chisindikizo Chachisanu. Ife sitibwerera njira yonse mmbuyo usiku uno, kungobwerera motalika kukwanira kuti titenge—Chisindikizo Chachisanu.

³² Tsopano, ife tikupeza kuti apo panali wotsutsakhristu amene anakwerapo, ndi kudzadzitsirizitsa yekha, kuchokera ku mphamvu zitatu. Zonse zinalowa ku mphamvu imodzi, ndipo anakwera kavalo wotumbululuka, "Imfa," mpaka kuphomphe lopanda malire, mpaka ku chiwonongeko, kumene iye anachokera. Ndiyeno ife tikupeza pamene...

³³ Lemba limati, “Pamene mdani alowa mkati ngati kusefukira kwa madzi, Mzimu wa Mulungu umadzutsa muyezo wotsutsa iko.” Ndipo ife tinaziwona izo zikutsimikiziridwa mwangwiro mu Mawu usiku watha, pakuti panali Zamoyo zinai zomwe—zomwe zimayankha kwa—nthawi zinai zomwe wokwera uyu anakwera.

³⁴ Ndipo iye anakwera kavalo wosiyana nthawi iliyonse, kavalo woyera, ndiyeno kavalo wofiira, ndi kavalo wakuda, ndiyeno kavalo wotumbululuka. Ndipo ife tinapeza, mitundu imeneyo, ndi chimene iyo inali ndi chimene iyo inachita. Ndiye kuzitengera izo kubwerera nazo mu mibadwo ya mipingo, ndipo chimodzimodzi ndicho chimene iyo inachita, mwangwiro basi.

³⁵ Chotero, inu mukuwona, pamene Mawu a Mulungu akulumikizana pamodzi, icho chimatanthawuza kuti Iwo akulondola, inu mukuwona. Eya. Ine ndikukhulupirira, chirichonse chimene chimagwirizana nawo Mawu a Mulungu chiri nthawizonse “ameni.” Mukuwona?

³⁶ Tsopano, monga munthu anati iwo anali nawo masomphenya, ndipo ananena kuti iwo anali. O, iwo akudziwa kuti Ambuye anawapereka iwo, chifukwa iwo anabwera ndi mphamvu yayikulu. Chabwino, masomphenyawo akhoza kukhala abwino. Koma ngati sali limodzi nawo Mawu, ndipo akusiyana ndi Mawu, iwo sali olondola. Mukuwona?

³⁷ Tsopano, tsopano akhoza kukhalapo, abale ena a Achimormoni kapena mlongo. Ndipo akhoza kukhalapo ena ati atenge matepi awa, tsopano. Ndipo ine sindikufuna kunena izo. . . Ena a anthu abwino omwe ine ndi inu tikufuna kukumana nawo, akhoza kukhala—kukhala mwa anthu Achimormoni; anthu a mtundu wabwino kwambiri. Ndiyeno wawo—mneneri wawo, Joseph Smith, yemwe anthu Amethodisiti anamupha kuno mu Illinois, pa ulendo wawo kumeneko. Ndipo kotero ndiye uyo—munthu wabwino uyo, ndipo masomphenyawo, ine sindikukayikira konse koma kuti iye anali nawo masomphenya. Ine ndikukhulupirira iye anali munthu wodzipereka. Koma masomphenya omwe iye anali nawo anali osiyana nalo Lemba. Mukuwona? Chotero, iwo anachita kukhala nalo Baibulo la Chimormoni, kuti—kuti apange izo. Mukuwona?

³⁸ *Ili* ndilo Ilo apa, kwa ine. Ili ndilo. Ndicho chifukwa, Mawu basi. Ndicho Icho. Mukuwona?

³⁹ Nthawi imodzi, m—m—m—mtumiki anabwera kuno kuchokera ku dziko lakutali, ndipo iye. . . Ndipo ine ndinamuwona iye akutuluka naye a—a. . . atakwera nkumazungulira mu galimoto, ndi yemwe sali. . . ndi d—dona. Ndipo iwo anabwera ku msonkhano. Ndipo ine ndinapeza kuti, iwo anali atayenda masiku awiri kapena atatu, iye yekha ndi mkaziyo, mu msonkhano, kuti abwere ku msonkhano, limodzi.

Ndipo mkaziyo anali atakwatiwa, katatu kapena kanayi nthawi zosiyana.

⁴⁰ Ndipo mtumiki uyu analowa mu pofikira ku hotelo kumene ine ndinali, ndipo tinakomana ndi kugwirana nane dzanja. Ndipo ine ndinagwedeza dzanja lake, ndinadzuka ndipo ndinali kulankhula kwa iye. Ine ndinamufunsa iye, ine ndinati, “Pamene inu muli womasuka, kodi ndingakhoze kulankhula kwa inu mu chipinda changa kamphindi chabe?”

Iye anati, “Ndithudi, M’bale Branham.”

⁴¹ Ine ndinamutengera iye ku chipinda. Ndipo ine ndinati kwa mtumikiyo, ine ndinati, “M’busa, bwana, ndinu mulendo mu dziko lino.” Ine ndinati, “Koma dona uyu ali nalo dzina ndithu.” Ine ndinati, “Kodi . . . Ndipo inu mwabwera njira yonse kuchokera ku malo *akuti-ndi akuti*, mpaka ku malo *akuti-ndi akuti*?”

Anati, “Inde, bwana.”

⁴² Ndipo ine ndinati, “Kodi inu simukuwopa kuti icho chidzakhala ngati . . . Ine sindikukayikirani inu, koma kodi inu simukuganiza kuti icho chidzawalira pa mbiri yanu monga mtumiki? Kodi inu simukuganiza kuti ife tiyenera kuyika chitsanzo chabwino pang’ono kuposa icho?”

Ndipo iye anati, “O, dona uyu ndi woyera.”

⁴³ Ine ndinati, “Ine—ine sindikukayikirira izo.” Koma ine ndinati, “Koma, m’bale, chinthu chake chiri kuti, aliyense amene akuyang’ana pa iye sali woyera, mwawona, omwe akuyang’ana pa chimene inu mukuchita.” Ndipo ine ndinati, “Ine ndikukhulupirira inu munayenera kukhala wosamala. Ndicho kokha m’bale mmodzi kwa wina.” Ndipo iye anati . . . Ine ndinati, “Donayo wakwatiwapo kanai kapena kasanu tsopano.”

Ndipo iye anati, “Inde, ine ndikudziwa izo.” Anati, “Inu mukudziwa, ine—ine . . .”

⁴⁴ Ine ndinati, “Inu simumaphunzitsa zimenezo mu mpingo wanu kwanu, kodi mumatero, pa zimenezo?”

⁴⁵ Koteri anati, “Ayi. Koma,” anati, “inu mukudziwa, ine ndinali ndi masomphenya a izo, M’bale Branham.”

Ine ndinati, “Chabwino, izo nzabwino.” Ine ndinati . . .

⁴⁶ Iye anati, “Kodi inu mukusamala?” Anati, “Ine ndikukhulupirira ine ndikhoza kukuwongolani inu pang’ono pokha pa kuphunzitsa kwanu za izo.”

⁴⁷ Ndipo ine ndinati, “Chabwino.” Ndipo iye . . . ine ndinati, “Ine—ine ndidzakhala wokondwa kudziwa izo, bwana.”

⁴⁸ Ndipo iye anati, “Chabwino,” anati, “inu mukudziwa, mu masomphenya awa,” iye anati, “Ine ndinali nditagona.”

Ndipo ine ndinati, “Eya.” Ine ndinawona, ndiye, anali maloto. Mukuwona?

49 Ndipo iye anati, “Wanga—mkazi wanga,” anati, “iye anali akukhala ndi mwamuna wina,” ndipo anati, “ndi kuthamanga chozemba pa ine.” Ndipo anati, “Ndiye iye anabwera kwa ine, ndipo iye anati kwa ine, ‘O, wokonedwa, mundikhululukire ine, mundikhululukire ine!’ Anati, ‘Ine—ine—ine—ine ndalakwa ndinachita izo. Ine ndidzakhala woona kuchokera tsopano mpaka mtsogolo.” Anati, “Zedi, ine ndinali kumukonda iye kwambiri, ine ndinangomukhululukira iye, ndinati, ‘Chabwino.’” Ndipo anati, “Ndiye. . .”

50 Ndipo anati, “Kodi inu mukudziwa chiyani? Ndiye ine ndinapeza tanhawuzo la masomphenya awa.” Anati, “Mkazi wake anali ameneyo.” Anati, “Zedi, iye wakwatiwa, ndi—ndi zina zotero, ndipo nthawi zonse izi.” Ndipo ananena, kuti, “Chiri chabwino kwa iye kuti akwatiwe, chifukwa Ambuye anamukonda iye kochuluka choncho. Iye akhoza kukwatiwa nthawi zochuluka monga mmene iye akufunira, malingana ngati. . .”

51 Ine ndinati, “Masomphenya anu anali okoma mwamphamvu, koma iwo anali kutali kwa Njira yopunthidwa apa.” Ine ndinati, “Ndicho—ndicho cholakwika, mukuwona. Inu simumayenera kuchita izo.” Kotero kuti. . . Mwawona?

52 Koma pamene inu muwona Lemba, likulumikizana ndi Lemba, kuchipangitsa icho kupitirizika kosasintha pamene iwo abwera pamodzi. Malemba, pamene Awa akuchoka apa, amodzi ena Awa apa akubwera ndi kululumikizana umo, ndi kujambula chithunzi chonse.

53 Monga kuyika mawu opingatsana pamodzi, monga. Iwe umapeza chidutswa chimene chiti chikwaniremo. Palibe chirichonse chimene chingakhoze kukwaniramo. Ndiye inu mukulumikiza chithunzicho.

54 Ndipo pali Mmodzi yekha amene angachite izo, ndiye Mwanawankhosa, ndipo kotero ife tikuyang’anira kwa Iye.

55 Koma ife tikupeza kuti pamene awa, wokwera uyu, iye anali wokwera mmodzi yemwe anakwera akavalo awa. Ndiyeno ife tamuthamangitsa iye mpaka mmusi, ndi kuwona chimene iye anachita ndi chirichonse, ndi kupeza, mmbuyo mu mibadwo ya mpingo ndicho chimodzimidzi chimene iye anachita.

56 Ndiye pamene iye anatuluka pa chamoyo china ndi kukachita chinthu china, ife tikupeza kuti apo panali mmodzi anatomizidwa kukamenyana nacho chimene iye anachita.

57 Panali mmodzi wotumidwira kwa m’badwo woyamba, wa mwanawankhosa. . . wa mkango. Amenewo anali Mawu, ndithudi, Khristu.

58 Yotsatira inali ng’ombe, mu nthawi ya m’badwo wa mdima, pamene—pamene m—mpingo unali utachita bungwe ndipo unali utalandira miyambi mmalo mwa Mawu.

⁵⁹ Ndipo kumbukirani, chinthu chonsecho chakhazikika pa zinthu ziwiri: chimodzi, wotsutsakhristu; chimodzi chinacho, cha Khristu.

⁶⁰ Chikadali chinthu chomwecho lero. Palibe Mkhristu wa theka. Palibe munthu wakumwa bwino; palibe mbalame zakuda-zoyera; ayi, ayi; palibe wochimwa-woyera. Ayi. Ndiwe mwina wochimwa kapena woyera. Mukuwona? Palibe kukhala pakati pokha. Ndiwe mwina wobadwa kachiwiri kapena ndiwe wosabadwa kachiwiri. Ndiwe mwina wodzazidwa nawo Mzimu Woyera kapena ndiwe wosadzazidwa nawo Mzimu Woyera. Ziribe kanthu kaya iwe unali ndi kugirigisha kungati, ngati iwe sunadzazidwe nawo Mzimu Woyera, iwe sunadzazidwe nawo Iwo. Mukuwona? Ndipo ngati iwe wadzazidwa nawo Iwo, moyo wako umasonyeza izo, umapita mpaka mmwamba kwa Iwo. Mukuwona? Palibe aliyense ayenera kumuwuza aliyense za icho. Iwo akuwona izo, mwawona, chifukwa Chiri Chisindikizo.

⁶¹ Tsopano, ndipo ife tikuzipeza zamoyo zimenezo, momwe izo zinkakwerera nthawi iliyonse. Chimodzi kutumizidwa pa utumiki wake, mu mphamvu zandale, kulumikizanita mphamvu zachipembedzo ndi—ndi mphamvu zandale, pamodzi. Ife tikuzipeza, Mulungu ankatumiza mphamvu Yake kukamenyane nayo iyo. Ife tibwerere kumene mmbuyo ndi kukawona chimene m’badwo wa mpingo unali, ndi kupenya mmbuyo; ndipo apo izo ziri, chimodzimidzi basi mwanjira iyo.

⁶² Ndiye ife tikuzipeza, m’badwo wina ukubwera motsatira, ndipo mdani ankatumiza wotsutsakhristu pansu pa dzina la chipembedzo, pansu pa Dzina la Khristu, pansu pa dzina la Mpingo. Inde, bwana. Ankatuluka pansu pa dzina la Mpingo, ngakhale. “Umenewo unali Mpingo weniweni,” iye anatero. Mukuwona?

Wotsutsakhristu sali Russia. Wotsutsakhristu sali ameneyo.

⁶³ Wotsutsakhristu ali wapafupi kwambiri monga Chikhristu chenicheni, mpaka, Baibulo linati, “Iye akanadzapusitsa chirichonse chimene sichinakonzedweretu.” Uko nkulondola. Baibulo linanena kuti, “Mu masiku otsiriza, chirichonse chimene sichinakonzedweretu, Osankhidwa.” Ilo likuti, “Osankhidwa!” Tsopano, aliyense, atenge mawu amenewo ndi kubwerera nawo iwo mu mphepete mwanu, muwona chomwe iwo amatanthawuza. Ilo likuti, “Osankhidwa, okonzedweratu.” Mukuwona? “Iye akanadzapusitsa aliyense wa iwo amene maina awo sanali pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa kuchokera pa makhazikitsidwe a dziko.”

⁶⁴ Pamene Mwanawankhosa anaphedwa, maina analembedwa pa Bukhu. Iye akuyimirira mu Malo Woyera usiku uno, mu Ulemerero, monga Wotetezera, kupangira chitetezero kwa mmodzi aliyense wa miyoyo iyo yomwe maina awo ali pa Bukhu limenelo. Ndipo palibe amene amalidziwa dzina limenelo koma

Iye. Iye ali Mmodzi yemwe ali nalo Bukhu mu mdzanja Lake, ndipo Iye akudziwa. Pamene mmodzi wotsirizayo adzalowa mkati, ndiye masiku Ake otetezera atha. Iye akutulukira ndiye kudzatenga zomwe Iye wazitetezera. Iye akuchita ntchito ya Wowombola Wachibale tsopano; ndipo akubwera kudzalandira Ake Omwe. O, mai!

⁶⁵ Ichu chiyenera kumuyika Mkhristu aliyense ku—ku kudzifufuza yekha, ndi kugwira manja ake pamaso pa Mulungu, ndi kunena, “Mundiyeretse ine, O, Ambuye! Muyang’ane mmoyo wanga, ndipo—ndipo mundilole ine—mundilole ine ndiwone pamene pali mbali yanga yoyipa. Mundilole ine ndiyichotse iyo pa njira, mwamsanga kumene.” “Pakuti ngati olungama akapulumutsidwe mochepa, nanga wochimwa ndi wopanda umulungu akawonekera pati?” Ndi nthawi-yofufuza.

⁶⁶ Ndipo ngati inu mukanachiyika icho, ndi kufuna kuti . . . ndi kupereka Mawu awa. (Tsopano, ine sindikufuna kuti, kuti inu mundifunse funso pa izi, chifukwa izo zimanditengera kuwolokera pa zina; ine ndikutanthawuza, mu kulemba mafunso anu. Ine ndikuganiza mafunso alembedwa, mulimonse.) Iyi ndi nthawi yofufuza chiweruzo. Uko nkulondola. Tsopano, ife tidzapeza izo pa—pa Malipenga pamene ife tidzabwera kwa izo, pamene Ambuye adzapereka, kapena Mbale, ndipo ife tidzapeza pa kufufuza kwa chiweruzo uko, chabe pamene Matsoka asanapitepo. Ndipo—ndipo ife tikuwona kuti izo ziri zowona. Ndipo Angelo atatu amene anakantha dziko lapansi, akulira, inu mukudziwa, “Tsoka! Tsoka! Tsoka kwa okhala a mdziko lapansi!”

Ndipo ife tikukhala mu nthawi yowopsya, nthawi imene . . .

⁶⁷ Inu mukuwona, zinthu izi zomwe ife tirimo tsopano, zomwe ife tikuwerenga pakali pano, ziri Mpingo utapita kale, mwawona, zinthu izi mu nthawi ya Chisawutso. Ndipo ine ndikuganiza izo ziyenera kukhazikika mowona mu mtima wa wokhulupirira aliyense, kuti Mpingo uwu sukutenga nthawi ya Chisawutso. Inu simungawuyike, paliponse, Mpingo mu Chisawutso. Ine . . . Inu muwuyike mpingo pamenepo, koma osati Mkwatibwi. Mwawona, Mkwatibwi wapita kale.

⁶⁸ Chifukwa, mukuwona, Iye, Iye alibe tchimo limodzi, palibe kanthu komutsutsa Iye. Chisomo cha Mulungu chamuphimba Iye. Ndipo bulitchi yatengera tchimo lirilonse kutali, palibe ngakhale nkomwe kukumbukirika kwa ilo; palibe kanthu koma chiyero, wangwiro, mu Kukhalapo kwa Mulungu. O, izo ziyenera kumupanga Mkwatibwi kugwada pa mawondo Ake ndi kulirira kwa Mulungu!

⁶⁹ Ine ndikuganiza za kankhani kakang’ono; ngati ine sindikutenga nthawi yanu yochuluka tsopano, mu zoyambirira izi. Ine ndiri . . . ine—ine ndimachita izi kwa cholinga, kuti

ndimverere, mpaka ine nditamverera Mzimu mwabwino basi, kuti ndiyambe.

70 Ichi ndi—ichi ndi chinthu chopatulika. Mukuwona? Ndicho, mwawona, ndani amene amadziwa zinthu zimenezo uko? Palibe koma Mulungu. Ndipo izo sizimayenera kuti ziwlulidwe, ndipo zatsimikiziridwa mu Baibulo kuti izo sizikanadzawululidwa, mpaka tsiku lino. Uko nkulondola chimodzimodzi. Mukuwona? Izo zinali—izo zinapenedwa; koma tsopano ife tiyenera kuzitenga izo chimodzimodzi, Chowonadi, Chowonadi chotsimikiziridwa. Mukuwona? Zindikirani.

71 Tsopano, apo panali m—msungwana wamng’ono kumadzulo, yemwe momwe iye anali—iye analowa mu chikondi ndi... Mwamuna analowa mu chikondi naye iye. Monga wogula ng’ombe, anabwera kumeneko mmalo mwa Armour Company. Ndipo—ndipo iwo anali w—wamkulu... .

72 Bwana anabwera tsiku limodzi, mwana wa bwana kuchokera ku Chicago, ndipo, zedi, iwo anawayika iwo pa mndandanda, malire akumadzulo. A—asungwanawo kumeneko, iwo anavala; mmodzi aliyense ankafuna kuti amutenge mnyamata uyu, ndithudi, inu mukudziwa, chifukwa ameneyo anali mnyamata wa bambo wamkulu. Kotero, iwo anavala mu za kumalire a kumadzulo.

73 Ndipo—ndipo iwo iwo amachita zimenezo kumadzulo uko. Iwo angotsiriza kumene umodzi wa miyambo imeneyo. Ndipo M’bale Maguire, ine ndikuganiza iye ali pano tsopano, iwo anamugwira iye kumusi kwa mzinda wosavala zovala zake za kumadzulo, ndipo iwo anamuponyera iye mu—mu ndende. Ndi kumuyika iye mubwalo la mirandu la kangaroo, ndi kumulipiritsa iye chifukwa cha icho, ndiyeno kumpangitsa iye kupita kukagula chovala chakumadzulo. Ndipo ine ndinawawona ena onsewo akuyendayenda ndi mfuti pafupi zazitali *chonchi*, atapachikira pa iwo. Iwo amangopita mwaumbadwa kumeneko. Iwo akuyesera kukhala moyo mu chinachake mu masiku ammbuyo opita, opita kale. Mukuwona?

74 Ndiyeno, mu Kentucky, inu mukuyesera kukhala moyo wa mmasiku ammbuyo akummawa kuno, akubwererabe mu Chigwa cha Renfro ndi zinthu. Inu mumakonda kubwerera ku masiku akale. Pali chinachake chikuyambitsa icho.

75 Koma pamene chibwerera mmbuyo, kuti mubwerere ku Uthenga mu chiyambi, inu simukufuna kuchita izo. Inu mukufuna chinachake chamakono, inu mukuwona. Zimangosonyeza kuti, onani, inu—inu... . apo pali... .

76 Ndipo nchiyani chimampangitsa m—munthu kuchita cholakwika? Nchiyani chimampangitsa iye kumwa ndi kumapitirirabe, kapena mkazi kuchita cholakwika? Chiri chifukwa iye akuyesera ku... . Pali chinachake mwa iye, chikuchita ludzu. Pali chinachake mwa iye, chikuchita ludzu.

Ndipo iwo akuyesera kuthetsa ludzu loyera ilo ndi zinthu za mdziko. Pamene, Mulungu anayenera kukhala chothetsa ludzuchoko. Iye anakupangani inu mwanjira imeneyo, kuti muzimva ludzu. Ndicho chifukwa chake inu mumamva ludzu la chinachake. Mulungu anakupangani inu mwanjira imeneyo, kuti inu mutembenezire ludzu loyeralo kwa Iye. Mukuwona? Koma pamene inu muyesera kuthetsa ludzu ilo. . . Akulimba mtima bwanji aliyense kuchita izo! Inu mulibe ufulu wochitira izo, kuyesera kuthetsa ludzu lopatulika ilo lomwe inu mumamvera ludzu chinachake, ndipo, ndiye, ndipo inu mukutembenezira ilo kwa dziko, kuyesera kukhutitsa ilo ndi dziko. Inu simungakhoze kuchita izo. Pali chinthu chimodzi chokha chimene chidzadzaze ludzu ilo, ndipo ndicho Mulungu. Ndipo Iye anakupangani inu mwa njira imeneyo.

⁷⁷ Koteru, uyu—msungwana wamng’ono uyu anavala c—chovala chakumadzulo kumadzichititsa chifukwa cha mnyamata uyu pamene iye—iye anatulukira. Ndipo mmodzi aliyense wa iwo anali wotsimikiza kuti iwo amakamutenga mnyamata uyu.

⁷⁸ Panali msuwani wamng’ono kumeneko kodyetsera ziweto, ndipo iye anali wamasiiye, ndipo koteru iye ankangochita zonse n—ntchito yonse ya awa. Chifukwa, iwo anali atakonzazikhadababawo, inu mukudziwa, ndipo iwo sakanakhoza kutsuka mbale zawo ndi manja ndi zinthu. Ndipo iye ankagwira ntchito yovuta kwenikweni yonse.

⁷⁹ Ndiyeno, potsiriza, pamene mnyamatayo anabwera, iwo anapita kunja ndipo anakamutenga iye kumulowetsamo mu kachitidwe kakale kumadzulo, ndi ngolo. Ndipo iwo analowa mkati, kuwomba mfuti zawo ndi kumapitirira, inu mukudziwa, ndi kumachita mwasewero. Ndipo usiku umenewo iwo anali ndi kuvina kwakukulu kumeneko, pa—pa kavinidwe-kachikale, ndipo onse osamalira ziweto apozungulira, pafupi, ndi kubwera mmenemo ndi kuvina kwawo, ndi zina zotero. Ndipo, chinthu choyamba inu mukudziwa, bwanji, izi zinkapitirira, chinali chisangalalo cha masiku awiri kapena atatu.

⁸⁰ Ndiye, usiku umodzi, mnyamata uyu anatuluka panja, mpaka. . . kwa malowo, kukangopuma pang’ono ku kuvinako, ndi kuchoka kwa asungwana awa. Ndipo iye anapezeka kuti wayang’ana, akupita mmusi cha ku khola. Uko kunali kudutsa msungwana wamng’ono, wokhala ngati wowoneka-wamasanza. Ndipo iye anali ndi mbale yodzaza madzi, iye ankatsuka mbale. Ndipo iye anaganiza, “Ine sindinamuwonepo iye nkale lomwe. Ine ndikudabwa kumene iye akuchokera?” Koteru iye anangoyamba kuziyika mu njira yake kuti apite chozungulira ku mbali ya nyumba y—yochezera, ndi kupita kumusi kumeneko ndi kubwerera, kumbali ya khola, ndi kukakumana naye iye.

⁸¹ Iye anali wosavala nsapato. Iye anayima. Iye anatsitsira mutu wake pansi. Iye anamuwona yemwe iye anali, ndipo iye anali wamanyazi kwambiri. Iye ankamudziwa munthu wamkulu uyu. Ndipo iye anali chabe msuwani kwa asungwana ena awo. Bambo wawo anali woyang'anira wa pa malo akunja aakulu a Armour awa, kotero iwo anapitiriza . . . Iye anapitiriza kuyang'ana pansi. Iye anali wamanyazi kuti anali wosavala nsapato.

⁸² Iye anati, “Dzina lako ndiwe yani?” Iye anamuwuzwa iye. Anati, “Bwanji iwe sunapite kumeneko ku . . . kumene iwo onse ali?” Ndipo iye anakhala ngati kuwiringula.

⁸³ Ndipo kotero, usiku wotsatira, iye anamuyang'anira iye kachiwiri. Potsiriza . . . Iye anali atakhala kunja uko. Ndipo iwo onse amangopitirirabe, chirichonse. Iye—iye anakhala pa mpanda wakhola ndikumayang'anira iye kuti abwere, kudzataya madzi a mu mbale. Ndipo iye ankamuyang'ana iye. Ndipo iye anati kwa iye, iye anati, “Iwe ukudziwa cholinga changa chenicheni chokhala ndiri kuno?”

Iye anati, “Ayi, bwana, ine sindikudziwa.”

⁸⁴ Anati, “Cholinga changa chokhala ndiri kuno ndicho kusaka mkazi.” Iye anati, “Ine ndapeza chikhalidwe mwa iwe chimene iwo alibe.” Ine ndinali kuganiza za Mpingo, inu mukuwona. Anati, “Kodi iwe ungakwatiwe ndi ine?”

Iye anati, “Ine? Ine? Ine—ine sindingakhoze kuganiza za chinthu choterocho, ine.”

⁸⁵ Mwawona, ndiye mwana wa bwana wamkulu. Iye anali mwini wa makampani onse ndi malo oweta nyama kuzungulira dziko, ndi chirichonse, inu mukuwona. Anati, anati, “Inde.” Anati, “Ine—ine sindinakhoze kupeza mmodzi mu Chicago. Ine—ine ndikufuna mkazi weniweni. Ine ndikufuna mkazi wa khalidwe. Ndipo chinthu chimene ndikuchifunafuna, ine ndachiwona icho mwa iwe.” Anati, “Kodi iwe ungakwatiwe ndi ine?”

Iye anati, “Chabwino . . .” Icho chinamunyumwitsa iye. Ndipo iye anati, “Inde.”

⁸⁶ Ndipo iye anati, “Chabwino . . .” Anamuwuzwa iye kuti adzabwerera. Anati, “Tsopano, iwe uzingodzikonzekera wekha, ndipo chikatha chaka kuchokera lero ine ndidzabwerera. Chabwino . . . Ndipo ine ndidzakutenga iwe, ndipo ine ndidzakutengera iwe kutali kuchoka kuno. Iwe sumakagwiranso ntchito monga chonchi. Ine ndidzakutenga iwe. Ndipo ine ndidzapita ku Chicago, ndipo ine ndidzakumangira iwe nyumba yonga iwe sunayiwonepo konse.”

⁸⁷ Iye anati, “Ine ndiribe, nkomwe—sindinakhalepo ndi nyumba. Ndine wamasiye,” iye anatero.

88 Iye anati, “Ine ndidzakumangira iwe nyumba, imodzi yeniyeni.” Anati, “Ine ndidzabweranso.”

89 Iye anali akumvetsera za iye, mu nthawi iyo, chaka. Iye anagwira ntchito ndi chirichonse chomwe iye akanakhoza kuchita, kuti asunge ndalama zokwanira kuchokera pa dola yake pa tsiku, kapena chirichonse chimene iye ankakhala nacho kwa gulu lake, kuti agulire diresi ya chikwati yake. Choyimira changwiro cha Mpingo! Mukuwona? Mukuwona? Iye anakonzekera zovala zake.

90 Ndipo, inu Mukudziwa, pamene anawonetsa chovala cha chikwati ichi, ake—asuwani ake anati, “Bwanji, iwe mwana wopusa, chitsiru. Iwe ukutanthawuza kuganiza kuti mwamuna ngati amene uja angakhale nacho chochita nawe iwe?”

91 Iye anati, “Koma iye anandilonjeza ine.” Ameni. Anati, “Iye wandilonjeza.” Anati, “Ine ndikukhulupirira mawu ake.”

92 “O, iye amangokupanga iwe kukhala chitsiru.” Anati, “Ngati iye akanatenga winawake, iye akanatenga mmodzi wa iwo.”

93 “Inde,” anati, “koma iye anandilonjeza ine. Ine ndikuyembekezera icho.” Ameni. Ine ndiri, inenso.

94 Kotero, anayamba kuchedwera chedwera. Potsiriza tsiku linafika, ora linalake iye anali woti akhala kumeneko, kotero iye anadziveka mu chovala chake. Ndipo iye anali asanamve konse kuchokera kwa iye. Koma iye anadziwa kuti iye adzakhalapo uko, kotero iye anadziveka mu zovala zachikwati zake, anakonzekera zinthu.

95 Chabwino, ndiye iwo anaseka kwenikweni apa. Chifukwa, bwana wamkulu anali atatumiza kwa—kwa woyang’anira, kapena—kapena kwa. . . Popanda wa asungwana awo anamva kanthu za icho, kotero izo zonse zinali chinthu chachinsinsi kwa iwo. Ichu chiri, nachonso. Ichu ndithudi chiri.

96 Koma msungwana uyu, basi pamaso pa zonse izo, mwa kukhazikika pa mawu ake kuti iye adzabwerera kwa iye.

97 Kotero, iwo anali kumangoseka. Ndi kukolowekana manja awo, wina ndi mzake ndi kumavina momuzungulira iye. Ankati, “Ha!” Kuseka, inu mukudziwa, monga choncho, anati, “Mwana wosawuka, wamng’ono, wopusa!”

98 Iye anangoyima pamenepo, opanda manyazi nkomwe mwa iye. Iye anali atagwirizira maluwa ake. Ndipo chovala chachikwati chake zonse zitakonzedwa; iye anali atavutikira, inu mukudziwa. “Mkwatibwi Wake wadzikonzekera Yekha.” Mukuwona? Iye anangogwirizirabe maluwa ake, akuyembekezera.

99 Iwo anati, “Tsopano, ine ndinakuwuzwa iwe kuti zinali zolakwika. Ukuwona, iye sakubwera.”

Anati, “Ine ndiri ndi maminiti asanu ena.” Anati, “Iye akhala ali pano.”

O, iwo anangoseka!

¹⁰⁰ Ndipo basi pafupi nthawi pamene koloko yakaleyo inagunda mpaka maminiti asanu, iwo anamva akavalo akuthamanga, ndipo mchenga ukuzungulira pansi pa magudumu. Ngolo yachikale inayima.

¹⁰¹ Iye analumpha kuchoka pakati pa iwo, ndi kutuluka pa khomo. Ndipo iye analumpha kuchokera pokwerapo, ndipo iye anagwera mmikono mwake. Iye anati, “Zonse zatha tsopano, wokonedwa.” Anasiya msuwani wake wamng’ono zipembedzo atakhala pamenepo, akuyang’ana. Iye—iye anapita ku Chicago, kunyumba yake.

¹⁰² Ine ndikudziwa za lonjezo lina lalikulu longa ilo, nalonso, komabe. “Ine ndapita kukakukonzerani inu malo; ndikubweranso kudzakulandirani inu.” Iwo akhoza kumanena kuti ife tiri openga. Koma, m’bale, kwa ine, pakali pano, ndipo Zisindikizo izi kumatulika monga chonchi, pansi pa chinthu chawuzimu ichi, ine ndikhoza pafupi kumva mkokomo, pamene koloko ya nthawi iyo ikugundira kulowa ku Muyaya uko. Ine ndikhoza pafupi kumuwona Mngelo ameneyo atayimirira pamenepo ndi kumanena, pamapeto a Uthenga wa mngelo wa chisanu ndi chiwiri uyo, “Nthawi sidzakhalaponso.” Mkwatibwi wamng’ono, wolemekezeka uyo adzawulukira mmikono mwa Yesu limodzi la masiku amenewa, kutengedwera ku Nyumba ya Atate. Tiyeni tiganizire za zinthu izi pamene ife tikupita motsatira tsopano.

¹⁰³ Zindikirani utumiki wa mkango, Mawu; ng’ombe, ntchito ndi nsembe; kukanika, kwa okonzanso; ndi—m’badwo wa mphungu, ukubwera mkati, ndiko kudzawulula ndi kudzatenga zinthu izi ndi kuziwonetsa izo.

¹⁰⁴ Tsopano ife tinazipeza, mu msonkhano wa usiku wathawu, nawonso, chinsinsi chachikulu chinatsegulidwa ndi Chisindikizo ichi, chimene chinali mwamtheradi mosiyana ndi kumvetsa kwanga kwapoyamba. Kumangolingalira kuti izo zinali zolondola, ine nthawizonse ndimayilola miyoyo iyo ya pansi paguwa kukhala Akhristu ofera oyambirira. Koma ife tinazipeza, usiku watha, pamene Ambuye Mulungu anamatula Chisindikizo icho kwa ife, izo mwamtheradi ziri zosatheka. Sanali iwo. Iwo anali atapita ku Ulemerero, mpaka ku mbali yina, ndipo kumeneko iwo anali. Ife tikupeza kuti iwo anali Ayuda amene ati adzabwere mu nthawi, pamene a . . .

¹⁰⁵ Kuchokera pa kuyitana tsopano, kwa zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi, zomwe ife tilowemo usiku uno ndi mawa. Ndi—pakati pa Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi ndi Chisanu ndi chiwiri, zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi akuyitanidwa.

106 Ndiyeno ife tikuzipeza, kuti iwo anali ofera amene anali ataphedwa, ndipo komabe anali asanati...Anali atavala miinjiro yoyera, koma maina awo anali ali pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa. Ndipo iwo anapatsidwa miinjiro yoyera, mmodzi aliyense wa iwo. Ndipo ife tinatenga izo. Ndipo sikanthu mu dziko, ine sindikukhulupirira, koma gulu ilo la—la Ayuda limene linapyola mu nthawi ya chisawutso isanafike. Pamene, mu nthawi ya nkondo zotsiriza izi, iwo anali...iwo ali... Iwo ayenera kudandwa ndi aliyense. Ndipo Eichmann anapha mamilioni a iwo mu Germany. Inu mwamva kumene mulandu. Mamilioni a anthu osalakwa anaphedwa, Ayuda, basi chifukwa iwo anali Ayuda; popanda chifukwa china.

107 Baibulo linanena apa, kuti, “Iwo anaphedwa chifukwa cha umboni wawo wa Mulungu, chifukwa—Mawu a Mulungu, ndi umboni umene iwo anagwirizira.” Tsopano ife tikupeza kuti Mkwatibwi anali Mawu a Mulungu ndi umboni wa Yesu Khristu. Awa analibe umboni wa Yesu Khristu.

108 Ndipo ife tikupeza kuti Baibulo likunena, kuti, “Onse a Israeli, Israeli wokonzedweratu, adzapulumutsidwa,” Aroma 11. Tsopano ife tikudziwa izo. Ndipo pamene ife tinawona miyoyo imeneyo.

109 Tsopano penyani kuyandikira kwake. Chifukwa chiyani izi sizikanakhala kale? Chifukwa izo zinali zisanachitikepo kale. Tsopano inu mukhoza kuwona izo, inu mukuwona. Mwawona, Mzimu Woyera waukulu, kumawona zinthu zimenezo zikubwera mmusi kupyola m—mibadwo ndi nthawi. Ndipo tsopano izo zikuwululidwa, ndiyeno inu mukuyang’ana kumeneko ndi kuwona kuti ndicho Chowonadi. Apo pali pamene izo ziri.

110 Tsopano, iwo anali—iwo anali ofera mu chisawutso, kapena chisawutso-chisanachitike, a Eichmann. Tsopano, iwo akungoyimira chabe ofera a zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi, amene ife tikulowamo, pakati pa Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi ndi Chisanu ndi chiwiri. Mukuwona?

111 Ndipo Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri chiri chabe chinthu chimodzi, ndizo zonse, ndipo ichi, “Kunali chete Kumwamba kwa danga la theka la ora.” Ndipo tsopano Mulungu yekha akhoza kuwulula icho. Icho sichikuphiphiritidwa nkomwe, paliponse. Ndiwo mawa usiku. Mundipempherere ine. Mukuwona?

112 Tsopano, ife tikuzindikira tsopano, pamene ife tikulowa mu Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi. Tsopano Atate Akumwamba atatithandiza ife pamene ife tikukhazikika panso tsopano ku Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi ichi. Tsopano ndime ya 12 iyi ya mutu wa 6.

Ndipo ine ndinapenya pamene iye ...anatsegula chisindikizo chachisanu ndi chimodzi, ndipo, tawonani, kunali chivomezi chachikulu; ndipo dzuwa linakhala

lakuda monga chiguduli cha tsitsi, ndipo mwezi unakhala ngati magazi;

Ndipo nyenyezi za kumwamba zinagwa pa... dziko lapansi, ngakhale monga mkuyu utaya nkhuu zake zosapsya, pamene iwo ugwedezeka ndi mphepo yolimba.

Ndipo miyamba inachoka ngati mpukutu pamene iwo ukulungidwa pamodzi; ndipo phiri lirilonse ndi chisumbu chirichonse zinasuntha kuchoka mmalo awo.

Ndipo mafumu a dziko lapansi, ndi anthu otchuka, ndi anthu olemera, ndi akulu oyang'anira, ndi anthu amphamvu, ndi wansinga aliyense... ndi munthu mfulu aliyense, anadzibisa okha mu mapanga ndi mu matanthwe a mmapiiri;

113 Mwazindikira apo? Penyani pa iwo, “anthu amphamvu,” mwawona. Anali atachita chiyani iwo? “Iwo anali atalandira vinyo wa mkwiyo wa chiwerewere cha hule.” Mukuwona? Ndilo chimodzimodzi gulu lomwelo lomwe linamwa za vinyo wake. Mukuwona?

Ndipo ananena kwa mapiri ndi matanthwe, Igwani pa ife, ndipo tibiseni ife kwa nkhope ya iye amene akhala pa mpandowachifumu, ndi kwa mkwiyo wa Mwanawankhosa:

Pakuti tsiku lalikulu la mkwiyo wake labwera; ndipo ndani ati adzakhoze kuyima?

114 Malonje otani kwa...Mwawona, wokwera tsopano ali, wokwera chirombo, ndipo Zamoyo zoyankha, zafika pakutha. Ndiye, ife tatengedwera mmwamba, ife tikuwawona ofera pansu pa Mpandowachifumu. Tsopano ichi, kuchokera pa nthawi, ofera awa ali Ayuda a Chiorthodox chowona amene anafa mu chikhulupiriro Chachikristu... kapena mu—mu chikhulupiriro chachipembedzo, chifukwa iwo sakanakhoza kukhala Akristu.

115 Kumbukirani, Mulungu anachititsa khungu maso awo. Ndipo iwo akhala akhungu kwa nthawi yayitali, mpaka Mpingo wa Amitundu utachotsedwa pa njira. Chifukwa, Mulungu samachita nawo iwo anthu awiri pa nthawi yomweyo, chifukwa izo nzosiyana kwambiri kwa Mawu Ake.

116 Kumbukirani, Iye amachita naye Israeli monga fuko, nthawizonse. Ndi fuko la Israeli.

117 Amitundu, monga payekhapayekha, “anthu kutengedwa kuchokera kwa Amitundu.” Ndipo zinayenera kutero, Amitundu, anayenera kupanga...kupangidwa ndi anthu onse a mdziko, kotero tsopano ndiyeno pali Myuda akulowa mu chimenecho. Mukuwona? Monga ngati—monga Muluya, ndi Muairishi, ndi Mmwenye, ndi ena onse, ndi anthu onse a mdziko, akupanga mpukutu wa maluwa a Mkwatibwi awa. Mukuwona?

118 Koma, tsopano, pamene zifika pochita ndiye naye Israeli, mu gawo lotsiriza ili la sabata la makumi asanu ndi awiri, Iye akuchita nawo iwo ngati fuko, Amitundu atha. Ora likufika posachedwapa, ndipo mwinamwake nkuti uno—usiku womwe uno, kuti Mulungu atembenuka kwathunthu kuchoka kwa Amitundu, palimodzi. Momwemo! Iye ananena choncho. “Iwo adzapondereza pa makoma a Yerusalemu mpaka nyengo ya Amitundu itatsirizika, nthawi zatha.” Inde, bwana!

119 Ndiyeno, “Musiye niye amene ali woyipa akhalebe chiyipire; msiyeni iye amene ali wolungama akhalabe wolungama.” Mukuwona?

120 Palibenso Magazi pa mpando wa—wa—wa mmalo opatu... mu malo opatulika, konse. Palibenso Magazi pa guwa. Nsembe yachotsedwapo, ndipo palibenso kanthu koma utsi ndi mphezi ndi chiweruzo mmenemo. Ndipo ndicho chimodzimodzi basi chimene chatsanuliridwa apa usiku uno. Mwawona, Mwanawankhosa wasiya kale... ntchito Yake ya ukhalapakati. Ntchito ya ukhalapakati yatsirizika, kuchokera pa Mpandowachifumu. Ndipo Nsembe, monga ife tamufanizitsa Iye mwangwirowo, Wowombola Wachibale, Mwanawankhosa wamagazi amene akubwera. Mwanawankhosa yemwe anali ataphedwa, Mmodzi wamagazi, ataphedwa, atatunduzidwa, akubwera ndi kutenga Bukhu kuchokera m’dzanja Lake. Ndicho, masiku atsirizidwa. Tsopano Iye akubwera kudzatenga zomwe Iye waziwombola. Amen! Izo zikungotumiza chinachake kupyola mwa ine!

121 Ife tikuzipeza tsopano, Yohane anati, “Ine ndinawona pamene Iye anali atasegula Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi, kunali chivomezi chachikulu,” ndiye chirengedwe chonse chinakonezedwa. Mukuwona?

122 Mulungu wakhala akuchita zinthu zazikulu, monga kuchiritisa odwala, ndi kutsegula maso a akhungu, ndi kuchita ntchito zazikulu.

123 Koma ife tikupeza, apa, kuti chirengedwe chinatenga kugwa, inde, chirengedwe chonse. Penyani chimene chinachitika, “C—chivomezi; dzuwa linada, ndipo mwezi sunakhoze kupereka kuwala kwake; ndipo nyenyezi zinagwedezeza ndipo zinagwa.” Ndipo, bwanji, chirichonse chinachitika, mwawona, pa nthawi kumene ya kutsegula kwa Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi ichi. Ndi pamene izo zikuchitika, mofulumira kumene kutachitika kulengeza kwa ofera awo, mwawona. Ofera anali atatsirizika.

124 Tsopano inu mukuwona ife tiri pafupi kumene kulowa mu ora limenero tsopano. Ife tikhoza kukhala, pa nthawi iliyonse, mwawona, chifukwa Mpingo uli chabe pafupi kukonzekera kutenga kuwuluka Kwake. Koma kumbukirani, pamene zinthu izi zikuchitika, Mkwatibwi sakhala ali kuno. Ingokumbukirani,

Mkwatibwi wapita, Iye sakuwona kupyola mu chirichonse cha izo. Iyi ili nthawi ya Chisawutso, ya kuyeretisa kwa m—kwa mpingo; chayikidwa pa iwo, kuti iwo ukapyole mu icho, osati Mkwatibwi. Iye akumutenga wokondedwa Wake kuchoka pa njira. Inde, bwana! Iye, wamuwombola kale Iye. Mukuwona, ziri ngati. . . Ndiko kusankha kwa Iye Mwini, kusankha Kwake Komwe, monga mwamuna aliyense amatenga mkwatibwi wake. Mukuwona? Tsopano, chivomezi. . .

¹²⁵ Tiyeni ife tifanizitse Malemba tsopano. Ine—ine ndikufuna. . . Kodi inu muli nayo pensulo ndi pepala limodzi nanu? Ine ndikufuna inu mundichitire ine chinachake. Pamene inu mukufuna kulemba, lembani izi, chifukwa, pokha ngati inu muti mutenge tepi. Tsopano ife. . . ine ndikufuna inu muwenge ndi ine, pamene inu mukuchita.

¹²⁶ Kufanizitsa Malemba a chochitika chachikulu ichi, chimene ife titi tichiwone kuti chobisika chachikulu ichi, kapena chinsinsi, chimene chinali pansu pa Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi cha Bukhu la Chiwombolo. Tsopano kumbukirani, izi ziri zinsinsi zobisika. Ndipo Zisindikizo zichisanu ndi chimodzi, zonse pamodzi, ziri Bukhu limodzi lalikulu, masikololo asanu ndi limodzi basi okulungidwa pamodzi, ndipo ichi chikufunyulula Bukhu lonse la Chiwombolo. Ndimu momwe dziko lapansi lonse linawomboledwera.

¹²⁷ Ndicho chifukwa chake Yohane analira, chifukwa, ngati panalibe mmodzi aliyense akanakhoza kutenga Bukhu, chirengedwe chonse, chirichonse chinali chitapita. Ilo likanangodzabwerera mophweka ku—ku—ku ma atomu ndi mamolekyulu, ndi zina zotero, ndi kuwala kwa dziko, ndipo nkusakhalaponso chirengedwe, munthu, popanda kalikonse. Chifukwa, Adamu anataya mafulu a Bukhu limenelo. Iye anapinyolitsa ilo pamene iye anamvetsera kwa mkazi wake, ndipo iye anamvetsera ku kulingalira kwa Satana, mmalo mwa Mawu a Mulungu. Mukuwona? Ilo linapinyolitsidwa.

¹²⁸ Ndiye, ilo silikanakhoza kubwerera mmanja akuda a Satana, amene anamuyesa iye kuti achoke pa njira, choncho kotero ilo linabwerera kwa mwini wake wapachiyambi, monga chikalata chamtheradi chirichonse chikanachitira, mwawona. Kubwerera komwe kwa Mwini wake wapachiyambi, ndipo ameneyo anali Mulungu, Mlengi, Yemwe analipanga ilo. Ndipo Iye akugwirizira ilo.

¹²⁹ Ndipo pali mtengo, ndipo ndicho chiwombolo. Panali mtengo wina wa chiwombolo, ndipo panalibe aliyense akanakhoza kuchita icho. Kotero, Iye anati, anapanga malamulo Ake, malamulo Ake Omwe a Wowombola Wachibale. Ndiye, iwo sanakhoze kupeza aliyense. Munthu aliyense anabadwa mwa kugonana, anabadwa mwa kukhumbirana kwa kugonana; iye anali mu tchimo lapachiyambi, Satana ndi Eva, kotero

iyе sakanakhoza kuchita icho. Palibe chirichonse mwa iye. Palibe papa woyera, wansembe, Dokotala Wauzimu, aliyense iye angakhale, iye sakanakhala aliyense woyenera. Ndipo iye sakanakhoza kukhala Mngelo, chifukwa iye anayenera kukhala Wachibale. Iye amayenera kukhala munthu.

¹³⁰ Ndiye Mulungu Mwiniwake anakhala Wachibale, pa kuvala thupi la munthu, kupyolera mu kubadwa mwa namwali. Ndipo Iye anakhetsa Magazi Ake. Amenewo sanali magazi a Myuda. Awo sanali magazi a Wamitundu. Iwo anali Magazi a Mulungu. Mukuwona? Baibulo linati, “Ife tapulumutsidwa kupyolera mu Magazi a Mulungu.”

¹³¹ Mwana amatenga magazi a abambo ake. Ife tikudziwa izo. Chirichonse mwa zazimuna chimatulutsa magazi amoyo. Kotero ife tikupeza kuti, monga nsoti kuyikira dzira; iwo ukhoza kuyikira dzira, koma ngati tambala, kapena wogona naye, sanakhale nawo iwo, ilo silidzaswa. Siliri lachonde. Mkazi ali chofungatira chabe chomwe chimanyamula dzira. Koma dzira limabwera . . . Nyongolosi imachokera kwa champhongo.

¹³² Ndipo, mu nkhani iyi, champhongo chinali Mulungu Mwiniwake. Ndimomomwe ine ndikunenera, momwe kumwamba kuli pansi, ndipo—ndipo chachikulu chiri chaching’ono. Mulungu anali wamkulu kwambiri mpaka Iye anakhala, ngakhale kudzipanga Yekha mu kachinthu kakang’ono chotero, ku kanyongolosi kakang’ono kwambiri mpaka mu chibereko cha namwali. Ndipo mozungulira iko Iye anayambitsa makhungu ndi Magazi. Ndipo anabadwa, ndipo analeredwa pa dziko lapansi. Ndipo kuchokera pa kuyamba kwa mtundu umenewo, wosakhudzidwa, wopanda chikhumbo choganana kwa icho, nkomwe.

¹³³ Ndiyeno Iye anapereka Magazi amenewo, chifukwa Iye anakhala wachibale kwa ife. Ndipo Iye anali Wowombola Wachibale. Ndipo Iye anakhetsa Magazi amenewo, mwawulere. Iye sanasowe kutero. Iye anapereka Iwo kwawulerere, kuti awombole.

¹³⁴ Ndiye Iye akupita pa guwa la Mulungu, ndipo akuyembekezera pamenepo, pamene Mulungu akugwirizira Bukhu la Chiwombolo mmanja Ake. Ndipo Mwanawankhosa wamagazi akuyimirira pa guwa la nsembe. Pamenepo pali Mwanawankhosa kuti apange chiwombolo, kupanga chitetezero.

¹³⁵ Ndiye, wina angayelekeze bwanji kunena kuti Mariya, kapena Yosefe, kapena wachivundi wina aliyense, angakhoze kukhala—kukhala wotetezera! Inu simungakhoze kutetezera pokha pali Magazi pamenepo. Inde, bwana. “Pali Mkhlapakati mmodzi pakati pa Mulungu ndi munthu, ndipo ndiye Khristu Yesu.” Ndicho chimene Lemba limanena. Apo Iye akuyima, ndipo mpaka moyo wotsiriza unali utawomboledwa; ndiyeno Iye

akubwera kudzatenga zomwe Iye waziwombola. O, ali—ali Atate wamkulu bwanji Iye!

¹³⁶ Tsopano kumbukirani, tsopano, ine nthawizonse ndaphunzitsa, kuti, “Mkamwa mwa mboni ziwiri kapena zitatu, mawu aliwonse avomerezedwe.” Ndipo, Lemba, monga ngati inu simungatenge Lemba limodzi ndi kusatsimikizira kanthu pokha apo pali chinachake chimene chikupita nalo ilo. Mukuwona?

¹³⁷ Mwawona, ine ndikhoza kutenga Lemba limodzi ndi kunena, “Yudasi anapita ndi kukadzipachika yekha,” kutenga lina ndi kunena, “Inu mupite mukachite mofanana.” Mukuwona? Koma, onani, icho sichikalumikizana nawo ena onsewo.

¹³⁸ Ndipo ine ndinaganiza, pansi pa Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi ichi, pamene Mzimu Woyera unamatula Icho kuchokera pamenepo, ndipo ine ndinawona chomwe icho chinali, ndiye ine ndinaganiza icho chikanakhala chinthu chabwino kupereka kwa kalasi chinachake chosiyana pang’ono usiku uno. Mukuwona? Chifukwa, icho chikhoza kukhala chotopetsa, mukungomvetsera kwa ine ndikulankhula nthawi zonse, kotero ine ndinaganiza kuti ife tichita chinachake chosiyana.

¹³⁹ Tsopano zindikirani. Chochitika chachikulu ichi chinasinikizidwa pansi pa Bukhu la chinsinsi, cha chiwombolo. Tsopano Mwanawankhosa ali nalo Ilo mu dzanja Lake, kuti alimatule Ilo.

¹⁴⁰ Tsopano tiyeni tipenye ku Mateyu mutu wa 24, Mwanawankhosa Mwiniwake akulankhula. Tsopano, aliyense akudziwa kuti Khristu ali mlembi wa Bukhu lonse, malingana momwe izo zikukhudzidwa. Koma uku kuli Kwake—kulankhula Kwake apa, kapena Lake—ulaliki Wake kwa a—anthu, chabwino, kwa Ayuda.

¹⁴¹ Tsopano ine ndikufuna inu mugwirize Bukhu lanu monga *chonchi*, Mateyu 24 ndi Chivumbulutso 6, monga *chonchi*. [M’bale Branham wagwirizira Baibulo lake lotsegulidwa pa mitu iwiri iyi—Mkonzi.] Ndipo tiyeni tifanizitse chinachake apa chabe pang’ono pokha.

¹⁴² Tsopano, yang’anani ichi tsopano, ndipo inu mukhoza kuzipeza chabe momwe—momwe izo ziliri. Mwawona, chimene Mwanawankhosa *apa* akusonyeza, chimodzimodzi mu chophiphiritsa, chimene Iye ananena cha *apa* mu Mawu. Kuchita chimodzimodzi, kotero kuti zikupanga icho kulondola. Tsopano, ndicho—ndicho chonse chiri kwa icho. Apa pali . . . *Apa* pali mmodzi, Iye akulankhula za icho, ndipo *apa* pali pamene icho chinachitika. Mukuwona? Icho chiri chabe kutsimikizira kwangwiro.

¹⁴³ Tsopano, tsopano tiyeni tiyang’ane pa mutu wa 24 wa Mateyu Woyera, ndi Chivumbulutso 6, ndi kufanizitsa mutu wa 24 wa Mateyu. Ife tonse tikudziwa kuti umenewo unali

mutu umene sikolala aliyense, munthu aliyense amapitapo, ku—kukalankhula za nthawi ya Chisawutso. Izo zimachokera pa mutu wa 24 wa Mateyu. Ndipo tsopano tiyeni. . . Ngati izo ziri choncho, tsopano ife. . . Pakuti, ife tikudziwa kuti Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi ichi chiri Chisindikizo chachiweruzo. Chiri Chisindikizo chachiweruzo, momwemo chomwe Icho chiri.

144 Tsopano, onani, ife takhala nako—kukwera kwa wotsutsakhristu. Tawuwona Mpingo ukupita; tsopano Iwo watsirizika, ukupita mmwamba. Ndiye ife tikuwawona ofera, a iwo Ayuda kumbuyo uko, pansu pa guwa. Tsopano apa pali kumatulidwa kwa chiweruzo, pa anthu amene ali. . .

145 Kuchokera mu chiweruzo cha Chisawutso ichi mudzatuluka zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi Ayuda owomboledwa. Ine nditsimikizira kwa inu kuti iwo ali Ayuda, ndipo osati Amitundu. Iwo alibe chochita naye Mkwatibwi, osati kanthu. Mkwatibwi, ife tamuwona kale Mkwatibwi wapita. Inu simungachiyike icho pena paliponse; osabwereranso mpaka mutu wa 19 wa Bukhu la Machitidwe.

146 Tsopano zindikirani, pakuti, Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi chiri Chisindikizo chachiweruzo cha Mawu.

147 Tsopano, apa, tiyeni tiyambe tsopano ndipo tiyeni tiwerenge Mateyu Woyera, mutu wa 24. Tsopano ine ndikungofuna kukupatsani inu chinachake apa ndangoziyang'ana, kuti ndipeze. Tsopano, Mateyu Woyera, kuchokera 1 mpaka 3, chabwino, ndi pamene ife titi tiwerenge poyamba.

Ndipo Yesu anatuluka, ndipo anachoka ku kachisi: ndipo akuphunzira ake anadza kwa iye kuti adzamuwonetse iye kamangidwe ka kachisiyo.

Ndipo iye anati kwa iwo, Musawone inu zinthu zonse izi? indetu Ine ndinena kwa inu, Sipadzakhala umodzi. . . kukhala utasiyidwa apa mwala umodzi pamwamba pa umzache, umene sudzagwetseredwa pansu.

Tsopano, ndipo (ndime ya 3) pamene iye anakhala. . . phiri. . . Azitona, ophunzira anabwera kwa iye mwapadera, kunena, Tiwuzeni ife, pamene zinthu izi ziti zidzakhale? . . . chidzakhala chiyani chizindikiro cha kudza kwanu, ndi cha mathero a dziko?

148 Tsopano tiyeni tiyime pamenepo. Ndime zitatatu izi, izo zinachitika makamaka, Lachiwiri madzulo, Epulo pa 4, A.D. 30. Ndipo ndime ziwiri zoyamba zinachitika madzulo a. . . a Epulo pa 4, mu A.D. 30. Ndipo ndime yachitatu inachitika Lachiwiri usiku wa tsiku lomwelo. Mukuwona?

149 Iwo anabwera ku kachisi, ndipo iwo anamufunsa Iye zinthu izi. “Nanga bwanji *ichi*? Nanga bwanji *ichi*? Tayang'anani pa kachisi wamkulu uyu! Kodi sali wodabwitsa iye?”

Iye anati, “Apo sipadzakhala mwala umodzi wosiyidwa pa umzache.”

150 Ndiye Iye anapita pamwamba pa phiri ndi kukhala pansi, mukuwona. Kuti apo, apo Iye akuyamba; ndi madzulo. Ndiyeno pamene iwo anatero, iwo anamufunsa Iye pamwamba apo, anati, “Ife tikufuna kudziwa za zinthu zina.”

151 Tsopano zindikirani, apa pali—apa pali mafunso atatu amene akufunsidwa ndi Ayuda, ophunzira Ake. Mafunso atatu akufunsidwa. Ndipo yang’anani. “Chiyani,” loyamba, loyamba, “chiyani... Zidzachtika liti zinthu izi?” pamene, ‘Sipadzakhala mwala umodzi wosiyidwa pamwamba pa umzake?’ “Chidzakhala chiyani chizindikiro cha Kudza Kwanu?” funso lachiwiri. “Ndi cha kutha kwa dziko?” Mwawona izo? Apo pali mafunso atatu.

152 Tsopano, apo pali pamene anthu ambiri amalakwitsira. Iwo amaziyika zinthu izi apa kwa m’badwo wina ndiye, pamene, inu mukuwona, Iye akuyankha mafunso atatu. Iwo . . .

153 Yang’anani tsopano momwe—momwe ziriri zokongola, ndime ya 3, onani, ganizo lotsiriza pamenepo mu ndime ya 3. “Ndipo chidzakhala chiyani. . .” Poyamba, iwo anamuyitanira Iye ku phiri la Azitona apa, mwapadera. “Tiwuzeni ife, zidzakhala liti zinthu izi?” funso loyamba. “Chidzakhala chiyani chizindikiro cha Kudza Kwanu?” funso lachiwiri. “Ndi cha matsiriziro a dziko?” funso lachitatu. Mukuwona? Apo pali mafunso atatu osiyana afunsidwa. Tsopano, tsopano ine ndikufuna inu mutembenuze ndi kuyang’ana momwe Yesu apa akuwawuzira iwo za zinthu izi.

154 O, ndi chokongola kwambiri! Ine . . . Chimangondipangitsa ine . . . Ine—ine—ine ndikupeza . . . Anali chiyani mawu aja omwe ife tinagwiritsa ntchito usiku wina? [Osonkhana, “Kukondoweza.”—Mkonzi.] Kukondoweza kuchokera ku vumbulutso! Zindikirani.

155 Tsopano tiyeni titsegule tsopano ku Chisindikizo Choyamba cha—Zisindikizo za Bukhu ili, ndi kufanizitsa Chisindikizo Choyamba ichi ndi funso loyamba ili.

156 Ndipo funso lirilonse, kulifanizitsa ilo mpaka mmusi, ndi kuwona ngati sizikuyenda dzanja mu dzanja, basi monga ife tinachitira mu zinthu zina zonse izi kutsegula, kwa mibadwo ya mpingo ndi chirichonse, chimodzimodzi momwemo. Apo pali Chisindikizo, chitatsegulidwa mwangwiwo, ndiye. Zindikirani, tsopano. Tsopano ife tiwerenga, poyamba, kwa . . . “Ndiye Iye anawayankha iwo . . .” Ndipo—ndiyeno Iye—Iye ayamba kuwayankha tsopano, ndipo ife tikufuna kufanizitsa izo ndi Zisindikizo.

157 Tsopano yang’anani. Chisindikizo Choyamba chiri Chivumbulutso 6:1 ndi 2. Tsopano ife tiwerenge 6:1 ndi 2.

Ndipo—ndipo ine ndinawona...Mwanawankhosa pamene iye anali atatsegula chimodzi cha zisindikizo, ndipo ine ndinamva, ngati kuti unali mkokomo wa bingu, chimodzi cha zamoyo zinai kunena, Bwera ndipo udzawone.

Ndipo ine ndinawona, ndipo tawonani kavalo woyera: ndipo iye amene anakhala pa iye anali nawo uta; ndipo korona anapatsidwa kwa iye: ndipo iye anatulukira akugonjetsa, ndi kukagonjetsa.

158 Munthu ameneyu tinampeza kuti anali ndani? [Osonkhana ati, “Wotsutsakhristu.”—Mkonzi.] Wotsutsakhristu. Mateyu 24, tsopano, 4 ndi 5.

Ndipo Yesu anayankha ndipo anati kwa iwo—kwa iwo, Samalani kuti munthu asakunyengeni inu.

Pakuti ambiri adzabwera mu dzina langa, kunena, ine ndine Khristu; ndipo adzanyenga ambiri.

159 Mwaona izo? Wotsutsakhristu. Apo pali Chisindikizo chanu. Mwawona? Mwawona? Iye wachilankhula icho apa; ndipo apa iwo akutsegula Chisindikizo, ndipo apa iye anali, mwangwiro kumene.

160 Tsopano Chisindikizo Chachiwiri, Mateyu 24:6, Chivumbulutso 6:3 ndi 4. Tsopano yang’anani, Mateyu 24:6. Tsopano ndiroleni ine ndiwone chimene iyo ikunena.

Ndipo inu mudzamva za nkhondo ndi mbiri za nkhondo: onani kuti inu musakhale ovutika: pakuti zinthu zonse izi ziyenera kuchitika, koma chitsiriziro chisanafikebe.

161 Chabwino, tiyeni titenge Chisindikizo Chachiwiri, Chivumbulutso 6:3 ndi...2. Yang’anani zomwe Iye akunena tsopano.

Ndipo pamene iye anali atatsegula chisindikizo chachiwiri, ndipo ine ndinamva chamoyo chachiwiri chikunena, Bwera...udzawone.

Ndipo pamenepo panatuluka kavalo wina yemwe anali wofira: ndipo mphamvu inapatsidwa kwa iye amene anakhala pamenepo kuti akatenge mtendere ku dziko lapansi, ndipo kuti iwo aphane mmodzi ndi mzake: ndipo apo kunapatsidwa kwa iye lupanga lalikuru.

162 Mwangwiro, chimodzimodzi basi! O, ine ndimakonda kupanga Lemba kudziyankha Lokha. Kodi inu simutero? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Mzimu Woyera unalemba Ilo lonse, koma Iye ali wokhoza kuliwulula Ilo.

163 Tsopano tiyeni tizindikire Chisindikizo Chachitatu. Tsopano, iyi ili njala. Tsopano, Mateyu 24:7 ndi 8. Tiyeni tipeze 7 ndi 8, mu Mateyu.

Ndipo fuko lidzawukira motsutsa fuko, ndi ufumu motsutsa ufumu: ndipo apo kudzakhala njala, . . . zowawitsa, . . . zivomezi, mu malo akuti akuti.

Zinthu zonse izi ziri chiyambi cha chisoni.

164 Mukuwona, inu mukubwera bwino tsopano. Tsopano, Chivumbulutso 6, mu wa 6, tsopano ife titsegula Chisindikizo Chachitatu. Icho chikupezeka mu Chivumbulutso 6:5 ndi 6.

Ndipo pamene iye anali atatsegula chisindikizo chachitatu, ine—ine ndinawona chamoyo chachitatu chikunena, Bwera ndipo udzawone. Ndipo ine ndinapenya, ndipo tawonani kavalo wakuda; ndipo iye amene anakhala pa iye anali nawo muyeso mu dzanja lake.

Ndipo ine ndinamva liwu mkati mwa zamoyo zinai likunena, Muyeso . . . rupiya . . . Muyeso wa tirigu wogula rupiya, ndi miyeso itatu ya barele yogula rupiya; ndipo ona ive usawononge mafuta ndi . . . vinyo.

165 Njala! Mwawona, chimodzimodzi Chisindikizo chomwecho, chinthu chomwecho Yesu ananena. Chabwino.

166 Chisindikizo Chachinai, “zowawitsa” ndi “imfa.” Zindikirani, Mateyu 24. Ife tiwerenga n—ndime ya 8, ya 7 ndi ya 8, ine ndikukhulupirira izo ziri, pa Chisindikizo Chachinai ichi, ine ndiri nazo apa. Chabwino.

167 Tsopano, ndinawerenga chiyani pambuyo apa? Kodi ine ndinawerenga chinachake cholakwika? Eya, ine ndachilemba icho. Eya, ife tiri apa. Tsopano ife tikupita. Tsopano ife tipite. Chabwino, bwana.

168 Tsopano tiyeni tiyambire apa pa ya 7, pa ichi, Chisindikizo Chachinai; ndi pa 6:7 ndi 8, pa chimodzi chinacho, pa Chivumbulutso.

169 Tsopano tiyeni tiwone ya 7 ndi ya 8 ya Mateyu 24. Chabwino, tsopano.

Ndipo fuko lidzawukira motsutsa fuko, ndi ufumu kutsutsa ufumu: ndipo kudzakhala njala, . . . zowawitsa, . . . zivomezi, mmalo akuti akuti.

Zinthu zonse izi ziri chiyambi cha chisoni.

170 Tsopano Chisindikizo Chachinai, monga ife tawerenga icho cha apa, chinali . . . Chisindikizo Chachinai, chinali kuyambira ya 7 ndi ya 8, pa china ichi tsopano.

Ndipo pamene iye anali atatsegula chisindikizo chachinai, ndipo tawonani . . . chamoyo chachinai chinati, Bwera ndipo udzawone.

Ndipo ine ndinapenya, ndipo tawonani kavalo wotumbululuka: . . .

171 Tsopano yembekezani. Ine ndapeza izi molakwika. Eya. Eya. Tsopano miniti chabe, tsopano, 7 ndi 8.

172 Tsopano tiyeni tiwone, Mateyu 24:7 ndi 8. Tsopano tiyeni tiwone. Ife tipeza icho. Ndicho Chachitatu, kutsegula, sichoncho? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Mateyu 24:7 ndi 8. Ine ndikupepesa. Tsopano, icho chikutsegula mvula... kapena njala, chikutsegula njala. Chabwino.

173 Tsopano, “miliri” ndi “imfa.” Inde, bwana. Tsopano ife tikupita kwa icho, 7 ndi 8. Tsopano, icho chidzakhala Chisindikizo Chachinai. Tiyeni tiwone pamene ife tikupeza Chisindikizo Chachinai. “Ndipo pamene iye anali atatsegula Chisindikizo Chachinai—Chachinai...” Eya, ali wokwera pa kavalo wotumbululuka, “Imfa,” mwawona.

Ndipo—ndipo ine ndinapenya, ndipo tawonani kavalo wotumbululuka: ndipo iye...kavalo wotumbululuka: ndipo dzina lake amene anakhala pa iye amatchedwa Imfa, ndipo Gehena inatsatira...iye. Ndipo mphamvu inapatsidwa kwa iye pa zinai... madera a dziko lapansi, kukapha ndi lupanga, ndi njala, ndi imfa, ndiponso ndi zirombo za padziko lapansi.

174 Tsopano, mwawona, imeneyo inali “Imfa.”

175 Tsopano, Chisindikizo Chachisanu, Mateyu 24:9-13. Tiyeni tiwone ngati ndapeza ichi molondola, tsopano kachiwiri. Mukuwona?

Ndipo ndiye iwo adzakuperekani inu kuti mukazunzidwe, ndipo adzakuphani inu (ndi zimenezotu): ndipo inu adzakudani mafuko onse chifukwa cha dzina langa. Ndipo pamene...

Ndiyeno ambiri adzakuperekani...ambiri adzakhumudwitsidwa, ndipo adzaperekana wina ndi mzake, ndipo adzadana wina ndi mzake.

Ndipo aneneri abodza ambiri adzawuka, ndipo...adzanyenga ambiri.

Ndipo chifukwa kusayeruzika kudzachuluka, chikondi cha ambiri chidzazirala.

Koma iye amene...adzapirire mpaka kumapeto, yemweyo adzapulumutsidwa.

176 Tsopano, ife tiri pa Chisindikizo Chachisanu tsopano. Ndipo umenewo unali usiku watha, mwawona. “Iwo adzakuperekani inu, kuperekana wina ndi mzake,” ndi zina zotero.

177 Tsopano yang’anani apa pa Chisindikizo, Chachisanu ndi chimodzi, 6:9 mpaka 11. Tsopano tiyeni tipeze chimenecho, Chivumbulutso 6:9 mpaka 11.

Ndipo pamene iye anali atatsegula chisindikizo chachisanu, ine ndinawona pansu pa guwa miyoyo ya

ivo amene anaphedwa chifukwa cha mawu a Mulungu, ndi chifukwa cha umboni umene iwo anagwirizira:

Ndipo iwo anafuwula ndi liwu lalikulu, kunena, Mpakana liti, . . . Ambuye, woyera . . . wooka, muchita inu . . . kuweruza ndi kubwezera magazi athu pa iwo akukhala pa dziko lapansi?

Tsopano, ndipo miinjira yoyera inapatsidwa kwa mmodzi aliyense wa iwo; ndipo kunanenedwa kwa iwo, kuti iwo apumulebe kwa kanthawi pang'ono, mpaka antchito amzawo nawonso ndi abale awo, . . . ayenera kuphedwa monga iwo anatero, zikhale zitakwaniritsidwa.

¹⁷⁸ Tsopano, inu mukuwona, pansi pa Chisindikizo Chachisanu, ife tikupeza—ife tikupeza apa kufera.

¹⁷⁹ Ndipo pansi pa 24:9 cha apa, ife . . . mpaka 13, ife tikupeza aponso kuti iwo anali ofera. “Iwo adzakuperekani inu, ndi kukuphani inu,” ndi zina zotero. Mwawona, Chisindikizo chomwecho kutsegulidwa.

¹⁸⁰ Tsopano, mu Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi, chiri chimodzi chomwe ife tikubwerako tsopano, Mateyu 24:29 ndi 30. 24, ndipo tiyeni titenge 29 ndi 30—ndi 30. Apa ife tiri.

Tsopano, tsopano ife titenganso, Chivumbulutso 6:12 mpaka 17.

¹⁸¹ Ndizo chimodzimodzi zomwe ife tangowerenga kumene. Tsopano mverani kwa ichi, tsopano, chimene Yesu ananena mu Mateyu . . . :29, 24:29 ndi 30.

Mwamsanga chitatha chisawutso cha masiku amenewo . . .

¹⁸² Chiyani? Pamene . . . chisawutso ichi, chisawutso chaching'ono ichi chimene iwo apyolamo apa, mukuwona.

. . . dzuwa lidzadetsedwa, ndipo mwezi sudzapereka kuwala kwake, ndipo nyenyezi zidzagwa kuchokera kumwamba, ndipo mphamvu za . . . miyamba zidzagwedezeka:

Ndiyeno kudzawonekera chizindikiro cha Mwana wa munthu mmwamba: ndiyeno mitundu yonse ya pa dziko lapansi idzabuma, ndipo iwo adzamuwona Mwana wa munthu alinkudza mu mitambo ya kumwamba ndi mphamvu ndi ulemerero wawukulu.

¹⁸³ Tsopano, werengani cha apa mu Chivumbulutso tsopano, c—Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi, chimodzi chimene ife tiripo tsopano.

Ndipo . . . tawonani pamene iye anali atatsegula chisindikizo chachisanu ndi chimodzi, ndipo, onani, kunali chivomezi chachikulu; ndipo dzuwa linada ngati

chiguduli (mwawona?) cha ubweya, ndi mwezi unakhala ngati magari;

Ndipo nyenyezi za kumwamba zinagwa pa dziko lapansi, ngakhale monga mkuyu utaya nkhyu zake zosacha, pamene iwo...wagwedezeka ndi mphepo yamphamvu.

Ndipo miyamba inachoka monga mpukutu pamene iwo ukulungidwa pamodzi; ndipo phiri lirilonse ndi chisumbu chirichonse...zinasuntha kuchoka mmalo ake.

Ndipo mafumu a dziko lapansi, ndi anthu akulu, ndi anthu olemera, ndi oyang'anira akulu, ndi anthu amphamvu, ndi munthu wa mumsinga aliyense,... munthu waufulu aliyense, anadzibisa okha mu mapanga...mu matanthwe a phiri;

Ndipo ananena kwa mapiri ndi matanthwe, Igwani pa ife, ndipo tibiseni ife ku nkhope ya iye amene akhala pa mpandowachifumu, ndi ku mkwiyo—mkwiyo wa Mwanawankhosa:

Chifukwa tsiku lalikulu la mkwiyo wake lafika; ... ndani ati adzakhoze kuyima?

184 Mwangwiro basi, bwererani mmbuyo momwe, onani chimene Yesu ananena apa tsopano mu Mateyu 24:29. Mverani. "Litatha," vuto la Eichmann uyu, ndi zina zotero.

Mwamsanga chitachitika chisawutso cha masiku amenewo dzuwa lidzadetsedwa,...mwezi sudzati—sudzapereka kuwala kwake,...nyenyezi zidzagwa kuchokera kumwamba,...mphamvu za...kumwamba zidzagwedezeka:

Tsopano yang'anani.

Ndiyeno padzawoneka chizindikiro cha Mwana wa munthu mmwamba: ndipo iwo adzawona, ndipo iwo... ndiyeno mitundu yonse ya pa dziko lapansi idzabuma, ndipo iwo adzawona Mwana wa munthu akubwera mu mitambo ya kumwamba ndi mphamvu yayikulu ndi ulemmerero

Ndipo...kutumiza angelo ake, ndi zina zotero, ndi palimodzi...liwu la lipenga, ndipo... adzasonkhanitsa iwo pamodzi...mphepo zinai,... zinalimbana pamodzi.

185 Mukuwona, chimodzimidzi basi, kufanizitsa zimene Yesu ananena mu Mateyu 24, ndi chimene mvumbulutsi apa anatsigula mu Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi, ziri chimodzimidzi basi. Ndipo Yesu anali kulankhula za nthawi ya Chisawutso. [M'bale Branham agogoda pa guwa katatu—Mkonzi.] Mwawona?

186 Poyamba, iye anafunsa pamene zinthu izi ziti zidzakhale, pamene kachisi ati adzachotsedwepo. Iye anayankha ilo. Chinthu chotsatira iye anafunsa, pamene iti idzabwere nthawi. . . Apo kunabwera m'badwo wa ofera. Ndi pamene *izi* ziti zidzachte, pamene wotsutsakhristu akanadzawuka; ndi pamene wotsutsakhristu ati adzachotsepo kachisi.

187 Daniele, momwe ife tingakhoze kupita mmbuyo ndi kukamutenga Daniele mmenemo, pamene iye ananena kuti, kalonga uyu amene akanadzabwera. Inu owerenga mukudziwa zimenezo. Ndipo iye akanadzachita chiyani? Iye akanadzachotsa nsembe za tsiku ndi tsiku, ndi zonse zomwe zikanadzachitika pa nthawiyo. Anati. . .

188 Yesu, ngakhale, kulankhula za izo apa, anatsimikizira izo. Anati, “Pamene inu muwona choyipa chopanga chipasuko, cholankhulidwa ndi mneneri Daniele, chikuyima mu malo oyer.” [M'bale Branham agogoda pa guwa katatu—Mkonzi.] Nchiyani chimenecho? Mzikiti wa Omari, unayima mu malo a kachisi pamene iwo anamuwotcha iye. Anati, “Two amene ali mu mapiri. . . Iwo amene ali pa tsindwi la nyumba, asabwere pansu kudzatenga zinthu mnyumba, kapena iye yemwe ali mmunda kubwerera mmbuyo. Pakuti kudzakhala nthawi ya vuto!” Inu mukuwona? Ndipo zinthu zonse izi zikanadzachitika, tinazisuntha izo mpaka mmusi tsopano ndi kuzitsimikizira izo, kubwerera ku kutsegula kwa Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi ichi.

189 Tsopano ine ndikufuna inu muzindikire. Yesu. . . Tsopano, za mawa usiku, pa Ichi, Yesu anadumpha kuphunzitsa kwa Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri. Icho sichiri apa. Yang'anani, Iye akupitirira ndi mafanizo tsopano, zitatha izo. Ndipo Yohane anadumpha Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri. Chachisanu ndi chiwiri, chotsiriza, Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri, icho chikhala chinthu chachikulu. Icho sichinalembedwe nkomwe, mwawona. Anadumpha Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri; onse a iwo anatero. Ndipo mvumbulutsi, pamene Mulungu anangoti apo panali. . . Yohane anati, “Kunangokhala chete Kumwamba.” Yesu sananene liwu za Icho.

190 Zindikirani tsopano, kubwerera ku ndime ya 12, zindikirani, palibe Chamoyo. Ndiyo ndime ya 12, kuyambira pa Chisindikizo chathu, kuti tichiwone icho chitatsegulidwa. Palibe Chamoyo, chonga, Zolengedwa zamoyo, zikuyimiridwa apa, ngakhale, monga zinaliri pa Chisindikizo Chachisanu. Chifukwa? Izi zinachitika, mbali yina ya m'badwo wa Uthenga, mu nthawi ya Chisawutso. Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi ichi chiri nthawi ya Chisawutso. Ndicho chimene chikuchitika. Mkwatibwi wapita. Mwawona? Apo palibe Chamoyo kapena chinthu pamenepo kuti chinene izo. Pali chabe. . . Tsopano,

Mulungu sakuchitanso nawo Mpingo konse; Iwo wakhala utapita.

¹⁹¹ Iye akuchita naye Israeli, mwawona. Mwawona, iyi ili mbali yina, apa ndi pamene Israeli analandira Uthenga wa ufumu, mwa aneneri awiri a Chivumbulutso 11. Kumbukirani, Israeli ali fuko, antchito a Mulungu, fuko. Ndipo pamene—pamene—pamene Israeli wabweretsedwa mkati, icho chidzakhala—chochitika chafuko.

¹⁹² Israeli, m’badwo wa ufumu, ndiko kumene Davide... Mwana wa Davide, akukhala pa mpandowachifumu. Ndicho chifukwa chake mkazi uja analira, “Inu Mwana wa Davide!” Ndipo Davide ali kwa... Mwana wa Davide! Mulungu analumbira pa Iye, kwa Davide, kuti Iye adzawutsa Mwana Wake yemwe ati adzatenge mpandowachifumu wake. Iwo udzakhala mpandowachifumu wa nthawi za nthawi. Mukuwona? Iwo sudzakhala nawo mapeto. Solomoni anawupereka iwo, mwa choyimira, mu kachisi. Ndipo Yesu anangowawuza iwo apa, ndicho, “Apo sipadzakhala mwala wotsalira pa umodzi wa iyo.” Koma Iye akuyesera kuwawuza iwo apa, chimene... Iye akubwereranso.

“Mudzabwera liti Inu?”

¹⁹³ “Zinthu izi zidzachitika Ine ndisanabwerere.” Ndipo apa izo ziri!

Tsopano ife tiri pa nthawi ya Chisawutso.

Kumbukirani, pamene ufumu wakhazikitsidwa, pa dziko lapansi... .

¹⁹⁴ Tsopano, ichi chikhoza kukhala chogwedeza pang’ono. Ndipo ngati pali funso, ndipo inu—inu mukhoza kundifunsabe ine; ngati inu mukufuna kupereka funsolo, ilo litayitanidwa kale, ndipo kungoligunda ilo; ngati inu simukuchidziwa, inu simukudziwa kale icho.

¹⁹⁵ Mu nthawi ya Zakachikwi, ndi Israeli amene ali fuko, mafuko khumi ndi awiri monga fuko.

¹⁹⁶ Koma Mkwatibwi ali mu nyumba yachifumu. Iye ali Mfumukazi tsopano. Iye wakwatiwa. Ndipo onse a dziko lapansi adzabwera mu mzinda uwu, Yerusalemu, ndipo adzabweretsa ulemerero wa iwo mmenemo. “Ndipo zipata sizidzatsekedwa, u—u—usiku, chifukwa uko sikudzakhala konse usiku.” Mukuwona? Zipata zidzakhala nthawizonse zotsegula. “Ndipo mafumu a dziko lapansi,” Chivumbulutso... 22, “adzabweretsa ulemu wawo ndi ulemerero mu mzinda uwu.” Koma Mkwatibwi ali mmenemo ndi Mwanawankhosa. O, mai! Inu mukhoza kuwona zimenezo, mmenemo! Osati... Mkwatibwi sadzakhala ali kunja kuno akugwira ntchito mminda ya mpesa. Ayi, bwana. Iye ali Mkwatibwi. Iye ali Mfumukazi kwa Mfumu. Ndi enawo amene

akugwira ntchito kunjako, fuko, osati Mkwatibwi. Amen. Chabwino.

197 Zindikirani atumiki awa tsopano, atumiki awa a Chivumbulutso...:12, aneneri awiri awa, iwo akalalikirira, “Ufumu wayandikirira!” Mukuwona? Ufumu wa Kumwamba uli woti ukhazikitsidwe. Nthawi, zaka zitatu ndi theka zotsiriza za sabata la makumi asanu ndi awiri la Daniele, olonjezedwa kwa Ayuda, anthu Ake. Kumbukirani tsopano, icho, kuti zitsimikizire izo, kuti ili liri gawo lotsiriza la sabata la makumi asanu ndi awiri la Daniele. Ine ndiri nalo funso pa izo la mawa. Mukuwona?

198 Tsopano, masabata makumi asanu ndi awiri analonjezedwa, zimene zinali zaka zisanu ndi ziwiri. Ndipo mkati mwa masabata asanu ndi awiri, Mesiya anali woti adzadulidwa, kuti akapangidwe nsembe. Iye akanadzanenera zaka zitatu ndi theka, ndiyeno iye adzadulidwa, kwa nsembe ya anthu. Ndipo apo pakadali motsimizika, kuti zaka zitatu ndi theka nzotsimikizika kwa Israeli. Ndiye, pamene Mesiya anadulidwa, Myuda anachititsidwa khungu kotero iye sanakhoze kuwona uyo anali Mesiya.

199 Ndipo, ndiye, pamene Mesiya anadulidwa, ndiye Uthenga ndi m’badwo wa chisomo zinabwera kwa Amitundu. Ndipo iwo anabwera mmusi, ndipo Mulungu anakokera mmodzi kuchokera *apa* ndi *apo*, ndi *apa* ndi *apo*, ndi kuwayika iwo kumbali pansu pa atumiki; ndipo *apa* ndi *apo*, ndi *apa* ndi *apo*, ndi kuwayika iwo kumbali pansu pa azitumiki.

200 Ndipo Iye anatumiza mtumiki woyamba, ndipo iye analalikirira, ndipo lipenga linawomba; monga ife titi titengere izo, pakapita kanthawi. Ndipo, ndiye, lipenga linali kufotokoza nkondo. Lipenga nthawizonse limanena za nkondo. Mtumiki, mngelo, anabwera pa dziko lapansi, mtumiki wa ora, monga Lutera, monga aliyense wa atumiki omwe ife tinawakamba. Iye akuchita chiyani? Iye akufika; ndipo Chisindikizo chikutsegulidwa, kuwululidwa; lipenga likuwomba, nkondo ikulengezedwa, ndipo kutali iwo akupita. Ndiyeno mtumiki akufa. Iye akusindikizika kulichotsa gulu ili; Iwo ayikidwa mkati. Ndipo mliri ukugwa pa iwo amene anakana Icho. Mukuwona?

201 Ndiye zikupitirira, ndiye iwo akuchita bungwe, kutenga bungwe lina. Ife tangopyola kumene zimenezo. Ndiye, apa iwo akutuluka ndi mphanvu yina, mwawona, mphanvu yina, m’badwo wina wa mpingo, utumiki wina. Ndiye, pamene iye akuchita icho, motsatira akubwera Mulungu ndi utumiki Wake, pamene wotsatsakhristu akubwera nawo wake. Mukuwona, *anti* ndi “kutsutsa.” Iwo amayenda mbali ndi mbali.

202 Ine ndikufuna inu kuti muzindikire chinachake chaching’ono. Itangokwana pafupi nthawi yomwe—yomwe

Kaini akubwera pa dziko lapansi, Abele anabwera pa dziko lapansi. Ine ndikufuna inu muzindikire, itangokwana pafupi nthawi yomwe—yomwe Khristu anabwera pa dziko lapansi, Yudasi anabwera pa dziko lapansi. Pafupi nthawi imene Khristu anachoka pa dziko lapansi, Yudasi anachoka pa dziko lapansi. Itangokwana pafupi nthawi yomwe—Mzimu Woyera unagwa, mzimu wotsutsakhristu unagwa. Itangokwana pafupi nthawi yomwe Mzimu Woyera ukudziwulula Wokha apa mu masiku otsiriza, wotsutsakhristu akuwonetsa manga ake, akubwera kupyolera mu ndale zake ndi zinthu. Ndipo itangokwana pafupi nthawi yomwe wotsutsakhristu akudzisunthira yekha kwathunthu pa mse-. . . powonekera; Mulungu akudzisunthira Yekha kwathunthu pamenepo, kuti awombole izo zonse. Mukuwona, kungoyenda, kungoyenda pamodzi. Ndipo izo ziri, zonse, mbali kwa mbali. Kaini ndi Abale! [M'bale Branham awombetsa manja ake pamodzi kamodzi—Mkonzi.] Khwangwala ndi nkhunda, pa chombo! Yudasi ndi Yesu! Ndipo basi mpaka mmusi, inu mukhoza kutenga izo. . .

203 Apa panali Moabu ndi Israeli; onse awiri awo. Moabu sanali fuko losapembedza. Ayi, bwana. Iwo anapereka nsembe yomweyo yomwe Israeli anali kupereka. Iwo ankapemphera kwa Mulungu yemweyo. Chimodzimodzi. Moabu anali kutcha-. . . Anali mmodzi wa ana a Loti yemwe anagona ndi abambo ake, ndipo anali ndi mwana. Ndipo mwana ameneyo anatchedwa Moabu. Ndipo kuchokera mwa iye munatuluka mtundu wa Moabu, dziko la Moabu.

Ndipo pamene iwo anawona Israeli, m'bale wawo wowomboledwa, akubwera.

204 Iwo anali achikhazikitso. Iwo anali chipembedzo chachikulu. Israeli analibe chipembedzo; iye ankangokhala mmahema ndi kulikonse inu muti mupite. Koma Moabu anali nawo awudindo, mafumu, ndi zina zotero. Ndipo iwo anali naye Balaamu kumeneko, m—mneneri wabodza. Ndipo iwo anali nazo zonse izi. Ndiye iwo anabwera kumusi uko kudzatemberera m'bale wawo wamng'ono yemwe anali pa ulendo wopita ku dziko lolonjezedwa, kupita ku lonjezo lake.

205 Ndipo iye anapita ndi kukawafunsa iwo, “Kodi ine ndingadutse dziko lanu? Ngati ng'ombe zanga zimwa madzi, ine ndidzalipira icho. Ngati izo zinyambite udzu, ife tidzalipirira izo.”

206 Iye anati, “Ayi. Iwe sukhala nacho chitsitsimutso monga chotero kozungulira kuno. Uko nkulondola. Iwe sukhala nacho chirichonse ngati icho kozungulira kuno.”

207 Ndiyeno yang'anani chimene iye anachita. Iye anabwerera kumene mmbuyo mu mawonekedwe a Yezebeli, ndi kubwera pansu kupyolera mwa mneneri wabodza uyo, ndi kupangitsa ana

a Mulungu kulakwa. Ndi kukwatira akazi Achimoabu kulowa—kulowa mu Israeli, ndi kupangitsa chigololo.

208 Ndipo iye anachita chinthu chomwecho, mu m’badwo womwewo, pa ulendo, pa msewu wa ku Dziko lolonjezedwa, ife tirimo. Iye anachita chiyani? Mneneri wabodza anabwera pomwepo ndi kukwatira, ndipo anayitanira mu mpingo wa Protesifanti, ndi kupangitsa zipembedzo, chimodzimidzi basi zomwe iwo anachita mmbuyo uko. [M’bale Branham agogoda pa guwa kanai—Mkonzi.]

209 Koma Israeli wamng’ono wakale anasuntha patsogolobe, chomwecho. Iye anazungulira mu chipululu kwa nthawi yaitali, ndipo onse iwo omenyera akale aja anayenera kufa, koma iye anapitirirabe mpaka ku dziko lolonjezedwa. Eya. Inde. Yang’anani iwo onse akugwirana mikono, chabe iwo asanawoloke Yorodani. A-ha! Ine ndikuzikonda zimenezo. Tsopano ife tikufika ku m’badwo umenewo pakali pano, apa tsopano. Zindikirani.

210 Taonani ife tikupeza kuti, nthawi, yotsiriza (ine ndinati) zaka zitatu ndi theka za masabata makumi asanu ndi awiri a Daniele.

211 Ndiroleni ine ndifotokoze zimenezo mwatcheru pang’ono tsopano, chifukwa ine ndikuwona winawake apa yemwe nthawizonse wakhala akuyang’anira icho, ndipo ine—ine ndikufuna kuyesera kuzipanga ndekha kumveka; mphunzitsi.

212 Zindikirani pamene masabata makumi asanu ndi awiri akubwera mkati. Pamene Daniele anawona masomphenya a nthawi ikubwera, ndi kutsiriza kwa Ayuda, koma iye anati apo panatsimikizika masabata makumi asanu ndi awiri. Ndizo zaka zisanu ndi ziwiri; mkati mwa izo, bwanji, Mesiya akanadzakhala kuno, kapena, ndipo akanadzadulidwa, chifukwa cha nsembe. Tsopano, ndicho chimodzimidzi chimene chinachitika.

213 Ndiye, Mulungu anachita nawo Amitundu mpaka iwo atachotsamo anthu kwa Dzina Lake. Ndipo mwansanga pamene Mpingo wa Amitundu watulutsidwamo, Iye akuwutengera mmwamba Mpingo.

214 Ndipo pamene Iye anatero, namwali wogona, mpingo iwowokha...Mkwatibwi anapita mmwamba. Ndipo mpingo iwowokha unaponyedwa ku “mdima wakunja, kumene kuli kulira, ndi kuisima, ndi kukukuta kwa mano.” Mu nthawi yomweyo, Chisawutso chikugwa pa anthu amenewo.

215 Ndipo pamene Chisawutso chikugwa, mmenemo mukubwera aneneri awiri awa a Chivumbulutso 11, kukalalikira Uthenga kwa iwo. Ndipo iwo akulalikira masiku chikwi, zana limodzi . . . ndi makumi awiri atatu. Mwawona? Chabwino, ndizo chimodzimidzi, ndi masiku makumi atatu mu mwezi monga mmene kalendala weniweni ali nawo, ziri kwenikweni zaka zitatu ndi theka. Ndilo gawo la makumi asanu ndi awiri la

Daniele, gawo lotsiriza la sabata la makumi asanu ndi awiri. Mukuwona?

Mulungu sakuchita ndi Israeli mkati umu. Ayi, bwana.

216 M'bale anandifunsa ine, osati kale litali, anati, “Kodi ine ndipite ku. . .” M—m'bale apa mu mpingo, m'bale wokoma, m'bale wokonedwa, anati, “Ine—ine ndikufuna kupita ku Israeli. Ine ndikukhulupirira uko kuli kuwuka.”

217 Winawake ananena kwa ine, “M'bale Branham, inu muyenera kupita ku Israeli pakali pano. Iwo akachiwona icho.” Mukuwona, inu simungakhoze kuchita izo.

Ine ndinayima pomwepo, ndipo ine ndinaganiza. . .

218 Ayuda amenewo anati, “Ngati ine. . . Chabwino, ngati uyu ali, Yesu kukhala—kukhala Mesiya,” anati, “mundirole ine ndimuwone Iye akuchita chizindikiro cha mneneri. Ife tidzakhulupirira aneneri athu, chifukwa ndicho chomwe iwo ali—iwo akuyenera kukhala.”

219 “Ndi dongosolo lotani,” ine ndinaganiza. “Apa ine ndikupita!” Pamene ine ndinafika kumeneko, nditayandikira kumene ndi iko, kumene. . . ine ndinali, chabwino, ine ndinali ku Cairo. Ndipo ine ndinali nayo tikiti yanga mu dzanja langa, yopita ku Israeli. Ndipo ine ndinati, “Ine, ine ndipita, ndikawone ngati iwo akafunse icho, ngati iwo angakhoze kuwona chizindikiro cha mneneri. Ife tidzawona ngati iwo ati adzambulandire Khristu.”

220 Lewi Pethrus, wa mpingo wa ku Stockholm, anawatumizira iwo ma Baibulo milioni.

221 Ndipo Ayuda amene akubwera mmenemo awo! Inu mwachiwona chithunzi. Ine ndiri nacho icho pa filimu, kumbuyo komwe uko tsopano, *Maminiti Atatu Isanakwane Pakati pa usiku*. Ndipo Ayuda amenewo akubwera mmenemo, kuchokera konse konse mu dziko, kulikonse, kuyamba kusonkhana mmenemo kumeneko.

222 England atapita kale kumeneko, mu nthawi ya General Allenby. Mu *Kutha Kwa Nkhondo Yadziko Lonse*, mu bukhu lalikulu lachiwiri, ine ndikuganiza ilo liri. Ndipo iwo anagonja, Atarki anagonja. Ndiye iye analibwezera ilo kwa Israeli. Ndipo iye wakhala akukula monga fuko, ndipo tsopano iye ali fuko langwiro: ndalama zakezake, zamapepala, mbendera, ankhondo, ndi china chirichonse. Mukuwona?

223 Ndipo Ayuda amenewa, akubwereranso ku dziko la kwawo, iwo anali. . . Chinthu choyamba, pamene iwo anapita mpaka mu Iran, ndi kumusi kumeneko, kukawatenga iwo, iwo anafunsa. . . Iwo anati iye. . . Iwo akufuna kuwatengera iwo kuti abwerere ku Israeli, kukawapatsa iwo malo awo; kuwatengera iwo kubwerera mu dziko lawo, Palesitina, kumene iwo akuyenera kukhala ali.

224 Ndipo, kumbukirani, malingana ngati Israeli ali kunja kwa dziko limenelo, iye ali kunja kwa chifuniro cha Mulungu; monga Abrahamu, kwa yemwe ilo linapatsidwa. Ndipo pamene. . .

225 Iwo sakanakwera mu ndege imeneyo. Iwo anali asanawonepo chirichonse monga icho. Apo panali mphunzitsi wachikulire anabwera pamenepo, anati, “Mneneri wathu anatiwuzwa ife, kuti, pamene Israeli azidzapita kwawo, izo zikanadzakhala ‘pa mapiko a mphungu,’” pa ndege, kupita kwawo.

226 Apo iye ali tsopano, akumanga. Mtengo wa mkuyu ukubwezeretsa! Ameni! Mbendera yakale ya nyenyezi ya nsonga zisanu ndi imodzi ya Davide ikuwuluka!

227 “Masiku a Amitundu akwanira, zovuta zikuchuluka!” Nthawi ya Chisawutso yayandikira kumene!

228 Ndipo kuyimirira pomwe pano, ndipo Zisindikizo zikutsegulidwa, Mpingo wakonzekera kuti utenge kuwuluka Kwake kumka mumlengalenga!

229 Ndipo Chisawutso kulowamo, ndiye Mulungu akubwera pansu ndi kusolola zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi kuchokera mmenemo. Ameni! Apo, o, ndi zangwiro! Inu mukuwona pamene Zisindikizo zikutulutsa izo tsopano, mwawona, kutsegula izo? Tsopano, izi ndi zaka zitatu ndi theka zotsiriza kwa anthu. Ndiponso, ngati inu mungazindikire, ndi nthawi yomwe Mulungu ati adzayitane Ayuda zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi, mu zaka zitatu ndi theka zotsiriza izi.

230 Mukuwona, Iye sakuchitanso nawo iwo, nkomwe. Iwo analibe mneneri. Iwo sadzakhulupirira kanthu kalikonse koma mneneri. Inu simungawapusitse iwo. Kotero, iwo adzamva mneneri, inde, bwana, ndipo ndicho zonse. Kutu, Mulungu anawawuza iwo izo pachiyambi, ndipo akukhala nachobe icho.

231 Iye anati, “Ambuye Mulungu wanu adzawukitsa Mneneri pakati pa inu, wonga ine.” Mose ananena zimenezo. Ndipo anati, “Iye inu mudzamumvere. Ndipo yense yemwe sadzamumvera Mneneri ameneyo, adzadulidwa kuchoka kwa anthu.” Uko nkulondola.

232 Ndipo, inu mukuwona, maso awo anachita kuchititsidwa khungu, kapena iwo akanadzamuzindikira Iye. Mmallo mwa icho, pochititsidwa khungu, iwo anali. . .Icho chinamulola Satana kufika pa iwo, ndipo iwo akuti, “Iye ndi wambwebwe, Bezezebule. Magazi Ake akhale pa ife. Iye tikudziwa palibepo kanthu za Iye.” Mwawona?

233 Ndipo anthu osawuka anachititsidwa khungu. Ndicho chifukwa chake gulu la Eichmann ndi gulu lonse ilo anaphedwa mmbuyo umo. Analinawo mwayi wobwera mkati; Atate awo

omwe anachita kuwachititsa khungu maso awo kotero Iye akanakhoza kutitenga ife.

²³⁴ Ndicho chinthu chomvetsa chisoni kwambiri mu Malemba, pafupifupi. Ingoganiza za kumeneko, Ayuda, kuyitana Magazi a Atate awo omwe, Mulungu wawo yemwe atapachikidwa pamenepo, akuwukha magazi. Penyani, “Kumeneko iwo anampachika Iye,” Baibulo linatero. Ndiwo anai a mawu akulu kwambiri. Penyani. “Kumeneko,” Yerusalemu, mzinda woyera kwambiri mu dziko. “Iwo,” anthu oyera kwambiri mu dziko. “Anampachika,” imfa yoyipa zedi mu dziko. “Iye,” Munthu wofunikira kwambiri mu dziko. Mukuwona? Chifukwa? Anthu achipembedzo, chipembedzo chachikulu kwambiri mu dziko, chipembedzo chowona chokhacho mu dziko, chinali kuyima pamenepo, kupachika Mulungu yemwe amene Baibulo lawo linati akanabwera.

²³⁵ Chifukwa chiyani iwo sanachiwone icho? Baibulo limatiwuzwa ife kuti Mulungu anawachititsa khungu iwo kotero iwo sakanakhoza kuwona icho. Iwo. . . Iye anati, “Ndani mmodzi wa inu angakhoze kunditsutsa Ine za tchimo?” Mwa kulankhula kwina, “Ngati ine ndikanapanda kuchita chimodzimodzi chimene chanenedweratu kwa Ine kuti ndichite, ndiye inu mundiwuzwa Ine.” *Tchimo* ndi “kusakhulupirira.” Iye anachita chimodzimodzi chimene Mulungu anamuwuzwa Iye, koma iwo sakanakhoza kuchiwona icho.

²³⁶ Tsopano pamene iwe ulankhula kwa anthu, ziri monga ngati kuponyera madzi pa nsana wa bakha. Kodi inu mukuwona chimene ine ndikutanthawuza? Icho ndi chinthu chomvetsa chisoni, pamene iwe uwona mafuko awa ndi anthu, momwe iwo achitira, okhuthala kwambiri ndi chipembedzo! Koma kodi Mzimu Woyera sumatiwuzwa ife izo? “Iwo adzakhala a mmutu, otukumuka-mtima, okonda zokondweretsa anthu kuposa kokonda Mulungu, osayanjanitsika, otsutsa mwabodza, osadzigwira, ndi onyoza iwo amene ali abwino. Iwo adzakhala nawo mawonekedwe achipembedzo, koma adzakana Mphamvu ya Uthenga.” Anati, “Kwa otere, patuka kwa iwo.”

²³⁷ Apa ife tiri, zipembedzo izi zikupotola Icho. Iwo akutenga ulemerero wonse ndi Mphamvu, kuziyika Izo mmbuyo ndi atumwi, ndipo zina zonse Izo mu Zakachikwi. Izo ziri monga ngati munthu, monga ine ndinanena kale; munthu nthawizonse akupereka mayamiko kwa Mulungu pa zomwe Iye wachita, kuyang’ana mtsogolo ku zomwe Iye ati adzachite, ndi kunyalanyaza zomwe Iye akuchita pakali pano. Ndicho chimodzimodzi. Munthu akadali chinthu chomwecho.

²³⁸ Panali Ayuda amenewo atayimirira pamenepo, akunena, “Ulemerero kwa Mulungu! Bwanji,” pa mutu wa 6 wa Yohane Woyera, anati, “Makolo athu ankadya mana mchipululu!”

Ndipo Yesu anati, “Iwo ali, aliyense, wakufa.”

239 “Iwo anamwa madzi kuchokera pa Thanthwe mu chipululu, ndi chirichonse.”

240 Iye anati, “Ine ndine Thanthwe limenelo.” Uko nkulondola. Amen. Iye anati, “Koma ine ndine Mkate wa Moyo umene ukuchokera kwa Mulungu Kumwamba, Mtengo wa Moyo uwo kuchokera ku Edeni kutsidya uko. Ngati munthu adya Mkate uwu, iye sadzafa; Ine ndidzamuwutsa iye kachiwiri mmasiku otsiriza.” Ndipo iwo sanakhozebe kuchiwona icho! Uko nkulondola.

241 Mesiya yemwe kuyimirira pamenepo, akulankhula mawu omwewo a za mu mtima wawo, ndi zinthu monga choncho, kusonyeza kuti Iye anali Mesiya, basi chimene Mesiya anayenera kuchita!

242 Ndipo iwo atayimirira pamenepo ndi manja kumbuyo kwawo, ndipo, “Ha! Sizingakhale. Ayi, ayi. Iye—Iye—Iye sanabwere mu njira yoyenera. Mukuwona, Iye anachokera ku Betelehemu. Ndipo Iye—Iye sali kanthu koma mwana wapathengo. Ndipo ndiye Mdierekezi akugwira ntchito pa Iye. Ife—ife tikudziwa Iye ndi wamisala. Iye ndi wopenga. Iye ali naye mdierekezi.” Mukuwona? Maso awo anachititsidwa kwenikweni kwa icho, tsopano.

243 Koma iwo akuyembekezera mneneri wawo. Ndipo iwo alandira icho, alandira awiri a iwo. Uko nkulondola.

244 Tsopano zindikirani, kachiwiri, tsopano, ndiponso, pamene Ayuda awa... Ine ndikupatsani inu chophiphiritsa chaching’ono, koteri inu mukhoza kuzindikira kuti ali Ayuda cha apa tsopano, pa mbali iyi ya Mkwatulo. Yang’anani chimene chikuchitika. Icho chikuphiphiritsidwanso... Ife sititenga nthawi kuti tichite icho, chifukwa ife tikuthamanga—yatithera apa. Zikuphiphiritsidwanso mu... mu chomwe chikutchedwa “vuto la Yakobo.” Tsopano penyani. Ayuda awa apa ali... Zindikirani. O, chiri... .

245 Ine—ine—ine ndingotenga nthawi pang’ono pokha apa, mwawona. Zimandipangitsa ine manjenje pamene ine ndiyamba kudumpha chozungulira monga choncho. Ndipo... Mukuwona? Zindikirani. Ine ndikufuna inu muwone icho. Ndipo ine—ine—ine basi... Chabwino, Mulungu awonetsa icho kwa inu, ndiri wotsimikiza. Penyani.

246 Yakobo anali nawo ufulu wa kubadwa. Nkulondola uko? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Koma iye ndithudi anali shyashya pang’ono nawo iwo. Mwawona? Iye anapita uko ndipo iye anawanyenga abambo ake. Iye anamunyenga mchimwene wake. Iye anachita chirichonse. Koma, apobe, mwalamulo, mpaka mmusi, iye anali nawo iwo, chifukwa Esau anali atawugulitsa iwo. Koma ndiye pamene iye akupita kumeneko kukawagwirira ntchito apongozi ake amuna, iye anayika mitengo ya popula iyo mmadzi, kuzipanga ng’ombe zabelezo

ndi zina kubala ana amanga-manga. Ndipo, o, inu mukudziwa chirichonse chimene iye anachita monga choncho, basi ku—kuti apeze ndalama. Tsopano yang'anani, tsopano. Iye anachotsedwa kwa anthu ake.

²⁴⁷ Tsopano, chiri choyimira cha Myuda tsopano. Iye ali wolanda-ndalama. Ine sindikusamala momwe iye ati apezere izo, iye azipeza izo. Iye adzakusenda iwe wamoyo, kuti apeze izo. Tsopano, inu mukudziwa izo. Iye ndi shyashya pang'ono, ndizo zonse. Mnyamata, usamachite naye iye; iye—iye adzakutenga iwe, mnyamata. Inde, bwana. Chifukwa? Iye ayenera kukhala chimenecho. Ndiwo mtundu wa mzimu umene ukulamulira.

²⁴⁸ Chimodzimodzi basi monga okonzanso awo, sankakhoza kumvetsa Mawu awa, chifukwa umenewo unali mzimu wa munthu wotumidwa kwa iwo.

²⁴⁹ Ndi m'badwo wa mphungu umene ukutenga Mawu ndi vumbulutso. Onse amene akumvetsa izo, kwezani manja anu, kotero ine... Izo nzabwino. Izo nzabwino. Mukuwona? Izo nzabwino. Tsopano, mwawona, ngati inu mungabwerere apa pansu pa Zisindikizo izi, ngati Izo konse zinafikapo... Pamene Izo zatsegulidwa, inu mukukhoza kuwona chimodzimodzi chimene Mulungu akuchita, chimene Iye wachita, chimene Iye ati achite. Apa izo ziri, chimodzimodzi.

²⁵⁰ Ndipo ndicho chifukwa chake anthu ankachita mwanjira iyo, chifukwa ndiwo mzimu umene wanenedweratu kwa m'badwo umenewo, kuti ukakhale pa iwo. Iwo sakanakhoza kuchita kanthu kena kalikonse.

²⁵¹ Ine ndikuganiza za Yohane, Paulo, ndi iwo, Mzimu wa mkango uwo kumeneko, m-k-a-n-g-o kuyimirira pamene, Mawu Iwoomwe.

²⁵² Paulo anayima nawo kumene Mawu amenewo, ndipo anati, "Ine ndikudziwa ichi, kuti padzakhala abale abodza adzawuka pakati pa inu, kupita ponseponse. Ndi zomwe iwo ati adzapange, zipembedzo ndi china chirichonse, pakati pa inu, ndi zomwe ati adzachite. Ndipo izo zidzapitirira mpaka ku masiku otsiriza, ndi nthawi zowopsya." Chifukwa? Iye anali mneneri. Apo panayima Mawu amenewo mwa iye. Momwe izo ziti zikanatsirizikira, kutali cha kumeneko; Anati, "Anthu abodza pakati pa inu adzawuka, ndi kulankhula zinthu, ndi kukopera kwina abale amene ali ophunzira." Ndicho chimodzimodzi wotsutsakhristu. Icho basi chinachita chimodzimodzi zimenezo.

²⁵³ Zindikirani atatha iwo kupita mu m'badwo wa mdima wa chisawutso. Chinali chiyani icho? Panalibe kanthu kamene iwo akanakhoza kuchita. Roma anali mwini wa... Iye anali nayo mphamvu ya chipembedzo, ndipo iye anali nayo mphamvu ya ndale. Panalibe kanthu komwe iwo akanachita, koma kungovutikira kuti akhale amoyo, ndi kudzipereka okha mwa nsembe. Iyo inali ng'ombe. Ndicho chonse iwo akanakhoza

kuchita. Ndiwo mtundu wa Mzimu womwe iwo anali nawo, Mzimu wa Mulungu, ng'ombe.

²⁵⁴ Ndiye, apa pakubwera okonzanso, mutu wa munthu, wothyathalika, wanzeru; Marteni Lutera, Joni Wesile, ndi ena onse, Calvin, Finney, Knox, ndi onse a iwo. Apa iwo akutulukira, ndipo, pamene iwo anatero, iwo anali okonzanso. Iwo amatulukira, akukonzanso, kuwatulutsa anthu kunja.

²⁵⁵ Ndipo anatembenukiranso mmbuyo momwe, chimodzimodzi monga iwo anachitira mmbuyo uko, ndi kukwatiwanso molunjika kumene mmbuyo kwa iye kachiwiri, pa kachitidwe kachipembedzo kawo, chimodzimodzi basi. Baibulo linanena choncho. Iye anali “hule,” ndiyeno iye anali nato “timahule,” ana aakazi, chimodzimodzi basi.

²⁵⁶ Ndipo Mulungu anati, “Ine—Ine ndinampatsa iye danga kuti alape, ndipo iye sanachite izo. Kotero ine ndimutenga iye ndi ana ake, kuwaponyera iwo cha kumeneko kumene iwo akuyenera.” Ndicho chimodzimodzi. Tsopano, kuti, Mulungu ananena icho, pansu pa ichi, mwawona, pansu pa Chisindikizo. Tsopano, apo iye anali. Iye tikupeza kuti Iye akuchita zimenezo, ndipo Iye adzachita izo. Ndipo iwo ali, mmodzi aliyense, walunjika njira imeneyo.

²⁵⁷ Koma, kwa onse amene ali nawo maina awo pa Bukhu la Moyo, Mulungu adzawayitana. Iwo adzalimva Ilo. “Nkhosa Zanga zimamva Liwu Langa,” Yesu anatero. Chinthu chokhacho ife tiyenera kuchita ndicho kupanga kuyitana kwa nkhusa. Mbuzi sizimadziwa Iko. Zindikirani. Koma, inu mukuwona, kuyitana kwa nkhusa, “Nkhosa Zanga zimamva Liwu Langa.” Chifukwa? Liwulo liri chiyani? Ine ndikufuna ndikuwuzeni inu chomwe Liwu liri. Liwu liri—liri chizindikiro chauzimu.

²⁵⁸ Iye ananena kwa Mose, “Ngati iwo sakamva Liwu la chizindikiro choyamba, iwo akamva Liwu la chizindikiro chachiwiri.”

²⁵⁹ “Nkhosa Zanga zimamva Liwu Langa.” Pamene zinthu izi zikuyenera kumachitika mu masiku otsiriza, nkhusa za Mulungu zikulizindikira Ilo. Inde, bwana. Mukuwona? Izo—izo zikulizindikira Ilo. “Nkhosa Zanga zikundidziwa Ine.” Mukuwona? “Mlendo izo sizingamutsate.” Osamasata alendo awo. Chiyenera kukhala chizindikiro chotsimikiziridwa cha tsiku, ndipo izo zimawona Icho. Tsopano, tsopano zindikirani.

²⁶⁰ Tsopano, Yakobo, pamene iye anafika tsopano, chinthu choyamba inu mukudziwa, iye anakhala nacho chikhumbo chopita (kuti?) kubwerera ku dziko la kwawo.

²⁶¹ O, ndicho chimodzimodzi chimene Israeli wachita! Ndicho—ndicho... Ameneyo ndi Israeli. Yakobo ali Israeli. Iye anangosinthidwa dzina lake, inu mukudziwa. Mukuwona? Ndipo iye ali... .

262 Iye anafika kumeneko, ndipo iye anatenga ndalama zonse zomwe iye anali nazo, ndipo iye akanakhoza kupeza, ndipo anatenga izo mwanjira iliyonse iye akanakhoza, kuchokera kwa abale ake kapena wina aliyense. Chotero, kuchita bodza, kuba, kunama, njira iliyonse yomwe iye akanakhoza kutengera izo, iye anatenga izo. Mwawona? Iye anatero.

263 Ndiyeno pamene iye akuyamba kubwerera kwawo, iye anayamba kumverera kupukwa kufuna kwawo mu mtima mwake. Koma pamene iye anayamba kubwerera, pa ulendo wake wobwerera, iye anakomana naye Mulungu, ndiye dzina lake linasinthidwa. Mukuwona? Koma, mu nthawi iyi, iye anatopetsedwa kwambiri, chifukwa iye ankachita mantha kuti Esau anali kumulondola iye. Mukuwona?

264 Ndipo—ndipo yang’anani, yang’anani ndalama, nkhani ya ndalama. Basi monga Myuda adzayesa kupanga pangano ili ndi—ndi Roma, mwawona, mu nkhani yawo ya ndalama. Zindikirani icho. Kuti Esau sanafune ndalama zake; ngakhalenso Roma. Iye ali nacho chuma cha mdziko mu dzanja lake. Mwawona? Koma izo sizinagwire ntchito.

265 Koma ife tikupeza tsopano, kuti Israeli, mu nthawi iyo ya vuto, pamene iye anali Yakobo, iye analimbana naye. . . .kuti anagwira Chinachake chimene chinali chenicheni. Apo panali Munthu akubwera mmusi. Yakobo anakulunga manja ake pa Iye, ndipo iye anakhala pomwepo. Ndipo—ndipo m—Munthuyo anati, “Ine ndiyenera kumapita tsopano. Kukuyamba kucha.” O, kutuluka-kwa-tsiku uko! Mukuwona? Kumakonzekera kubwera kwa tsiku.”

266 Koma Yakobo anati, “Ine—ine sindikusiyani Inu. Inu, Inu simungapite. Ine ndikhala nanu basi Inu.” Mukuwona? “Ine ndikufuna zinthu zisinthe pano.”

267 Ndiwo zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi, gulu lolanda ndalama ilo, ndi zinthu monga choncho, pamene iwo awona chowona, chinthu chenicheni choti achigwire. Apo payima Mose, ndipo apo payima Eliya. Amen! Iwo adzalimbana naye Mulungu mpaka zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi a mafuko a Israeli atayitanidwa kuti atuluke pomwe apo.

268 Ndiyo chabe isanafike nthawi ya Chisawutso, mwawona, (o nzodabwitsa chotani) aponso, “Vuto la Yakobo.”

269 Apa pali pamene zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi akuyitanidwa kuti atuluke. Iwo, a—alaliki, aneneri awiri awo, iwo akulalikira monga Yohane Mbatizi. “Ufumu wa Kumwamba wayandikira. Lapani, Israeli!” Alape chiyani? “Lapani muchoke ku machimo anu, kusakhulupirira kwanu, ndipo mubwerenso kwa Mulungu!”

270 Tsopano tiyeni ife tikumbukire chinachake apa. Zochitika zazikulu izi, kwa chirengedwe, zinachitikapo kale. Mu ndime

ya 12 iyi apa, mwawona, “Dzuwa linada bii ngati chiguduli cha ubweya.” Tsopano fanizitsani izi.

²⁷¹ Tsopano, kumbukirani, izo sizikuchitika mwa Amitundu. Ndi Israeli. Ndiroleni ine ndikuwonetseni inu. Tsopano, kumbukirani, ine ndinati ndiko kuyitana kwa zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi. Mukuwona? Nthawi iyi tsopano, ili pamene Chisawutso, chimene chiti chikachite izo. Ndipo izi zikutiwuzza zomwe ziti zichitike mu Chisawutso ichi.

²⁷² Tsopano tiyeni titsegule ku Eksodo 10:21-23. Ndipo yang’anani apa pamene. . . Eksodo ali pamene, zedi, Israeli anali kutuluka, kuti akatulutsidwa. Eksodo, mutu wa 10, ndipo ya 21, ndime ya 23. Ine ndiri wokomedwa kwambiri ndi kufuwula, pamene ine ndikulemba zolembe izi, mwakuti nthawizina ine ndimazisokoneza izo. Chabwino, Eksodo 10:21-23. Chabwino, apa ife tikupita, 21 ndi 23.

Ndipo YEHOVA anati kwa Mose, Tambasulira dzanja lako moloza kumwamba, kuti kukhoze kukhala mdima pa dziko la Igupto, ngakhale mdima umene ukhoza kukhudzika.

Ndipo Mose anatambasulira dzanja lake moloza kumwamba; ndipo apo panabwera mdima wokandapala mu dziko lonse la Igupto masiku atatu: (Mukuwona?)

Tsopano, iwo sanawonane wina ndi mzake, ngakhale kuwuka aliyense kuchokera pa malo ake kwa masiku atatu: koma . . . ana a Israeli anali nako kuwala mokhala mwawo.

²⁷³ Zindikirani, chimodzimidzi basi, tsopano bwerani cha apa, “Ndipo dzuwa linada bii ngati chiguduli.” Mwawona, chinthu chomwecho! Zochitika izi za chirengedwe, chinali chiyani icho? Chiyani? Pamene chirengedwe chichitika monga chonchi, chakhala Mulungu akuyitana Israeli. Mukuwona? Mulungu akuyitana Israeli kuti atuluke. Tsopano, “Dzuwa lakuda ngati. . . ubweya.” Tsopano, Mulungu anali pafupi kuwombola Israeli kumeneko, chabwino, kuwabweretsa iwo kuchokera mdzanja la mdani wawo, yemwe anali Igupto, pa nthawi imeneyo. Tsopano, apa, Iye akuwabweretsa iwo kuchokera mdzanja la Aroma, kumene iwo anali atapanga pangano lawo. Chinthu chomwecho chikuchitika. Ndiyo miliri, n—nthawi yimene miliri iyi iti idzayitane.

²⁷⁴ Idzagwera gulu ili la Amitundu. Ngati ife tikanakhala nayo nthawi, ine ndikanakhoza kuwonetsa chimene chiti chidzachitike kwa mpingo wa Amitundu uwo.

²⁷⁵ Baibulo linanena, kuti, “C—chinjoka, Satana, anakwiwitsidwa (ndiko, kukwiya) naye mkazi (Myuda, Israeli), ndipo iye analavula madzi kuchokera mkamwa mwake, khamu ndi unyinjwa wa anthu, amene anapita kukachita nkondo ndi

otsalira a mbewu ya mkazi.” Chivumbulutso 13. Tsopano, mukuwona pamenepo, ife tiri nazo izo. Ndipo mpamene Israeli akutumiza ake...ine ndikutanthawuza, Roma akutumiza ankhondo ake kutsatira otsalira, otsalira a mbewu ya mkazi.

²⁷⁶ Tsopano yang’anani. Nthawi yoyamba, mmanja a mdani wake, pamene Iye anali kuwawombola iwo kuti atuluke, dzuwa linasanduka chigudu-...lakuda ngati chiguduli. Tsopano, iyi ili nthawi yachiwiri, kutha kwa nthawi ya Chisawutso.

²⁷⁷ Tsopano, mu Daniele 12. Ngati ife tikanakhala nayo nthawi, tikanakhoza kuwerenga izo. Mu Daniele, ya 12—ndime ya 12...mutu wa 12, kani. Daniele anati, “Yense yemwe anapezeka atalembedwa mu Bukhu akanawomboledwa.” Tsopano, kumbukirani, Daniele tsopano akulankhula za nthawi iyi pamene izi...chinthu ichi chiyenera kuchitika, pamene Israeli ali woti awomboledwe, pamene m—mapeto a sabata lawo la makumi asanu ndi awiri. Ndipo pamene iwo akuyenera kuti awomboledwe. Tsopano penyani. Tiyeni ife tipite ku Daniele 12 apa, miniti yokha.

Ndipo pa nthawi imeneyo adzayimirira Mikaeli, kalonga wamkulu yemwe anayimira ana...kwa—kwa ana a anthu ako (mukuwona, ndiwo Ayuda): ndipo kudzakhala...vuto, longa...silinakhalepo kuyambira pamene kunakhala fuko ngakhale mpaka nthawi yomweyo:...

²⁷⁸ Tsopano fanizitsani izo, chimodzimidzi zomwe Yesu ananena, Mateyu 24, “Padzakhala nthawi ya vuto limene silinakhalepo kuyambira pamene kunakhala fuko.” Penyani pa Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi, mwawona, chinthu chomwecho, nthawi ya vuto. Zindikirani.

...kuyambira pamene kunakhala fuko ngakhale mpaka nthawi yomweyo: ndipo pa nthawi imeneyo anthu ako... (Tsopano, mu la makumi asanu ndi awiri ili, gawo lotsiriza la chaka chachisanu ndi chiwiri) ... anthu ako adzawomboledwa, aliynse yemwe ati adzapezeke atalembedwa mu bukhu.

²⁷⁹ Wokonzedweratu, inu mukuwona, amene analembedwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa, adzawomboledwa pa nthawi imeneyo.

Ndipo ambiri a iwo omwe akugona mu fumbi la dziko lapansi adzawuka, ndipo ena kumka ku moyo wosatha, ndi ena ku manyazi osatha ndi mnyozo.

Tsopano, ndiyeno anzeru adzawala ngati kunyezimira kwa thambo; ndi—ndi iwo amene atembenuzira ambiri ku chilungamo adzawala ngati nyenyezi ku nthawi za nthawi.

280 Icho, ndiye anapitiriza, anamuwuzwa Daniele kuti “atseke Bukhulo,” pakuti iye akanakhala akupumula mu malo ake mpaka nthawi imeneyo.

281 Tsopano, mukuwona, sizipanga kusiyana kulikonse kaya iwe ukhala moyo kapena umwalira. Iwe udzatulukira, mulimonse. Mukuwona? Musati. . . .Kuti, kufa, si kanthu kwa Mkristu. Iye samamwalira, mulimonse. Mwawona?

282 Tsopano, Daniele 12, ananena kuti aliyense amene anapezeka atalembedwa mu Bukhu akanadzawomboledwa.

283 Apa, Mulungu ali pafupi kuwombola mwana Wake wachiwiri, Israeli, chitatha Chisawutso. Mukuwona, nthawi yachiwiri, Israeli, Wake. . . .Israeli ndi mwana Wake. Inu mukudziwa zimenezo. Israeli ndi mwana wa Mulungu, kotero Iye akudzamuwombola iye apa mu nthawi ya Chisawutso, chimodzimidzi basi momwe Iye anachitira uko mu Igupto.

284 Tsopano tiyeni tiyimire apa, kachiwiri, ndi—ndi kutenga chinachake, kotero, tisanabweretse izo mpaka pachimake. Tsopano yang’anani apa. Aneneri awiri awa, penyani chimene iwo akukachita tsopano, basi monga Mose ndi iwo anachitira kumeneko. “Ndipo apo anandipatsa ine bango. . . .” Ndipo ndime ya 3 ya mutu wa 11.

Ndipo Ine ndidzapatsa mphamvu kwa mboni zanga ziwiri, kuti izo zidzanenera masiku chikwi chimodzi mazana awiri ndi makumi asanu ndi limodzi, zitavekedwa mu chiguduli.

Izo ndiyo mitengo iwiri ya azitona, . . .

285 Inu mukukumbukira izo, ndipo Zerubabelo, ndi ena otero, anali woti akamangenso kachisi.

. . . ndi zoyikapo nyali ziwiri zomwe zikuyima pamaso pa Mulungu wa dziko lapansi.

. . . ngati munthu aliyense. . . ayipsa iwo, moto ukutuluka kuchokera mkamwa mwawo, . . .

286 Mukukumbukira, kuchokera mkamwa mwa Khristu munatuluka lupanga, Mawu.

. . . kuwononga adani awo: ndipo ngati munthu aliyense adzayipsya iwo, iye ayenera mu chikhalidwe ichi kuphedwa.

287 Tsopano, ife tikudziwa, “moto.” Mu mutu wa 19, wa Kudza kwa Khristu, “munatuluka lupanga Lake kuchokera mkamwa Mwake,” amene anali Mawu. Nkulondola uko? Mawu! O, ngati inu mutamvetse chipangizo ichi tsopano, kwa Chisindikizo icho mawa usiku! Mwawona, Mawu ali chinthu chimene Mulungu amadulira nacho mdani Wake. Mukuwona?

288 Tsopano penyani apa. Pamene aneneri awa akunenera kumeneko, iwo. . . .Ngati munthu aliyense awachitira iwo

mosayenera, kuwapweteka iwo: “moto ukutuluka kuchokera mkamwa mwawo,” Moto wa Mzimu Woyera, Mawu. Mawu ali Mulungu. Mawu ali Moto. Mawu ali Mzimu. Mwawona? “Kutuluka kuchokera mkamwa mwawo.”

289 Penyani pa Mose. Tiyeni tiwone chimene chikutuluka kuchokera mkamwa mwake. Iwo, Israeli, anafika ku, momwe iwo ankachitira kumeneko, a—a...Ine ndikutanthawuza, Igupto, iwo anali kuwazunza Ayuda awa. Mose...Chabwino, iwo sankawalola iwo kuti apite. Farao sankawalola. Mulungu anayika mawu mkamwa mwa Mose. Mwawona, ndi maganizo a Mulungu kupita mu mtima mwa Mose; iye akupita uko tsopano kukawafotokoza iwo, ndiye iwo akukhala Mawu. Anatambasula dzanja lake, anati, “Pakhale ntchentche,” ndipo apa pakubwera ntchentche. Penyani apa.

Ndipo ngati munthu aliyense ayipsa iwo, moto ukutuluka kuchokera mkamwa mwawo, ndi kuwaononga adani awo: . . .

290 Mukuwona? Apo izo ziri. Iwo akhoza kulankhula chimene iwo akufuna, ndipo apo icho nkuchitika. Ameni!

. . . ndipo ngati munthu aliyense . . . ayipsa iwo, iwo ayenera mu chikhalidwe ichi kuphedwa.

291 M'bale, Mulungu akukwera powonekera apa!

Iwo ali nayo mphamvu kuti—mphamvu kuti atseke miyamba, kuti isavumbe mu masiku akunenera kwawo: . . .

292 Eliya, iye akudziwa kuchita kwake izo; iye anazichitapo izo kale. Ameni! Mose amadziwa kuchita kwake izo; iye anachitapo izo kale. Ndicho chifukwa chake iwo amakonda kuwabweretsanso. Tsopano . . . Ameni!

293 Ine ndikhoza kulankhula chinachake chowopsya bwino pomwe apa, koma ine ndibwino—ndibwino ndichisunge icho mpaka mawa usiku. Mwawona? Chabwino.

. . . ndipo ali nayo mphamvu pa madzi kuwasandutsa iwo kukhala magazi, ndi kukantha dziko lapansi nayo . . . miliri, mocholuka monga iwo adzafunire.

294 Nchiyani chimenecho? Nchiyani chimene chingabweretse zinthu izi koma Mawu? Iwo akhoza kuchita nacho chirengedwe mulimonse mmene iwo akufunira. Apa izo ziri. Ndiwo amene akubweretsa apo Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi ichi. Iwo akuvundukula ndi kuchitsegula icho. Ndiyo Mphamvu ya Mulungu, kuti asokoneze chirengedwe. Mukuwona, Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi chiri kwathunthu kusokonezeka kwa chirengedwe. Kodi inu mukumvetsa zimenezo tsopano? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndi chimenecho Chisindikizo chanu. Ndani yemwe akuchita izo? Ndi aneneri, mbali yina ya Mkwatulo. Ndi Mphamvu ya

Mulungu, Mawu a Mulungu, iwo akungotsutsa chirengedwe. Iwo akhoza kutumiza zivomezi, kusandutsa mwezi kukhala magazi, dzuwa likhoza kupita pansi, kapena chirichonse, mwa kulamula kwawo. Amen!

²⁹⁵ Ndi zimenezotu. Ndi zimenezotu. Mukuwona? Mwawona momwe Zisindikizo zinatsegukila, kumusi uko mu m’badwo wa mpingo, momwe izo zinawonetsera ofera?

²⁹⁶ Ndipo tsopano apa pali aneneri awiri awa atayimirira apa ali nawo Mawu a Mulungu, kuti achite chirichonse kwa chirengedwe chimene iwo akufuna. Ndipo iwo akugwedeza dziko lapansi. Ndipo izo zikuwonetsa chimodzimidzi yemwe akuchita izo. Ali Mose ndi Eliya, chifukwa apo pali utumiki wawo ukubwerezedwanso kachiwiri, ali amuna onsewo. O, mai! Kodi inu mukuwona izo tsopano? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Mwawona chimene chiri Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi? Ndicho aneneri amenewo. Tsopano zindikirani. Musalole icho chikutsamweni inu. Koma, yang’anani chimene chinatsegula Chisindikizo chimenecho, aneneri! Mukuwona? Psyi! Amen! Ndi zimenezotu.

²⁹⁷ O, ife tikukhala mu tsiku la mphungu, m’bale, kulunjika mmwamba pakati pa mitambo!

²⁹⁸ Iwo anatsegula Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi icho. Iwo ali nayo mphamvu kuti achite izo. Amen! Ndi chimenechotu Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi chanu kubwera chikutseguka. Mwawona?

²⁹⁹ Tsopano ife tibwerere mmbuyo kumene apa, ndipo Yesu analankhula kuti izo zidzachitika. Mmbuyo kale kutali mu Chipangano Chakale, mmbuyo mu Ezekieli, mmbuyo mwa aneneri akale, iwo analankhula kuti izo zikanadzachitika.

³⁰⁰ Ndipo apa Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi chatsegulidwa, ndi iwo akumati, “Chabwino, ndicho chinthu chachinsinsi. Nchiyani chinachita icho?”

³⁰¹ Apa pali chinsinsi cha icho, aneneri, chifukwa Baibulo linanena choncho apa. Iwo akhoza kutsegula icho, nthawi iliyonse iwo...Iwo akhoza kuchita chirichonse kwa chirengedwe chimene iwo akufuna kutero. Ndipo iwo akuchita chinthu chomwecho iwo anachichita, ameni, chifukwa iwo akudziwa momwe izo zimachitikira. Amen! Ulemerero!

³⁰² Pamene ine ndinawona zimenezo, ine ndinangonyamuka kuchokera pa mpando ndi kuyamba kuyenda mmwambandi-pansi. Ine ndinaganiza, “Ambuye, momwe ine ndikukuthokozerani Inu, Atate Akumwamba!”

³⁰³ Apo izo ziri. Ndi zimenezo. Iwo anatsegula Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi icho. Amen! Ayang’anani iwo, “Ngati munthu aliyense awayipsya iwo, moto ukutuluka kuchokera

mkamwa mwawo,” Mawu. Mzimu Woyera kubwera pa atumwi, inu mukuwona. “Moto unatuluka kuchokera mkamwa mwawo.”

304 Tsopano zindikirani uko mu Chivumbulutso 19, ife tikuwona chinthu chomwecho, “Ndipo lupanga lalikulu likutuluka kuchokera mkamwa Mwake,” Mawu. Mwawona? Kudza kwa Khristu. “Ndipo Iye anawapha adani Ake ndi Ilo.” Kodi nkulondola uko? [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.] Tsopano Iye ali pa njira Yake. Muyang’aneni Iye tsopano. Chabwino.

Awa ali nayo mphamvu kuti atseke miyamba, kuti isavumbenso mu masiku a uneneri wawo: . . .

305 Mnyamata, ndiko kusokoneza chirengedwe! Tsopano, ndi kwa nthawi yotalika bwanji anachita—anachita munthu uyu, Eliya, kutseka kwa miyamba? [Osonkhana ati, “Zaka zitatu ndi theka.”—Mkonzi.] Ndi zimenezotu, chimodzimidzi. Liri lotalika bwanji gawo la makumi asanu ndi chiwiri la Daniele, gawo lotsiriza la masabata makumi asanu ndi awiri? [“Zaka zitatu ndi theka.”] Ndi zimenezotu, chimodzimidzi.

306 Mose anachita chiyani? Iye—iye—iye anasandutsa m—madzi kukhala magazi. Iye anachita mtundu wonse uwu wa zozizwitsa, chimodzimidzi basi zomwe zanenedweratu apa pansu pa Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi. Ndipo apa iwo ali, mu Chivumbulutso 11, akuchita chinthu chomwecho. Amen!

307 Apo pali malo atatu osiyana mu Malemba, pomwe apo, kulumikiza chinthucho pamodzi kumene. Ndiko kutsegula kwa Chisindikizo Chachisanu chimodzi. Pomwepo icho chiri. Amen! Ulemerero! Tsopano zindikirani.

Awa ali nayo mphamvu kuti atseke miyamba, mu masiku a uneneri wawo, kuti isavumbe: ndi . . . mphamvu pa madzi kuwasandutsa iwo kukhala magazi, . . . kukantha dziko lapansi nayo . . . miliri, mochuluka momwe iwo adzafunire.

308 O, mai! Ndi zimenezotu. Tsopano tsegulani cha apa ku miliri, mwawona. Chirengedwe chonse chasokonezedwa, mu Mliri uwu wa Chisanu ndi chimodzi . . . kapena Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi, kutsegula. Ndicho chimodzimidzi zomwe zinachitika. Tsopano penyani. A . . .

309 Apa, Mulungu ali pafupi kuwombola mwana Wake, Israeli, chitatha chisawutso cha mtundu womwewo chimene Iye anachita kumusi uko. Iye anatumiza Mose kumusi uko ndipo anawombola Israeli. Kodi nkulondola uko? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndipo iye anachita zinthu zomwe zomwezo. Iye anatumiza Eliya kwa Ahabu, ndipo zikwi zisanu ndi ziwiri anatuluka. Nkulondola uko? [“Ameni.”] Iye akuwatumiza iwo uko apa kachiwiri, mu nthawi ya Chisawutso, ndipo akuyitana zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi.

310 Tsopano, onani, inu mukuzindikira, pakati pa Chivumbulu-...kapena pakati pa mutu wa 6, kapena Mliri wa Chisanu ndi chimodzi...Chisindikizo, mundikhululukire ine, Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi ndi Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri. Mutu wa 7 wa Chivumbulutso, mwamasamu, zikukhala pamodzi molondola.

311 Monga momwe Amerika ali chiwerengero cha khumi ndi zitatu: mayiko khumi ndi atatu anayamba nawo, nyenyezi khumi ndi zitatu mu mbendera, zigawo khumi ndi zitatu, milozo khumi ndi itatu. Chirichonse chiri khumi ndi zitatu, khumi ndi zitatu. Ndipo akuwonekera pomwe apa mu mutu wa 13 wa Chivumbulutso. Uko nkulondola. Iye ali khumi ndi zitatu, ndipo mkazi.

312 Tsopano, pamene Iye anali pafupi kuwombola Mwana Wake wobalidwa yekhayo, yemwe anali wobalidwa Wake yekhayo. Yakobo ali mwana Wake; koma uyu ali Mwana Wake wobalidwa yekhayo. Mateyu 27, tiyeni tiwone chimene Iye anachita kumeneko. Mateyu, mutu wa 27. Tsopano, kumbukirani, Mwana Wake anali atamenyedwa, ndipo anali atavutitsidwa, ndipo iwo anali atamutonza Iye. Ndipo Iye anali tsopano atapachikika pa mtanda, nthawi ya 3 koloko, pa Lachisanu Labwino madzulo. Ziri pafupi pokha kuti zichitike! Mateyu, mutu wa 27 wa Mateyu, ndipo n—ndime ya 45, ine ndikukhulupirira iyo ili.

Tsopano kuchokera ora lachisanu ndi chimodzi kunali mdima pa dziko lonse mpaka ora lachisanu ndi chinai.

313 Tsopano zindikirani chimodzimidzi basi zomwe Iye anachita mmbuyo muno tsopano, mu izi. Mwawona?

Ndipo ine ndinawona pamene iye anali atatsegula chisindikizo chachisanu ndi chimodzi, . . . tawonani, apo panali chivomezi chachikulu; ndipo dzuwa linada monga chiguduli cha ubweya, ndi mwezi—ndipo mwezi unakhala ngati magazi;

314 Kuda, mdima! Igupto; kuda, mdima!

315 Mulungu, akuwombola Yesu pa mtanda, basi Iye asanamudzutse Iyeyo kuchokera ku chiwukitsiro. Choyamba, mdima; dzuwa linalowa liri pakati pa tsiku, ndipo nyenyezi sizinathe kuwala. Masiku awiri kuchokera pamenepo, Iye amakamuwukitsa Iye ndi chigonjetso champhamvu.

316 Litatha dzuwa, ndi mwezi, ndi nyenyezi, ndi chirichonse, mu Igupto, zonse izi zomwe zitachitika, Iye anawombolera Israeli ku dziko lolonjzedwa.

317 Apo izo ziri, mu nthawi ya Chisawutso, ndipo apa pakuyima aneneri awo kwa amene ali nawo ulamuliro wa Mawu amene Mulungu akuwapatsa iwo. Iwo akhoza kulankhula pokha pamene Mulungu akuwapatsa iwo Mawu.

318 Tsopano, iwo sali milungu. Iwo ali mwakanthawi... Mochepa, iwo ali, chifukwa Yesu anati iwo anali. Anati, “Inu mmawatcha iwo milungu, amene Mawu a Mulungu ankafikirako.” Koma, penyani, ndiwo omwe Mulungu amabweretsako Mawu. Ndipo pamene iye alankhula Iwo, izo zimachitika. Ndizo zonse.

319 Ndipo apa iye ali ndi kutuma kochokera kwa Mulungu, kuti akanthe dziko lapansi, chirichonse chimene iye akufuna kuchita (o, mai), kuyimitsa miyamba. Ndipo iye amachita. Chavuta nchiyani? Iye akukonzekera kutenga zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi zituluke, mwa chiwombolo, kuchokera m’Bukhu la Chiwombolo. Ndipo izo ziri pansa pa Chisindikizo cha Chiwombolo, mu Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi. Ndi chimenechotu, amzanga okonedwa. Ndicho Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi icho; chakhala mwachinsinsi kwambiri.

320 Tiyeni tingotenga...Ife tiri nawo maminiti khumi ena. Tiyeni tingotenga pang’ono pokha, mwawona. Ine ndiri nawo pafupi masamba awiri kapena atatu. Chabwino, ine ndiyenera...Inu mukhoza kungowona, *apa*. Ine ndikuganiza apo pali pafupi...Pa chimodzi icho, ine ndikuganiza ine ndiri nawo pafupi masamba khumi ndi asanu atsalirabe, ine ndikanakhoza kufika kwa iwo. O, pali zambiri pa izo! Mai, iwe ukhoza kumangopitirirabe kuchoka pa malo kupita pa malo! Koma ine ndikuwopa ine ndidzakusokonezani inu pamene ine ndibalalitsa mochulukwa kwambiri. Ndipo ine sindiri...Ine sindingakhoze kuziyika izo pamodzi monga ine ndiyenera.

321 Mu Yesaya, tiyeni titenge ichi. Yesaya, mneneri, anawona Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi ichi chikutseguka, ndipo analankhula za Icho; monga kaya Icho nchofunikira, kapena ayi. Mukuwona?

322 Chabwino, chinthu chonse, dongosolo lonse la Chiwombolo, likugona pansa pa Zisindikizo izi; Bukhu lonse.

323 Tsopano kumbukirani, ife tinamuwona Yesu anachiwona Icho. Kodi nkulondola uko? Mwawona? Yesu anachiwona Icho. Ndipo tsopano ife tinapeza ena omwe anachiwona Icho. Ife tikupeza Icho chikuyimiridwa mu—mu Yakobo. Ife tinachipeza Icho chikuyimiridwa mu Igupto. Ife tikuchiwona Icho chikuyimiridwa pa mtanda.

324 Tsopano tiyeni tibwerere ku Yesaya. Ine ndiri nawo aneneri ambiri amene ndawalemba apa, nawonso. Tiyeni chabe...Ine ndimakonda izi, izi za Yesaya. Tiyeni tibwerere mmbuyo apa ku Yesaya, mutu wa 13 wa Yesaya. Ine ndimakonda... .

325 Yesaya ali Baibulo 1—lathunthu, mwa Lokha, inu mukudziwa. Kodi inu mukudziwa zimenezo? Mwawona, Yesaya akuyamba ndi chirengedwe; mkati mwa Bukhu iye akumubweretsa Yohane; ndipo pa mapeto iye akubweretsa

Zakachikwi. Ndipo muli Mabuku makumi asanu ndi limodzi mphambu asanu ndi limodzi mu Baibulo, ndi mitu makumi asanu ndi limodzi mphambu asanu ndi umodzi mu Yesaya. Ilo liri kufotokoza kwathunthu, Palokha.

³²⁶ Zindikirani, mutu wa 13 tsopano, wa—wa Yesaya. Tiyeni tiyambire apa pa ndime ya 6.

Kuwani inu; pakuti tsiku la YEHOVA liri pafupi; ilo lidzadza monga chiwonongeko kuchokera kwa Wamphamvuzonse.

³²⁷ Yang'anani Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi ichi chikutseguka pamwamba apa tsopano. Mmbuyo muno apa, zaka mazana asanu ndi awiri ndi khumi ndi zitatu Khristu asanabwere, ndipo Iye wakhala ali zaka zikwi ziwiri, zomwe zikanadzakhala pafupi zisanu ndi ziwiri. . . pafupi zaka mazana makumi awiri ndi zisanu ndi ziwiri zapitazo. Yesaya anawona Chisindikizo ichi chitapachikika pamenepo. Chabwino.

Chifukwa chake manja onse adzafowoka, ndi mtima wa munthu aliyense udzasungunuka:

³²⁸ Yesu ananena chiyani? “Ndipo chifukwa kusaweruzika kudzachuluka, c—chikondi cha ambiri chidzazirala ndiye.” “Ndipo mtima wa munthu udzakhala ukulepherera, chifukwa cha mantha; nyanja ikubangula.” Mwawona, mtima wa munthu udzafowoka.

Ndipo iwo adzawopa: kuwawa kwa zisoni zidzawagwira iwo; iwo adzakhala mu kupweteka monga mkazi yemwe akuvutika pakubala: iwo adzazizwa mmodzi pa mzake; nkhope zawo zidzakhala monga manyazi.

³²⁹ Zindikirani za icho apa, o, “nkhope zawo, manyazi.” Ife tiyenera kufika ku chimenecho, miniti chabe. Ine ndigwira kwa icho, mwawona.

Tawonani, tsiku la AMBUYE likudza, lankhanza limodzi nawo mkwiyo ndi ukali wowopsya, kuligoneka dziko bwinja: ndipo iye adzawononga ochimwa ake kuchokera mmenemo.

³³⁰ “Dzikolo,” ndizo zonse za izo, za izo inu mukuziwona. Zindikirani.

Pakuti nyenyezi za kumwamba ndi makamu awo sizidzapereka kuwala kwawo: dzuwa lidzadetsedwa mu kutuluka kwake, ndipo mwezi sudzapangitsa nyali zake kuti ziwale.

Ndipo ine ndidzalanga dziko chifukwa cha kuyipa kwawo, ndi kusaweruzika, ndi kuyipa kwa kusaweruzika kwawo; ndipo ine ndidzapangitsa mwa- . . .

331 Ine—ine sindikudziwa momwe ungatchulire ilo, mwa-... [Osonkhana ati, “Mwano.”—Mkonzi.] Ine sindingakhoze kunena ilo, mwawona.

*. . . a kudzikuza kusiya, ndipo ndidzatsitsira mmusi
kudzikweza kwa—kwa chowopsya—chowopsya.*

332 Mwawona, pamenepo, chimodzimodzi basi, Yesaya anawona chinthu chomwecho chimene Yesu analankhula za icho. Chimene Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri chikuwulula. Pamene Iye akuyeretisa dziko ndi chisawutso, ndiyo nthawi ya Chisawutso, Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi ichi. Inde, iye anali mneneri, ndipo Mawu a Mulungu anazindikirika kwa iye. Ndizo zaka makumi awiri ndi zisanu ndi ziwiri zapitazo.

333 Mowona! Ine ndikungofuna kunena ichi. Dziko lonse, monga Yesaya apa, “monga mkazi amavutikira,” chirengedwe chonse chikuvutikira. Kubuwula konse uku ndi kuvutikira nkwa chiyani? Monga m—m—mkazi amene ati akhale mayi; dziko lapansi palokha, chirengedwe.

334 Bwanji, mzinda uwu apa, tiyeni titenge mzinda wathu womwe; pamene, malo a mowa, ndi chiwerewere, ndi uve, ndi chonyansa, monga mzinda uliwonse!

335 Bwanji, ine ndikukhulupirira Mulungu akanakhala bwinoko, kuyang’ana pa ilo momwe Iye anali nalo ilo, zaka zikwi zapitazo. Pamene Ohio ankapita pansu, iwo analibe madzi obwerera ndi zosefukira. Iwo analibe tchimo mu chigwa. Njati zinkayenda kupyola kuno, ndipo—ndipo Cherokee wakale ankazisaka izo ndi kupanga kukhala moyo wabwino. Panalibe vuto, nkonse.

336 Koma, munthu anabweramo, apo pali pamene tchimo likubwera mkati. Pamene anthu anayamba kuchuluka pa nkhope ya dziko lapansi, ndiye tchimo ndi chisokonezo chinakhalamo. Uko nkulondola, nthawizonse munthu. Bwanji, ine ndikuganiza icho chiri chamanyazi!

337 Ine ndinali kuyimirira, tsiku lina, mu dziko la kwathu uko, tsopano mu Arizona. Ndipo ine—ine ndinawerenga, pamene ine ndinali mwana, za Geronimo, ndi—ndi Cochise, ndipo awo Apache akale. Chifukwa, ine ndinalalikirira kwa iwo kumeneko. Anthu abwino! Ndipo amodzi a anthu abwino kwambiri iwe ukufuna kukumana nawo, ali Amwenye achi Apache awo.

338 Ndiyeno ine ndinapita cha kumeneko ku—ku Tombstone, kumene iwo ali nazo zinthu zakale zonse ndi zinthu kuchokera ku nkondo. Ndipo ine ndiyang’ana pa . . . Iwo nthawizonse, inu mukudziwa, iwo nthawi zonse ankamutenga Geronimo monga—monga chigawenga. Kwa ine, iye anali Mmerika wa magazi-ofiira. Mwamtheradi! Iye anali kumenyera chabe maufulu ake, monga aliyense akanachitira. Iye sankafuna chivundi chimenecho mu dziko lake. Ndipo penyani chimene icho chiri tsopano; kuwatembenuza ana ake, ana aakazi ake, kukhala

mahule, ndi china chirichonse; ndipo azungu kubwera mkati umo. Mzungu ndi mthakati.

³³⁹ Mmwenye anali wosamalira. Iye anali—iye anali w—wosamalitsitsa. Iye amakhoza kutuluka ndi kukapha njati, fuko lonse linkadya chirichonse chotsalira cha iyo. Iwo ankagwiritsa ntchito chikopa kupangira nsalu ndi mahema, ndi china chirichonse. Ndipo mzungu akubwera ndi kudzawombera iyo, mwa chandamale; bwanji, chiri chamanyazi chotero!

³⁴⁰ Ine ndinawerenga nkhani mu pepala, pamene, mu Afrika, malo akulu awo odzaza ndi zinyama zakuthengo! Iwo ali nawo anyamata awa, Arthur Godfrey ndi iwo, akupita kumeneko, akukawombera njovu izi ndi zinthu, kuchokera mu helikopitala ndi zinthu monga choncho. Chithunzi cha njovu yaikazi yokalamba kuyesera kufa, ndipo misozi, monga, kusololera pansi nkhope yake. Ndipo zamphongo ziwiri zazikulu kuyesera kumugwira iye, kutetezera. . . Bwanji, ndi tchimo. Awo sindiwo masewera.

³⁴¹ Pamene ine ndiyima pa thengo kunjira kutsidya, ndi kumene ine ndimasaka ndi zinthu monga choncho, ndi kuwona kumene alenje achizunguwo amabwera kumeneko ndi kuwombera agwape awo, ndi kudula miyendo ya kumbuyo kuyichotsa kwa iye. Ndipo nthawizina kupha agwape aakazi ang'ono asanu ndi atatu kapena khumi, ndi kuwasiya iwo atagona pamenepo. Ndipo tiana tikuthamanga pozungulira, kuyesera kupeza mayi wawo. Ndipo inu mukutanthawuza uko ndi kudziwa masewera? Iko ndi kupha kwangwiro, mu bukhu langa.

³⁴² Ine ndikuyembekeza Canada sapeza misewu iliyonse mwa izo, malingana ngati ine ndikhala moyo, kuwaletsa zigawenga za Amerika asafike kumeneko. Uko nkulondola. Iwo ndi masewera osawuka amene ine ndinawawonapo mu moyo wanga.

³⁴³ Tsopano, osati onse a iwo. Alipo ena enieni, anthu enieni, koma ndi mmodzi kuchokera mu chikwi, inu mungamupeze.

³⁴⁴ Kuwombera chirichonse iwo angakhoze kuchipenya, mulimonse iwo akufuna kuchitira. Uko nkulondola. Iyo ndi mbanda. Uko nkulondola. Iye ndi wopanda mtima. Ndipo iye akuwombera, isali nyengo yake.

³⁴⁵ Chabwino, kumtunda uko mu Alaska uko, ine ndinali pamwamba apo ndi mmodzi wa anamulondola awo. Iye anati, “Ine ndinatenga. . . ine ndimakhoza kupita kumeneko tsopano, ndi kukapeza magulu onse agwape akulu awo kapena. . . osati gwape, koma insa itagona pamenepo; ili ndi zipolopolo za mfuti ya mphamvu makumi asanu zipololo zake kupyola nyanga zake, kumene mapayiloti Achimerika awa kumeneko, mu Alaska, mfuti zamizinga, kuchokera mu ndege, gulu la insa.” Iyo ndiwo mbanda yangwiro.

³⁴⁶ Iwo ankadziwa, pamene iwo apha njati, iwo akhoza kuwakhawulitsa Amwenye. Iye akanafa ndi njala. Ndicho

chifukwa chake a Cochise anachita kudzipereka; ake, akalonga ake onse, ndi ena onse a iwo, ana ake, ndi onse a anthu ake, anali kufa nayo njala. Iwo ankapita kumeneko ndi zazikulu, akatundu akulu mwamphamvu a izo, Mtengo wa Njati ndi anthu akuchigwa awo, ndi kuwombera njati zonsezo, makumi anai, makumi asanu, madzulo. Iwo akudziwa, pamene iwo anatha izo, iwo athana naye Mmwenye. O, mai! Banga pa mbendera, momwe iwo anachitira nawo Amwenye awo. Ndi zimenezotu.

³⁴⁷ Koma kumbukirani, Baibulo linati, “Ora lafika limene Mulungu ati adzawawononge iwo amene awononga dziko lapansi.” Ndi dziko lonse!

³⁴⁸ Yang’anani pa zigwa izo. Ine ndinali kuyimirira pamwamba apo tsiku lina, kuyang’ana mmusi pa chigwa ku Phoenix. Ndinapita pamwamba pa Phiri la South, mkazi wanga ndi ine tinali kukhala pamenepo, ndipo ndinayang’ana mmusi ku Phoenix. Ndipo ine ndinati, “Kodi icho si choyipa?”

Iye anati, “Choyipa? Iwe ukutanthawuza chiyani?”

³⁴⁹ Ine ndinati, “Tchimo. Ndi kuchuluka kotani kwa chigololo, ndi kumwa, ndi kutukwana, ndi Dzina la Ambuye kugwiritsidwa ntchito mwachabe, mu chigwa icho uko; ndi pafupi zana ndi—ndi makumi anai, anthu zikwi makumi asanu, kapena mwinamwake anthu zikwi mazana awiri, mu chigwa chimenecho!”

³⁵⁰ Ine ndinati, “Zaka mazana asanu zapitazo, kapena chikwi, umo munalibe kanthu koma akaloga, lijowe, ndipo ankhandwe akale akuthamangathamanga mu mchenga wa mu mtsinje kumeneko, m—makhwawa.” Ndipo ine ndinati, “Ndimomwe Mulungu analipangira ilo.”

³⁵¹ Koma, munthu anabweramo. Kodi iye anachita chiyani? Iye anadzazitsa dziko ndi uve. Misewu iyi yadzaza ndi ndulu. Zonyasa, n...Ndipo mitsinje yayipitsidwa ndi—ndi uve. Iwo sangakhoze...Bwanji, inu kuli bwino kusamwa dontho la ena a madzi awo; inu mungatenge chirichonse. Mukuwona? Penyani pa icho. Osati apa pokha, koma, dziko lonse, chinthucho chawonongedwa!

³⁵² Ndipo dziko, chirengedwe, (Mulungu achite chifundo!) dziko lonse...ndipo mu kupweteka kwa kubala. Dziko likuyesera, ilo “likusawutsika,” Yesaya anati. Chavuta nchiyani? Ilo liri mu...kuyesera kubala dziko latsopano, kwa Zakachikwi, kumene onse...?....Kuyesera kubala dziko latsopano, kwa anthu atsopano omwe sadzachimwa ndi kuliwononga ilo. Uko nkulondola. Ilo liri mu kusawutsika. Ndicho chifukwa chake i—i...Ife tiri mu kusawutsika, Khristu, kuti abale Mkwatibwi. Chirichonse chiri mu kusawutsika ndi kubuwula. Mwawona, pali chinachake chikukonzekera kuchitika.

³⁵³ Ndipo Mliri wa Chisanu ndi chimodzi uwu ukulola ilo kupita. M’bale, chivomezi chikuphulitsa motseguka, ndipo nyenyezi kugwedezeka, ziphala zamoto zidzatulukira, ndipo

dziko lapansi lidzadzisinha lokha. Phala lamoto latsopano lidzafalikira kuchokera mkati mwa dziko lapansi. Ndipo ilo lidzasweka, lonse mozungulira ndi kuzungulira ndi kuzungulira, pamene ilo likutembenezika kumeneko.

³⁵⁴ Ndipo ine ndikukuwuzani inu, mmawa umodzi pamene Yesu ndi Mkwatibwi Wake akubwerera pa dziko lapansi, padzakhala paradiso wa Mulungu pamenepo. Mwakuti, o, mai, ankhondo awo akale a nkhondo, akuyenda kudutsa mmenemo ndi abwenzi awo ndi okonedwa. Nyimbo zidzadzaza mu mlengalenga, za khamu la Angelo. “O, wachita bwino, wantchito Wanga wabwino ndi wokhulupirika. Lowa mu zisangalalo za Ambuye, zomwe zakonzeredwera iwe, zonga iwe ukanayenera kukhala nazo kumbuyo uko Eva asanayambe kugudubuza mpira mu tchimo.” Amen! Psyii! Inde.

³⁵⁵ Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi chichita chinachake. Inde, bwana. Mowona dziko lonse likubuwula ndi kumwa kuwawa, chifukwa cha m’badwo wa Zakachikwi!

³⁵⁶ Tsopano, ili lomwe tsopano lanyowetsedwa ndi uve! Izo ine ndinalalikira kuno, osati kale litali, ine ndikukhulupirira, ndinalalikira ku kachisi, *Dziko Likuphwasuka*. Ndicho chimodzimodzi. Penyani zomwe zikuphwasuka mu dziko. Penyani, chirichonse chikugwa, cha ilo. Ndithudi, ilo liri. Ilo—ilo liyenera kuphwasuka. Inde, bwana.

³⁵⁷ Penyani, chimango chake! Ndiroleni ine ndikusonyezeni inu chifukwa chimene dziko liyenera kuchita icho. Chimango cha dziko lino, chitsulo, ndi mkuwa, ndi zipangizo za dziko lapansi, zachotsedwa mkati mwa ilo, ntchito ya chimango chake, chifukwa cha nkhondo ndi mafakitale, mpaka ilo liri chabe pafupi kukonzeka. . . Chabwino, ife sitinakhalepo nacho chivomezi mpaka tsiku lina, kuno mu gawo ili la dziko; chabe tsiku lina kuno, inu mukuwona, St. Louis ndi pansu kupyola kumeneko. Ilo likuwonda kwambiri. Iwo asolola chirichonse mkati mwa ilo. Mukuwona?

³⁵⁸ Ndale zake ziri zowonongedwa kwambiri, uko kulibe nkomwe wowona mtima pakati pa iwo, mwawona, kachitidwe kake. Makhalidwe ake ali pansu kwambiri, ilo basi liribe alilonse. Ndizo zonse. Mukuwona? Ndithudi. Chipembedzo chake chawuma. Ine, bwana.

³⁵⁹ Ndiyo nthawi ya Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi, posachedwapa, kuti chizitseguka. Ndipo pamene ilo likutero, o, mai, ilo likutha! Mkwatibwi wapita kale, iye wachita kale. . . Mfumukazi yapita kale kukatenga malo Ake; Iye wakwatiwa tsopano, kwa Mfumu, pamene izi zikuchitika. Ndipo wotsalira wa Israeli wasindikizidwa ndi kukonzekera kupita, ndiyeno chirengedwe chisiya kugwira. O, nthawi yotani!

³⁶⁰ Zindikirani ndime yotsiriza ya Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi, yatsegulidwa. Iwo amene anaseka pa kulalikira

kwa Mawu, kwa Mawu otsimikiziridwa a Mulungu wamoyo; pamene aneneri awo anali atayima pamenepo ndi kuchita zodabwitsa, kutseka dzuwa, ndi china chirichonse, ndi monse mpaka mmusi kupyola mu m'badwo. Mwawona, "Iwo analirira kwa mathanthwe ndi mapiri kuti ziwabise iwo," mwawona, kuti ziwabise iwo kwa Mawu omwe iwo anawaseka, chifukwa iwo anamuwona Iye akubwera. "Tibiseni ife kwa mkwiyo wa Mwanawankhosa." Iye ali Mawu. Mwawona? Iwo anaseka pa Mawu. Ndipo apa Mawu anali, mu thupi. Ndipo iwo anali atawaserewula Iwo; anaseka pa iwo, kuwaserewula iwo. Ndipo Mawu mthupi anagwa pamenepo!

³⁶¹ Bwanji iwo sanalape? Iwo sakanakhoza. Icho chinali chapatali, apo. Kotero, iwo ankadziwa icho, chirango. Iwo akuwamva Iwo. Iwo anakhala mu misonkhano monga chonchi ndipo anadziwa za Iwo. Ndipo iwo anadziwa kuti zinthu za aneneri amenewo, zinali zitanenedweratu, zinali kuwayang'ana iwo mu nkhope momwe, chinthu chimene iwo anali atachikana. Iwo anali atakana chifundo kwa nthawi yotsiriza.

³⁶² Ndipo pamene iwe ukana chifundo, palibe kanthu katsalira koma chiweruzo. Pamene iwe ukana chifundo; ingoganizani za izo.

³⁶³ Ndipo apo iwo anali. Iwo analibe malo woti apiteko, popanda kothawira. Ndipo Baibulo linanena apa, "Iwo anayitanira...Kulirira kwa mathanthwe ndi mapiri, kuti, 'Igwanani pa ife, ndi kutibisa ife kwa—kwa nkhope ya...ndi mkwiyo wa Mwanawankhosa.'" Iwo anayesera kulapa, koma Mwanawankhosa anali atabwera kudzatenga Ake Omwe, mwawona. Ndipo iwo analirira kwa mathanthwe ndi phiri. Anapemphera, koma mapemphero anali mochedwa kwambiri.

³⁶⁴ M'bale wanga, mlongo, ubwino ndi zifundo za Mulungu, zinapitirizidwa kwa anthu. Pamene, Israeli anachititsidwa khungu kwa izi, kwa apa, chabe pafupi zaka mazana awiri, kuti atipatse ife mwayi kuti tilape. Kodi inu mwakankhira pansu chifundo chimenecho? Kodi inu mwatero? Kodi inu mwakana Icho?

³⁶⁵ Ndinu ndani, mulimonse? Nanga inu munachokera kuti? Ndipo inu mukupita kuti? Inu simungakhoze kumufunsa dokotala, inu simungakhoze kumufunsa aliyense mu dziko, ndipo palibe bukhu limene inu mungakhoze kuwerenga, lomwe lingakhoze kukuwuzani inu yemwe inu muli, kumene inu munachokera, ndi komwe inu mukupita, koma Bukhu ili.

³⁶⁶ Tsopano, inu mukudziwa, popanda inu kukhala nawo Magazi a Mwanawankhosa kuti achite mmalo anu, inu mukuwona komwe inu mwalunjika. Kotero, ngati—ngati Mulungu anachitira icho kwa inu, chinthu chochepa chomwe ife tikanakhoza kuchita chikanakhala kulandira zomwe Iye anachita. Ndicho chonse chomwe Iye anatifunsa ife kuti tichite.

³⁶⁷ Ndipo kukhazikika pa izi, ngati ine ndingapitirire, ine ndiyenera kubwera mpaka mu Mliri umenewo, zonse izo, ulaliki wa usiku wa mawa. Ndipo tsopano ine sindingakhoze kuchita izo, sindingapitirire paliponse. Ine ndalemba izo mmusi apa, mtanda, “yimira apa,” mwawona. Kotero, ndiye, ine—ine ndiyenera kuyembekezera mpaka mawa.

Tsopano tiyeni ife tiweramitse mitu yathu kamphindi chabe.

³⁶⁸ Ngati inu mulibe, amzanga ofunika, mulibe—simunalandire chikondi cha Mulungu uyu yemwe ine ndikumunena! Ngati inu simunati. . . Mvetserani kwa izi mwatcheru tsopano. Ngati inu simunalandire chikondi Chake ndi chifundo, inu mudzayenera kuyima pa ziweruzo Zake ndi mkwiyo.

³⁶⁹ Tsopano, inu, usiku uno, muli mu malo omwewo pamene Adamu ndi Eva anali m'munda wa Edeni. Inu muli nawo ufulu. Inu muli chinthu chawufulu. Inu mukhoza kupita ku Mtengo wa Moyo, kapena inu mukhoza kutenga dongosolo la chiweruzo. Koma, lero, pamene inu muli woganiza bwino, mu malingaliro anu olondola, ndipo inu muli athanzi mokwanira ku—kuwuka ndi kuvomereza izo, bwanji inu simukuchita icho ngati inu simunachite icho.

³⁷⁰ Kodi alipo anthu amenewo muno omwe sanati, nkomwe, kuchita icho? Ngati izo ziri choncho, mungangokweza dzanja lanu, kuti munene, “Mundipempherere ine, M'bale Branham. Ine tsopano ndikufuna kuchita izo. Ine sindikufuna ichi chibwere.” Tsopano kumbukirani, amzanga. . . Mulungu akudalitseni inu. Icho nchabwino. Ine ndiri. . .

³⁷¹ Awa sali malingaliro anga a Ichi. Ine—ine. . . Izi siziri zomwe ine ndakhala ndikuganiza; izo ziri zonse pamodzi kuchokera mwa ine. Kotero mundithandize ine, Mzimu Woyera ukudziwa izo. Ndipo inu mudikire, ngati Ambuye alola, mawa usiku, ine ndikufuna ndikuwonetseni inu chinsinsi chomwe chakhala chikupita nthawi yonse, pomwe apa mu msonkhano uno. Ine ndikukayikira kwambiri ngati inu munachiwonapo icho kapena ayi, mwawona, chomwe—chomwe chimachitika. Icho chakhala chinachake chomwe chayikidwa pomwe apa pamaso panu. Ndipo ine ndachiyang'ana, usiku uliwonse, ichi, kuti icho chiwuke, kuti winawake anene, “Ine ndachiwona icho.” Mukuwona?

³⁷² Musati muchikankhire Icho kutali, chonde, ine ndikukupemphani inu; ngati inu simuli Mkristu, ngati inu—inu simuli pansu pa Magazi, ngati inu simuli wobadwa kachiwiri, wodzazidwa nawo Mzimu Woyera.

³⁷³ Ngati inu simunapangepo kuvomereza kwa pagulu kwa—kwa Yesu Khristu, pa kubatizidwa mu Dzina Lake, kuchitira umboni imfa Yake, kuyikidwa mmanda ndi chiwukitsiro, kuti inu mwavomereza iyo, madzi ali okonzeka. Iwo akuyembekezera.

Miinjiro imaperekedwa muno, ndipo chirichonse chiri chokonzeka.

³⁷⁴ Khristu akuyima wokonzeka, ndi mkono wotambasula, kuti akulandireni inu. Mu ora limodzi kuchokera pano, chifundo icho mwina sichitambasuliridwa kwa inu. Inu mukhoza kuchikankhira kutali icho kwa nthawi yotsiriza; icho sichidzakhudza konse mtima wanu kachiwiri. Pamene inu mukhoza, pamene inu mukhoza, bwanji inu simukuchita icho? Tsopano pamene. . .

³⁷⁵ Ine ndikudziwa njira ya nthawizonse, yachizolowezi, ili kuwabweretsa anthu kuno ku guwa. Ife timachita zimenezo, ndipo ndicho chabwino mwangwiwo. Pa nthawi ino, ife tiri awunyanji chotere muno, pozungulira guwa pomwe, mpaka ine sindingakhoze kuchita izo.

³⁷⁶ Koma ine ndikufuna kunena ichi. Mu tsiku la utumwi, iwo ankati, “Onse omwe anakhulupirira anabatizidwa.” Mukuwona? Basi ngati inu mungakhoze, kwenikweni, pansu mu mtima wanu! Apa pali izo zonse. Izo siziri—izo siziri kutengeka, ngakhale kutengeka kumatsatira izo. Monga ngati chimene ine ndinanena, kusuta ndi kumwa siziri tchimo; izo ziri chotsatira cha tchimo; izo zimasonyeza kuti inu simukhulupirira. Mukuwona? Koma pamene inu mukhulupirira mowona mu mtima mwanu, ndipo inu mukudziwa kuti pa chikhazikitso cha, pamene inu mwakhala apo, inu mwavomereza icho ndi mtima wanu wonse, chinachake chichitika pomwe apo. Icho chichitika.

³⁷⁷ Ndiye inu mukhoza kuyima monga mboni kwa icho, kuti chinachake chachitika. Ndiye yendani kumka ku madzi, nenani, “Ine ndikufuna kusonyeza kwa osonkhana, ine ndikufuna kutsimikizira, ine ndikufuna kupanga umboni wanga kuyima, kuti ndidzatenga malo anga ndi Mkwatibwi. Ine ndikuyima apa tsopano kuti ndibatizidwe.”

³⁷⁸ Ine ndikudziwa kuti alipo akazi ambiri mu dziko usiku uno, akazi abwino, koma ine ndiri wosungulumwa moyipa kuti ndimuwone mmodzi. Alipo mmodzi wa iwo ndiye mkazi wanga. Iye amapita kunyumba ndi ine. Iye sanali mkazi wanga, kuyamba nkuyamba; koma momwe iye anakhala mkazi wanga, iye anatenga dzina langa.

³⁷⁹ Iye ali kubwera. Alipo akazi ambiri, mipingo, mu dziko, koma Iye akubwerera Mkazi Wake. Iye akutchedwa mwa Dzina Lake. “Iwo omwe ali mwa Khristu Mulungu adzawabweretsa limodzi naye Iye.” Ife timalowa chotani mwa Ilo? “Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwira mu Thupi limodzi.”

³⁸⁰ Tsopano pamene ife tikupemphera, inu mupemphere, inunso. Mkati kapena kunjia, alipo magulu akulu a anthu mu zipinda, kunjia, ayimirira pozungulira, kunjia mmisewu. Koma tsopano pamene—pamene inu muli. . .Ife sitingakhoze kukuyitanirani inu apa ku guwa. Koma, mtima wanu,

upangeni iwo guwa. Ndipo mu mtima mwanu momwe, nenani, “Ambuye Yesu, ine ndikukhulupirira Izi. Ine ndayima kunjira kuno mu mpweya wa usiku uno. Ine ndabanikitsidwa, mu chipinda chaching’ono ichi. Ine ndakhala muno, pakati pa anthu awa. Ine—ine—ine—ine—ine sindikufuna kukhala... Ine sindingakhoze kuphonya; Ine sindingakhoze kukwanitsa icho.”

381 Chirichonse, monga ine ndinakuwuzirani inu usiku watha, ndipo, kotero ndithandizeni ine, Ambuye akudziwa kuti ine ndikunena Chowonadi. “Ine sindinama ayi,” monga Paulo ananena. Masomphenya aja, kapena chirichonse chomwe chinali; Ine ndinayima pamenepo, ndinayang’ana, ndi kuwagwira anthu amenewo omwe apita kale, basi zenizeni monga ine ndikuyima pomwe apa. Musati muphonye icho, m’bale wanga wosawuka kapena mlongo; musati muchite izo. Ine ndikudziwa inu mwandimva ine ndikulalikira, inu mwamva *izi, izo*, ndi nkhani, zonse izo. Koma lolani... Ingomverani. Kwa ine, ichi chiri... Ine ndikudziwa icho chiri Chowonadi, mwawona. Inu basi... ine—ine sindingakhoze kuzipanga izo kumveka kulikonse, mwawona. Musati muphonye izo. Zonse ndi zanu.

Tsopano tiyeni tipemphere.

382 Ambuye Yesu, apa patsogolo pa ine pali bokosi la mipango yomwe ikuyimira anthu odwala. Pamene ine ndikupempherera iyo, kusanjika manja pa iyo, monga Baibulo linanena, “Iwo anatenga kuchokera mu thupi la Paulo, mipango ndi zovala, mizimu yoyipa inatuluka mwa anthu, ndipo zizindikiro zazikulu zinachitika.”

383 Chifukwa, iwo anamuwona Paulo, yemwe iwo ankadziwa kuti Mzimu wa Mulungu unali mwa iye. Iwo amadziwa kuti iye anali—iye anali munthu wachirendo, kuti, zinthu zomwe iye ankazilankhula, za Mawu. Iye ankakhoza kupita kukatenga mawu akale a Chihebri a mpingo wa Chihebri, ndi kuwabweretsa iwo kukhala amoyo, ndi kuwayika iwo mwa Khristu. Iwo ankadziwa kuti Mulungu anali mwa munthu. Ndiye iwo ankawona Mulungu akuchita ntchito zachirendo ndi zamphamvu mwa iye, kulosera zinthu ndipo izo nkudzachitika mwa njira imeneyo, ndipo iwo ankadziwa kuti iye anali wantchito wa Mulungu.

384 Ambuye, ine ndikupemphera kuti Inu mudzalemekeze anthu awa chifukwa cha malemekezo awo a Mawu, ndi kuwachiza iwo chifukwa cha Yesu. Kuchokera muno mu msonkhano, Ambuye, pali anthu akhala, monga ngati zinali omwe anamvera kwa mtumwi Petro pa Tsiku la Pentekoste. Momwe iye anabwererera mu Mawu, ndi kukatenga Mawu! Ndipo iye anati, “Yoweli anati, mu masiku otsiriza zinthu izi zidzachitika. Ndipo Ichi ndicho icho.” Ndipo zikwi zitatatu anakhulupirira Iwo, ndipo anabatizidwa.

³⁸⁵ Ndipo, Atate, lero ife tikuyima pano mwa chisomo Chanu. Ndipo siziri chifukwa chakuti—kuti iwo ali anthu apadera, koma chiri chifukwa (monga ngati tsiku la mkango, kapena ng'ombe, kapena munthu) iyi ili nthawi ya mphungu. Ndi kudzoza kwa ora. Ndi nthawi yomwe ife tikukhalamo. Kuli kugwira ntchito kwa Mzimu Woyera pa nthawi iyi, kuti zitsimikizire kuti Yesu sali wakufa. Zinthu zomwe Iye ananena kuti Iye adzachita basi Kuwala kwa madzulo kusanazime, ndipo apa ife takhala tikumuwona Iye akuchita izo, mmusi momwe kutsatira msewu. Ife tawawona Iwo akubwera uko mu kufufuza kwa sayansi ndipo anajambulitsa chithunzi Chake; Lawi la Moto lalikulu Yemwe anatsogolera ana a Israeli; Yemwe anakomana naye Paulo pa msewu.

³⁸⁶ Ndipo ife tikudziwa, Lawi la Moto lomweli lomwe linalondolera Mose kumusi uko mu chipululu, mwa Lawi la Moto lomwelo iye analemba Mabukhu ochuluka a Baibulo, pakuti iye anali wodzozedwa nawo Mawu.

³⁸⁷ Lawi la Moto lomwelo kubwera pa Paulo, pa msewu waku Damasiko, iye analemba Mabukhu ochuluka a Baibulo, otchedwa Mawu a Mulungu.

³⁸⁸ Ndipo tsopano, Ambuye, Lawi la Moto lomwelo, mwa umboni wa chitsimikizo cha Mawu, ndi mwa kufufuza kwa sayansi, ife tikuliwona Ilo apa likuwulula Mawu a Ambuye.

³⁸⁹ Mulungu, mulole anthu afulumire kudzutsidwa, Ambuye, mwamsanga! Iwo omwe ali nawo maina awo atalembedwa pa Bukhu la Moyo; pamene Ichi chiwalira modutsa njira yawo, lolani iwo awone. Monga mkazi wamng'ono wa mbiri yoyipa pa chitsime tsiku lija, iye anazindikira mwamsanga, ndipo iye anadziwa kuti Ilo linali Lemba.

³⁹⁰ Ndipo tsopano, Atate, ine ndikupemphera kuti onse amene adzakulandireni Inu pa nthawi iyi, mu mitima yawo, akhazikitsa icho kwa nthawizonse, pa ora ili, kuti iwo athana nalo tchimo; kuti ati awuke ndi kupanga kukonzekera tsopano mwa kuvomereza kwa pagulu, kwa ubatizo mu Dzina la Yesu Khristu, kwa chikhululukiro cha machimo awo; kukasonyeza kuti iwo akukhulupirira kuti Mulungu wawakhululukira iwo, ndipo iwo akutenga pa Dzina la Yesu Khristu.

³⁹¹ Ndiye, Atate, tsanulirani Mzimu Woyera, wa Mafuta, pa iwo, kuti iwo akakhoze kuyikidwa mu utumiki wa Ambuye Mulungu, kuti iwo akakhoze kukhala ogwira ntchito mu tsiku lotsiriza ili, loyipa, pakuti ife tikuzindikira kuti ife tiri nayo chabe nthawi yayifupi. Ndipo Mpingo ukhoza kupita nthawi iliyonse.

³⁹² Mwanawankhosa akhoza, pa nthawi iliyonse, kuchoka pa malo opatulika mmwamba Kumeneko, kapena Mpandowachifumu wansembe, kutulukira kuchokera ku Mpandowachifumu wa Mulungu kumene nsembe ikugona, ndiyeno izo zatha; apo palibenso ziyembekezo kwa dziko; ilo

latsirizika. Ndiye ilo likulowa mu zokhumudwitsa, kusalama kwakukulu kwa zivomezi, ndi—ndi kugwedeza kwakukulu konga kunalipo pa chiwukitsiro. Ndipo—ndipo, a—a. . .

³⁹³ Pamene Khristu anawuka kuchokera ku manda, pamene oyera awuka, chinthu chomwe chidzachitika. Ambuye, iyo ikhoza kukhala miniti iliyonse. Ife tikuyembekezera tsiku lachisangalalolo kuti lifike.

³⁹⁴ Atengereni ana Anu pansu pa mkono Wanu, Atate, tsopano. Kokerani anaankhosa aang’ono Anu ku chifuwa Chanu. Perekani izi. Ndipo adyetseni iwo pa Mawu, mpaka iwo atakhala mu mphamvu ya utumiki. Ife tikuwapereka iwo kwa Inu tsopano, Ambuye. Yankhani pemphero ili.

³⁹⁵ Inu munati, Atate, uko mu Marko, mutu wa 11, “Pamene inu mupemphera, imani mukupemphera, khulupirani kuti inu mulandira zomwe inu mwapempha, ndipo inu mudzakhala nazo izo.”

³⁹⁶ Ndipo ndi mtima wanga wonse kwa Iye yemwe wakhala akuwulula zinthu izi konse kudutsa mu zaka, ndi Zisindikizo izi apa mu sabata yathayi; ine ndikukhulupirira Inu, Ambuye Mulungu, kuti liri ora, pafupi tsopano, pafupi kuposa momwe ife tikuganizira kwenikweni, za kuyandikira Kwanu.

³⁹⁷ Chonde lolani pemphero langa liyankhidwe. Ndipo atati mwana aliyense woyitanidwa wa Mulungu, yemwe ali mu kamtunda ka kumvera pano, kapena mwina tepi idzawakhudza, atati pa nthawi iyo. . . ine ndikuwatenga iwo kwa Ufumu wa Mulungu, pa chikhazikitso cha kudziwa kuti awa ali Mawu omwe akuwululidwa. Lolani Kuwala kwa madzulo kuwale, Atate. Ine ndikuwapereka iwo kwa Inu, mu Dzina la Yesu. Ameni.

³⁹⁸ Tsopano, onse, mkati kapena kunja, omwe akukhulupirira, ndipo simunapangepo anu—kuvomereza kwanu kwa pagulu, kuti inu mwathana nalo tchimo; ndipo inu—inukufuna zifundo za Mulungu, ndipo inu mwazilandira izo mu Yesu Khristu. Dziwe. . . Iwo akhala okonzeka kubatiza aliyense yemwe akufuna kubatizidwa, lero kapena mawa, pakali pano kapena lirilonse lingakhale.

³⁹⁹ Kodi inu mukusangalala nacho Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Inu mwawona pamene Icho chatsegulidwa tsopano? [“Ameni.”] Kodi inu mwakhulupirira Icho? [“Ameni.”]

⁴⁰⁰ Izo zinanenedwa, “Ndani wakhulupirira uthenga wathu? Ndipo nkwa ndani mkono wa Ambuye wawululidwira?” Mukuwona? Kukhulupirira uthenga, ndiye mkono wa Ambuye wawululidwa. Mkono, Mawu a Mulungu, awululidwa.

⁴⁰¹ Ambuye akalola tsopano, mawa mmawa, ine ndidzayesa mwakukhoza kwanga kuyankha mayankho amenewo. Ine

ndidzakhala mwinamwake usiku wonse, ndipo, kapena kwawukulu kwa iwo, mu pemphero, pa iwo. Ine ndikutenga pafupi ora limodzi kapena atatu usiku. Ine sindinapite kukagona usiku watha mpaka ikupita pa wani, ndipo pa firii koloko ine ndinali mu kuwenga. Mukuwona? Mukuwona?

⁴⁰² Ine ndiyenera kukayankhira izi. Uko nkulondola. Ife tiri pafupi zedi kwa chirichonse, kupusa kulikonse, kapena kulingalira kulikonse, kapena kukhulupirira kwa theka. Ine ndiyenera kuziwona izo, poyamba. Ndiyeno, pamene ine ndaziwona izo, izo ziyenera kukhala mu Mawu, nazonso. Ndipo mpakana apa, mwa chisomo cha Mulungu, izo ziri mwangwiro. Ine ndazitenga izo kuchokera njira yonse kupyola, inu mukudziwa izo, ndipo ziri—zalumikizana pamodzi kumene.

⁴⁰³ Ziyenera kukhala PAKUTI ATERO AMBUYE. Chifukwa, osati kokha pamene ndinena Izo kuchokera pakuzidziwa ine Izo, inemwini, koma Mawu a Ambuye ali PAKUTI ATERO AMBUYE. Ndipo apa pali Mawu, kutenga zomwe Iye wandipatsa kwa ine, ndi kuzilumikiza Izo pamodzi ndi kukusonyezani inu. Kotero inu mukudziwa, inueni, kuti ziri PAKUTI ATERO AMBUYE. Mwawona?

⁴⁰⁴ Apa pali Mawu, akunena choncho. Ndiyeno vumbulutso lomwe Iye akundipatsa ine, lomwe liri losiyana kwa zomwe aliyense wa ife ankaganiza konse; bwanji, losiyana kwa zomwe ine ndinkaganiza, chifukwa ine sindinalowe mwa Iwo monga choncho. Koma tsopano, ife tikupeza kuti, izo zikukomana pamodzi kumene. Ndipo Izo ziri chiyani? Izo ziri PAKUTI ATERO AMBUYE. Mukuwona? Ziri chimodzimodzi. Izo zakhala malo otsegulidwa, kugwirizira pamenepo, kwa ora lino, ndiyeno Ambuye nkubwera ndi kukankhiramo Iwo mkati momwe monga choncho. Kotero, inu mukuwona, apo Izo ziri. Izo, ziri—ziri Ambuye. O, ine ndikumkonda Iye! Ine ndikumkonda Iye ndi mtima wanga wonse.

⁴⁰⁵ Tsopano kumbukirani, inu . . . Ife sitikanakhoza kubwera ku guwa. Ambiri agwirizira manja awo mmwamba. Tsopano, onani, chiri chinthu cha aliyense payekha, ndi inu. Ndicho chirichonse chimene inu mukufuna kuchita. Mukuwona?

⁴⁰⁶ Ora layandikira pafupi zedi, inu muyenera kukanikiza molimba monga inu mungathere, osati kumachita kukokedwa. Mwawona, kumangokanikiza, kuyesera kulowa mkati, “Ambuye, musandisiye ine kunjja. Musandisiye ine kunjja, Ambuye. Zitseko zikutseka; Ngati ine nditangolowa mkati!” Mukuwona?

⁴⁰⁷ Mulungu adzatseka chitseko tsiku limodzi. Iye anachita mu tsiku la Nowa, ndipo iwo anamenya pa khomo. [M’bale Branham agogoda pa guwa kambiri—Mkonzi.] Nkulondola uko? [Osonkhana, “Ameni.”]

408 Tsopano kumbukirani, Baibulo linanena, kuti, “Mu ulonda wachisanu ndi chiwiri.” Nkulondola uko? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ena anagona mu ulonda woyamba, wachiwiri, wachitatu, wachinai, wachisanu, wachisanu ndi chimodzi, wachisanu ndi chiwiri. Koma, mu ulonda wachisanu ndi chiwiri, kunabwera kulengeza, kufuula, “Mkwati akubwera! Tulukani mukakumane naye Iye.”

409 Anamwali ogona anati, “Nnena, ine ndikufuna kukhala nawo ena a Mafuta awo tsopano.”

410 Mkwatibwi anati, “Ine ndangokhala nawo ondikwanira inendekha; ndangokhala nawo okwanira. Ngati inu mukuwafuna Iwo, inu mupite mukapempherere Iwo.”

411 Kodi inu simukuwawona anamwali ogona tsopano? Yang’anani pa a Episcopalia, a Presbateria, a Chilutera, ndi chirichonse, kuyesera kutero. Ndipo vuto lake liri, mmalo mopeza Mzimu Woyera, iwo akuyesera kulankhula mmalirime.

412 Ndipo ambiri a iwo amalankhula mmalirime, ndipo amachita manyazi kubwera ku mpingo uno kuti adzapemphereredwe; akufuna ine ndibwere ku nyumba yawo ndi kukawapempherera iwo. Inu mumawutcha uwo Mzimu Woyera? Uko ndi kulankhula mmalirime, koma osati Mzimu Woyera. Mukuwona?

413 Tsopano, ine ndikukhulupirira kuti Mzimu Woyera umalankhula mmalirime. Inu mukudziwa kuti ine ndimakhulupirira zimenezo, mwawona. Koma pali chokopera kwa Izo, nazonso. Inde, bwana. Z—zipatso za Mzimu, zomwe zimatsimikizira chomwe Iwo uli. Zipatso za mtengo zimatsimikizira mtundu wa mtengo umene iwo uli. Osati khungwa; chipatso!

414 Tsopano zindikirani, ndiye, pamene iye abwera, ilo—ora lotsiriza ilo. Ndipo apo, pamene iwo abwera mkati, ndiye iwo anapita ndi kunena, “Chabwino, ine ndikukhulupirira ine ndiri nawo Iwo tsopano. Ine ndikukhulupirira ine ndiri nawo Iwo. Eya, ife tikulandira Iwo.

415 Ine—ine—ine kuli bwino ndisanene izi, mwawona, chifukwa izo zikhoza kuyambitsa chisokonezo. Pamene ine ndinanena tsiku lina, Mkwatulo, momwe Iwo uti udzabwerere, ine—ine . . . Tsopano, ngati inu munena inu—inu mudzatenga izo, chabwino. [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Yang’anani. Yang’anani. Chabwino, ziri kwa inu.

416 Pamene namwali wogona, mwawona, yemwe ankaganiza kuti iye anali atapemphera mokwana, kuti abwerere, Mkwatibwi anali atapita kale. Iwo unapita, ndipo iye sanadziwe izo; monga wakuba mu usiku. Ndiye iwo anayamba kugogoda pa zitseko. Ndipo chinachitika nchiyani? Nchiyani chomwe chinachitika? Iwo anaponyedwa mu nthawi ya Chisawutso. Baibulo linati,

“Uko kudzakhala kulira, ndi kuisima, ndi kukukuta kwa mano.” Nkulondola uko?

417 Pamene izo ziti zidzakhale, m’bale, mlongo, ine sindikudziwa. Koma, ine—ine, ine, zikukhoza kungokhala ine pano, tsopano, mwawona. Izi, izi ziri zomwe. . . Ili liri ganizo langa. Mukuwona? Ine—ine—ine ndikukhulupirira ziri pafupi zedi, ine—ine ndiri. . . Tsiku lililonse ine—ine ndikufuna. . . Ine ndikungoyesa kuyenda mofewa monga ine ndingathere. Mukuwona? Ndipo tsopano pamene, inu mukudziwa, pamene a. . .

418 Chinachake chinachitika lero, ndipo ine ndinawona chinachake chikubwera. Ine—ine basi. . . Ine sindinakhoze kupuma mopitiriza nkomwe, mwawona. Apo Iye anali, kuyima pamene, Kuwala kwakung’ono uko kutayima pomwe apo. Ndipo apa Iko kunali. Ine ndikudziwa ndicho Chowonadi.

419 Ine ndinaganiza, “O Mulungu, ine sindingakhoze kunena izo. Ine—ine sindingakhoze kunena izo. Ine sindingakhoze.” Ine ndinangotuluka mchchipindamo, kupita panja, ndinakayendayenda. M’bale, ine ndinaganiza, “Mai! Ndingachite chiyani ine? O!” Mukuwona? Ndipo ine—ine ndiyenera kupita kukawedza, kapena chinachake, kapena ine. . . Mnyamata, iwe ukanati. . . iwe. . . ine sindingakhoze kukuwuzani inu. Mukuwona?

420 Koteru, ife tiri nayo nthawi yabwino. Sichoncho ife? Ambuye alemkezeke! Ameni! Mukuwona? Ife tiri mu—ife tiri mu nthawi yopambana, mwawona, pakuti mtima wanga wasefukira nacho chisangalalo ndi chimwemwe.

421 Koma pamene ine ndiganiza za dziko lino ndi zikwi za omwe ine ndikuwadziwa amene atayika, mthunzi-wakuda, utawaphimba, ndiye mtima wako umangowukha. “Iwe ungachite chiyani? Iwe ungachite chiyani?” Iwe umangomverera Mzimu Woyera ukulira, mu mtima wako. Monga zikanayenera kukhalira mwa Ambuye wathu, pamene Iye anayang’ana pa Yerusalemu, anthu Ake Omwe, mwawona, anati, “Yerusalemu, Yerusalemu, Ine ndikufungatira kochuluka bwanji iwe, monga nsoti ukanachitira anapiye ake, koma iwe sukufuna ayi.” Iwe ukungomverera Mzimu Woyera ukuti, “Ine ndikusonkhanitsa iwe kowirikiza chotani, mwawona, koma iwe sukufuna.” Mukuwona?

422 Ife tiri, ife tiri pomwe apa pa chinachake, amzanga. Chirichonse chomwe icho chiri, Mulungu akudziwa. Palibe aliyense, palibe aliyense akudziwa pamene izo ziti zidzachitike. Ndicho chinsinsi. Palibe aliyense akudziwa pamene izo ziti zidzachitike.

423 Koma Yesu anatiwuza ife, “Pamene inu muwona zinthu izi, zinthu zonse izi.” Monga ngati zomwe ine ndinapita, kufanizitsa ndi Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi, kwa

zomwe Iye ananena mu Mateyu 24. Tsopano kumbukirani zomwe Iye ananena, “Pamene inu muwona zinthu izi zikubwera, zikayamba kubwera pokwaniritsika, ndiye nthawi ili pa khomo.” Yang’anani ndime yotsatira yomwe, ndime 30—30 ndi ya 31 monga tinapitira mpaka mmusi, ndime za 32, 33.

⁴²⁴ Iye anati, “Ndipo Iye adzatumiza angelo Ake ku ngodya zinai za mmiyamba, ku mphepo zinai, kukasonkhanitsa Osankhidwa Ake.” Nkulondola uko?”

Anati, “Tsopano phunzirani . . .”

⁴²⁵ Tsopano kumbukirani, Iye anayimira pomwe apo. Iye sanapitirire, chitachitika Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi icho. Iye sanene konse kalikonse za Chachisanu ndi chiwiri. Iye ananena Choyamba, Chachiwiri, Chachitatu, Chachinai, Chachisanu, ndi Chachisanu ndi chimodzi. Koma Iye anayimira pomwepo, sanatchule konse chirichonse za Icho.

⁴²⁶ Yang’anani chinthu chotsatira Iye ananena, “Tsopano phunzirani fanizo.” Mukuwona? Ndiye Iye akuyamba pa fanizo. Iye anati, “Zinthu izi zidzakhala.”

⁴²⁷ Iye akuyankha mafunso atatu awo. “Chidzakhala chiyani . . . zizindikiro izi? Ndipo chidzakhala chiyani chizindikiro cha Kudza Kwanu? Chidzakhala chiyani chizindikiro cha mapeto a dziko?”

⁴²⁸ Ndipo Icho Chachisanu ndi chimodzi, apo, chinali mapeto a dziko. Ndipo kuwomba kwa mngelo wachisanu ndi chiwiri . . . “Anakweza mmwamba manja, ndipo analumbira pa Iye yemwe akhala moyo kwa nthawi za nthawi, kuti sipadzakhalanso nthawi.” Dziko lapansi likupereka kubala kwa lina latsopano. Izo zatha.

⁴²⁹ Ndipo apa ife tiri, pomwe apa pa khomo. O, ine ndikunjenjera. “Ndipo ine ndiyenera kuchita chiyani, Ambuye? Chiyani—nchiyani chinanso ine ndingakhoze kuchita?” Mukuwona? Ndipo, ndiye, ingoganiza za kuwawona malo amenewo ndi anthu ofunika awo! Ine ndinayima pamenepo, ndikuziyang’ana pa inendekha. Ndipo ine ndinaganiza, “O Mulungu, bwanji, iwo—iwo sangakhoze kuphonya ichi. Ine—ine—ine ndiyenera kuwakankha iwo. Ine ndiyenera kukangofika mu chigulu ndi kuwatenga iwo, ndi kuwakankha.” Iwe sungakhoze kuchita izo. Iwe . . .

⁴³⁰ “Ndipo palibe munthu angakhoze kubwera pokha Atate Anga atamukoka iye.” Koma apa pali chithoncho chimodzi chomwe ife tiri nacho, “Onse omwe Atate andipatsa Ine adzabwera.”

⁴³¹ Koma ena onsewo, ndi mabungwe awa, kudalira pa iwo monga choncho, mwawona. “Ndipo iye ananyenga onse omwe akukhala pa, akukhala pa dziko lapansi, amene maina awo sanalembedwe mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa ilo,

wophedwa kuchokera ku maziko a dziko.” O, mai! Kotero, inu mukuwona, chiri chinthu chachisoni.

432 Chinthu chokhacho inu mungakhoze kuchita chiri chabe—chabe—chabe—kungokhala chabe nawo Mawu. Yang’anani chabe chirichonse chomwe Iye anena kuti muchite, ndiyeno muchite chimenecho. Mukuwona? Chirichonse chimene Iye anena chitani; chitani chimenecho.

433 Ndipo inu muziyang’ana kunjira uko, ndi kunena, “O, mai! Iwo amachita *izi*, ndiye . . . O!” chiri chabe . . .

434 Inu simumazindikira kufinya kwake! Tsopano ine ndikufuna kunena *izi*. Ine ndikuganiza matepi azimitsidwa. Anthu ambiri amanena, “M’bale Branham, ali ndi utumiki wa mtundu uwo . . .” (Ine ndimayenera kuyang’ana, chifukwa anthu amangotenga matepi awo ndi kungoyesera kuwatenga iwo ku zidutswa, inu mukudziwa.) Kotero pamene iwo anena, “M’bale Branham, tikukhumba ife tikanakhala nawo utumiki,” inu simukudziwa chomwe inu mukunena. Inu, mowona mtima, inu simukudziwa chomwe chimapita nawo iwo, m’bale, mlongo. O, mai! Ndi udindo, pamene uli nawo anthu amene amazendewera kwa zomwe iwe umanena! Kumbukirani, ngati iwe uwawuza iwo cholakwika, Mulungu adzafuna magazi awo pa manja ako. Ndiye, iwe ukaganiza za icho. Icho ndi chinthu chowopsya.

435 Kotero, khalani okonda. Mukondeni Yesu ndi mtima wanu wonse. Ingotsa- . . . Khalani wophweka. Musati nkomwe kuyesera—kuyesera kulingalira chirichonse. Ingokhali ophweka, pamaso pa Mulungu. Chifukwa, mukachulukitsa inu kuyesera kulingalira, inu mupita kutali ndi Iye. Mukuwona? Ingomukhulupirani mophweka Iye.

Nenani, “Tsopano, chabwino, Iye adzabwera liti?”

436 Ngati Iye abwera lero, chabwino. Ngati Iye abwera zaka makumi awiri kuchokera tsopano, ziri bwino. Ine ndipitirira basi momwe ine ndikupitira tsopano, kumutsatira Iye. “Ambuye, ngati Inu mungandigwiritse ine ntchito paliponse, ine ndiri pano, Ambuye.” Ngati ziri zaka zana kuchokera lero, ngati zazikulu—zazikulu—zazikulu—zazikulu—zidzukululu zikhale moyo kukaliwona ilo likubwera, lolani . . . “Ambuye, ine sindikudziwa pamene izo zidzakhale, koma mungondilola ine kuyenda molondola lero, chabe nanu Inu.” Mukuwona? Ine—ine ndikufuna . . . Chifukwa, ine—ine ndidzawuka pa tsiku lotsiriza ilo, basi mofanana ngati ine ndinagona pang’ono kwinkakwaka.

437 Ndikubwera mmusi kumeneko, nyumba yachimfumu yaulemerero iyo kutsidya, Ufumu wa Mulungu uwo kumeneko, kumene onse okalamba adzakhala aang’ono, kumene miinjira yoyera yakonzeka! Amuna ndi akazi asintha, mu kukongola, luso lomwe la—la m—mwamuna wokongola ndi m—mkazi wokondeka! Atayima pamenepo mu kukongola konse ndi

thunthu la mkazi wamng'ono ndi mwamuna wamng'ono, atayima pamenepo! Ndipo sangakhoze kukalambanso, sangakhale wochimwa nkomwe, sikungakhale chirichonse cha nsanje, kapena udani, kapena chirichonse! O, mai!

⁴³⁸ Ine ndikuganiza matepi azimitsidwa tsopano. Ndipo ine—ine ndiri nawo chabe pafupi maminiti atatu kapena anai. Ine ndikufuna kulankhula kwa inu. Ziri bwino kutero? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Tsopano, ichi chiri chabe cha kwa munthu payekha, mwawona. Chifukwa, mawa, ine—ine. . . Lidzakhala lopambana kwambiri! Ine ndikuganiza ine kulibwino ine ndingonena izo tsopano, mwawona, zomwe ine nditi ndinene. Ine. . . Izi ziri chabe kwa ife tsopano. Ine ndinali chabe. . .

⁴³⁹ Inu mukudziwa, ine—ine ndiri naye mkazi yemwe ine ndimamukonda, ndipo ameneyo ndi Meda. Ndipo ine—ine sindikanati ngakhale ndimukwatira iye, chifukwa cha chikondi changa kwa mkazi wanga woyamba. Ndipo komabe, monga mochulukwa ine ndinkasamala za iye, ine—ine sindikanamukwatira iye ngati zikanakhala kuti sanali Mulungu yemwe anandiwuza ine kuti ndichite izo. Ndipo inu mukudziwa nkhani ya izo; momwe iye anapitira kukapemphera, ndi momwe ine ndinachitira. Ndiyeno Iye anandiwuza ine chimodzimidzi choti ndichite, ndi, “Ndikupita, kukamukwatira iye,” ndi nthawi yeniyeni yokachitira izo. Iye ali mkazi wokondeka. Ndipo iye akundipempherera ine usiku uno. Ndipo kotero tsopano ili eyiti koloko, kwathu, iye mwina ali kupemphera tsopano.

⁴⁴⁰ Tsopano zindikirani. Tsiku lina iye ananena kwa ine, iye anati, “Bill,” iye anati, “Ine ndikungofuna kukufunsa iwe funso za Kumwamba.”

Ine ndinati, “Chabwino, Meda, ndi chiyani ilo?”

Iye anati, “Iwe ukudziwa ine ndimakukonda iwe.”

⁴⁴¹ Ndipo ine ndinati, “Eya.” Zinali izi zitachitika kumene kuno.

Iye anati, “Iwe ukudziwa kuti Hope anakukonda iwe, nayenso.”

Ine ndinati, “Eya.”

⁴⁴² Ndipo iye anati, “Tsopano,” iye anati, “Ine sindikuganiza ine ndikanakhala wansanje,” iye anati, “koma Hope anali.” Ndipo iye anati, “Tsopano, pamene ife tikafike Kumwamba. . . Ndipo iwe unati iwe unamuwona iye kumeneko.”

⁴⁴³ Ine ndinati, “Iye anali kumeneko. Ine ndinamuwona iye. Ine ndinamuwona iye kawiri, kumeneko.” Iye ali kumeneko. Iye akuyembekezera kuti ine ndibwere. Chotero ali. . . Chotero ali Sharon. Ine ndinamuwona iye, mofanana basi monga ine ndikupenyera pa iwe. Ine ndinamuwona iye kumeneko. Ndipo ine ndinati. . .

444 Iye anati, “Chabwino, tsopano, pamene ife tikafike kumeneko,” anati, “ndi uti ati akakhale mkazi wako?”

445 Ine ndinati, “Onse a inu. Uko sikukakhala aliyense, waona, komabe onse a inu mukakhala.”

Iye anati, “Ine sindingakhoze kumvetsa izo.”

446 Ine ndinati, “Tsopano, wokonededwa, khala pansu, undirole ine ndifotokoze chinachake kwa iwe.” Ine ndinati, “Tsopano, ine ndikudziwa iwe umandikonda ine, ndipo iwe ukudziwa momwe ine ndimakukondera iwe, ndi malemekezo ndi ulemu. Tsopano, mwachitsanzo, bwanji ine nditavala, nkupita kumusi kwa mzinda; ndipo hule lina laling’ono, lokongola kwenikweni, ndi kubwera ndi kuponya mikono yake mondikumbatira ine, ndi kunena, ‘O, M’bale Branham, ine ndikutsimikiza ndimakukonda iwe,’ nkuyima kuyika mikono yake mondigwira ine ndi kundikumbatira ine. Iwe ungaganize chiyani?”

Iye anati, “Ine sindikuganiza ine ndingakonde izo mwabwino kwambiri.”

447 Ndipo ine ndinati, “Ine ndikufuna ndikufunse iwe chinachake. Kodi iwe . . . Kodi iwe umamkonda kwambiri ndani, ngati patati pakhale chiwonetsero, ine kapena Ambuye Yesu?” Tsopano, ilo ndi banja chabe, kulankhulana.

448 Ndipo iye anati, “Ambuye Yesu.” Anati, “Inde, Bill, mochuluka momwe ine ndimakukondera iwe, koma, ndisanati ndimusiye Iye, ine ndikanakusiya kaye iwe.”

449 Ine ndinati, “Zikomo iwe, wokonededwa. Ine ndiri wokondwa kukumva iwe ukunena icho tsopano.” Ine ndinati, “Tsopano, bwanji ngati mkazi wamng’ono yemweyo akanabwera kwa Yesu ndi kuponyera mikono yake pozungulira Iye, nanena, ‘Yesu, ine ndimakukondani Inu,’ iwe ukanaganiza chiyani za izo?”

Iye anati, “Ine ndikanasangalala nazo izo.”

450 Mwawona, izo zimasintha kuchokera ku filiyo kupita ku agapao. Mwawona, ndi Chikondi chapamwamba. Mukuwona? Ndipo uko kulibe chinthu chonga mwamuna ndi mkazi wake, monga . . . ndi kulera ana. Izo zonse zatha, m—ziwalo za mkazi ndi mwamuna. Zofunitsana zonse ziri . . . Iwo onse ali ofanana, kumeneko. Mukuwona? Uko kulibe chirichonse cha izo, nkomwe. Mwawona, uko kulibe zofunitsa kugonana konse, ayi nkomwe. Mukuwona? Inu muli chabe . . . Ine, bwana. Tangoganizani za inu eni wopanda zofunitsa kugonana. Chifukwa chomwe izo zinayikidwa mwa ife ndi chakuti tichulukane mu dziko lapansi, inu mwawona. Koma, Uko, uko sikukakhala chirichonse kumeneko. Uko sikukakhala ngakhale chofunitsa champhongo kapena chachikazi. Ayi.

451 Koma thunthu la luso la Mulungu lidzakhala liripo. Ndicho cholondola chimodzimidzi. Koma ife mowona tidzakhala enieni. Ayi—wopanda filiyo, nkomwe; chonse agapao. Mukuwona?

Chotero, mkazi akanakhala wosaposa chabe winawake wokonedwa yemwe ali—ali wako, ndipo iye... Inu muli a wina ndi mzake. Uko kulibe chinthu chonga... Ayi, ayi, uko kulibe ngakhale... Mwawona, gawo la filiyoyi siliri ngakhale uko nkomwe. Mwawona, uko sikungakhale chirichonse chonga nsanje; palibe kanthu koti uchitire nsanje. Kulibe kanthu koteroko uko. Iwe suwungadziwe nkomwe chinthu chotero chonga icho. Mukuwona? Ndi basi mwamuna wamng'ono wokonedwa ndi mkazi wamng'ono, kukhala moyo.

Ndiyeno, zitatha, iye anati, “Ine ndachiwona icho tsopano, Bill.”

Ine ndinati, “Eya.”

⁴⁵² Ine ndikufuna ndikuwuzeni inu kanthu kakang'ono kanachitika. Ili linali loto. Ine ndinali kugona. Ndipo ine sindinanenepo ili pagulu kale. Ine ndinanena ilo kwa anthu angapo, koma osati kwa gulu nkale, monga ine ndikudziwira.

⁴⁵³ Ine—ine ndinalota, pafupi mwezi zitachitika zija, kuti ine ndinali kuyima tsiku lina, ndipo ine ndinali kuyang'ana nthawi yayikulu yomwe... Osati chiweruzo, tsopano. Ine sindikukhulupirira Mpingo ukafika konse ku, (ine ndikutanthawuza, Mkwatibwi), kupita ku chiweruzo. Koma, ine ndinali kumeneko pamene akorona anali kuperekedwa, mwawona. Ndipo waukulu—Mpandowachifumu waukulu utayikidwa pamwamba *apa*. Ndipo Yesu ndi Mngelo wolemba, ndi onse, anali atayima pamenepo. Ndipo kunali masitepe opita mmwamba, monga, kubwera pansu njira *iyi*, a minyanga yoyera; kupita mmusi, kuzungulira, anapanga chopitirira monga *chonchi*, ndipo anapita kunja, koteroko kuti khamu lalikulu lonse ili litayima pamenepo likanakhoza kuwona chimene chinali kuchitika.

⁴⁵⁴ Ndipo ine ndimayimirira cha kumbuyo, kumbuyo kutali ku mbali imodzi. Ndipo ine ndinali chabe kuyimirira pamenepo, wopanda lingaliro momwe ine ndimayenera kuyenda masitepe amenewo. Ine ndinali kuyima pamenepo. Ine ndimakhoza kuwona...

⁴⁵⁵ Mngelo wolemba amakhoza kuyitana dzina lina; ndipo ine ndimakhoza kulidziwa, kulizindikira dzina limenelo. Ine ndinayang'ana, ndipo kumbuyo kutali cha uko, apa pakubwera m'bale, akuyenda ndi mlongo, ankayenda mpaka kwa iwe, monga choncho. Mngelo wolemba atayima pamenepo pa mbali ya Khristu, (loto chabe tsopano), ndipo anali kuyang'ana. Ndipo dzina lawo linali pamenepo, ilo linapezeka mu Bukhu la Moyo; Iwo amakhoza kuyang'ana pa iwo, ndi kunena, “Unali—unachita bwino, wantchito Wanga wabwino ndi wokhulupirika. Tsopano lowa mkati.”

⁴⁵⁶ Ine ndinayang'ana kumbuyo, kumene iwo anali kupita. Uko kunali dziko latsopano, ndi zimwemwe. Ndipo anati, “Lowani

mu zimwemwe za Ambuye, zomwe zakhala—zomwe zakhala ziri zanu chikhazikitsireni maziko a dziko.” Mukuwona? Ndipo, o, ine ndinagaiza. . . Iwo adutsa kupyola pamenepo, ndi kukumana wina ndi mzake, ndipo akungosangalala, ndipo akupita kudutsa mapiri ndi malo akulu opambana.

⁴⁵⁷ Koma ine ndinaganiza, “O, kodi siziri zodabwitsa izo! Ulemerero! Aleluya!” Kumangolumpha mmwamba ndi pansi!

⁴⁵⁸ Ndiye ine ndimakhoza kumva dzina lina likuyitanidwa. Ine ndikuganiza, “O, ine ndikumudziwa iye. Ine ndikumudziwa iye. Ine. . . Uko, uko iye akupita, kumeneko.” Ndikumuyang’ana iye monga choncho.

“Lowani muzimwemwe za Ambuye, wabwino Wanga ndi. . .”

“O,” ine nkumati, “Mulungu alemekezeke! Mulungu alemekezeke!”

Kungonena, mwachitsanzo, monga iwo akuti, “Orman Neville,” mwawona.

⁴⁵⁹ Ndiyeno ine nkuti, “Ameneyo ndi M’bale Orman Neville uja. Apo iye ali.” Mukuwona? Ndipo apa iye akubwera, kuchokera mu unyinjini, akupita mmwamba.

⁴⁶⁰ Tsopano Iye nkuti, “Lowani mu zimwemwe za Ambuye, zomwe zakonzedwera inu chikhazikitsireni maziko a dziko. Lowani mkati.” Ndipo M’bale Neville uja nkungosintha, ndipo nkungoyambiranso kubwerera mmenemo, akungofuwula ndi kukuwa.

⁴⁶¹ Mnyamata, ine ndimangofuwula ndi kunena, “Ulemerero kwa Mulungu!” Nditayima cha apa mwa ndekha, ndikukhala nayo nthawi yodabwitsa, ndikuyang’ana abale anga akulowa mkati.

⁴⁶² Ndipo Mngelo wolemba anayima pamenepo, ndipo anati, “William Branham.”

⁴⁶³ Ine sindinaganize nkomwe kuti ndimayenera kuyenda mmemo. Kotero ndiye ine ndinawopsyedwa. Ine ndinaganiza, “O, mai! Kodi ine ndisowa kuchita izo?” Kotero ine ndinapita ndikuyenda kumusi uko. Ndipo basi aliyense akundisisita ine pa—pa. . . [M’bale Branham akuwonetsera mwa kudzisisita yekha kambiri—Mkonzi.] “Moni, M’bale Branham! Mulungu akudalitseni inu, M’bale Branham!” Akundisisita pamene ine ndikupita motsatira, kupyola unyinjini wawukulu wopambana wa anthu. Ndipo onse a iwo akufikira ndi kumandisisita ine monga chonchi. [M’bale Branham akuwonetsera pa kudzisisita yekha kambiri.] “Mulungu akudalitseni inu, m’bale! Mulungu akudalitseni inu, m’bale!”

⁴⁶⁴ Ine ndinali kupita. Ine ndinkati, “Zikomo inu. Zikomo inu. Zikomo inu.” Monga kutuluka kuchokera mu msonkhano, kapena chinachake, inu mukudziwa.

465 Ndipo ine ndinali kupita kukayenda masitepi a minyanga akulu opambana. Ine ndinayamba kuyenda mmwamba kupyola pamenepo. Ndipo ine nditangopanga sitepe yoyamba, ine ndinayima. Ndipo ine ndinaganiza...ine ndinayang'ana pa nkhope Yake. Ine ndinaganiza, "Ine ndikufuna kutenga kuyang'ana kwabwino pa Iye mbali iyi." Ndipo ine ndinayima.

466 Ine ndinali nditakweza manja anga monga *chonchi*. Ine ndinamverera chinachake chikugwera mu mkono mwanga *apa*. Icho chinali mkono wa winawake. Ine ndinapenya pozungulira, ndipo apo panayima Hope; maso akulu akuda awo, ndi tsitsi lakuda ilo likugwera pansu kumbuyo kwake, atavala mwinjiro woyera; akuyang'ana mmwamba pa ine monga choncho. Ine ndinati, "Hope!"

467 Ine ndinamverera chinachake chitagunda mkono *uwu*. Ndinayang'ana pozungulira, ndipo apo panali Meda; maso akuda awo akuyang'ana mmwamba, ndipo tsitsi lakuda ilo likugwera mmusi, atavala mwinjiro woyera. Ndipo ine ndinati, "Meda!"

468 Ndipo iwo anayang'anana, inu mukudziwa, monga choncho. Iwo anali...ine ndinawagwira iwo mu mikono yanga, ndipo apa ife tinapita, tikumka Kwathu.

469 Ine ndinawuka. O, ine ndinawuka. Ndipo ine—ine ndinadzuka ndi kukhala pansu mu mpando, ndipo ndinalira, inu mukudziwa. Ine ndinaganiza, "O Mulungu, ine ndikuyembekeza izo zikubwera monga choncho." Onsewo anathandizana nane mu moyo, ndi kubala ana, ndi zinthu monga choncho; ndipo apa ife tiri, tikuyenda kulowa mu dziko latsopano, o, mai, kumene ungwiro ndi chirichonse. Ayi, palibe kanthu... .

470 O, icho chikakhala chinthu chodabwitsa! Musati muphonye izo. Musati muphonye izo. Mwa chisomo cha Mulungu, chitani chonse inu mungathe kuchita, ndipo izo zikakhala kwa Mulungu kukasamalira zina zonsezo ndiye.

Ndimkonda Iye, ndimkonda Iye
Poti Iye anayamba kundikonda
Nagula chipulumutso changa
Pa wa Kalvare... .

471 Tiyeni tiyimbe iyo kachiwiri, ndi mtima wathu wonse. Tsopano kwezani maso anu kwa Mulungu.

Ndimkonda Iye

472 [M'bale Branham achoka pa guwa ndi kumupempherera mkazi, pamene osonkhana akuyimba *Ndimkonda Iye kamodzinsu—Mkonzi.*]

...mkonda Iye
Poti Iye anayamba kundikonda
Nagula chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

473 Chabwino, tsopano. Iye samayembekeza kuti akhala moyo mu msonkhano wonse. Uko nkulondola. Apo iye ali, manja onse ali mmwamba, akulemekeza Mulungu. Ndicho chifukwa chake ine ndimachedwa pano nthawi yayitali; osakuwuzani inu zomwe ine ndimachita. Ine ndinali kulankhula za Meda ndi iwo. Ndipo kuti ine ndinali kuyang'ana, kuti ndiwone chimene . . . ine ndimapitirira kuzindikira mkombero wa Kuwala uwo ukuzungulira mmbuyo ndi patsogolo, ndipo unapita ndi kukapachikika pa iye. Ine ndinaganiza, “Ndicho icho.” O, kodi sizodabwitsa? [Osonkhana akusangalala—Mkonzi.]

Ndimkonda Iye, ndimkonda Iye
Poti Iye anayamba kundikonda
Nagula chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

474 Tsopano, ndi mitima yathu, [M'bale Branham akuyamba kung'ung'uza *Ndimkonda Iye*—Mkonzi.] Tangoganizani za ubwino Wake ndi chifundo.

. . . Ndimkonda Iye (Ameni!)
. . . Iye anayamba kundikonda . . .

475 Tsopano mwawona momwe ubwino wake uliri? Ameni!. Ndi zimenezo. Tsopano . . . ? . . . Pitani ndipo mukakhala bwino. Ameni! Chisomo cha Mulungu chawonekera kwa inu, kukakupangani inu abwino. Ameni.

. . . pa mtengo wa Kalvare.
O, ulemerero kwa Mulungu!
Ndimkonda Iye, . . .
Chabwino, m'busa wanu.
Ndi . . .

476 [Winawake ati, “M'bale Branham, mawa tiyamba hafu pasiti naini?”—Mkonzi.] Naini mpaka hafu pasiti naini. Naini koloko, penapake mmenemo. [“Chitatha chakudya cha mmawa? Naini koloko?”] Inu mukayamba pa naini. Ine ndidzayamba pa hafupi pasiti naini.



CHIVUMBULUTSO CHA ZISINDIKIZO ZISANU NDI ZIWIRI
(The Revelation Of The Seven Seals)

Mauthenga khumi awa analalikidwa ndi M'bale William Marrion Branham pa Marichi 17 mpaka pa Marichi 24, 1963, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., ndipo *Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri* chinapitirira pa Marichi 25 ku Sherwood Motelo. Titapeza matepi apachiyambi omveka ndi otsirizika kwathunthu, Mauthenga awa abwerezedwanso molingana ndi dongosolo latsopano. Kuyesesa konse kwapangidwa pochotsa molondola Uthenga wolankhulidwa pa matepi a maginito kupita ku tsamba losindikizidwa, ndipo atsindikizidwa mkatimu mosachotsera mawu ena.

Maufulu onse mu bukhu ili ndi osungidwa. Bukhu ili silingagulitsidwe, kapena kusindikizidwanso, kumasuliridwa mu zilankhulo zina, kapena kugwiritsidwa ntchito popezera ndalama wopanda kufotokoza kwa chilolezo cholembedwa cha William Branham Evangelistic Association. Kunasindikizidwa kachiwiri mu 2005.

CHICHEWA

©1994 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org